Mafunso ndi Mayankho

. . . apa, ine ndingolipinda ilo. Ilo likuti:

24b. Kodi inu mumakhala ndi tsiku kumaganizira zinthu zimene muti mudzayankhule usiku?

Izo ndithudi zingatenge tsiku, sichoncho izo?

Ayi, Mkhristu, m'bale wanga, ine sindikhala konse ndi lingaliro limodzi la zimene ine nditi ndidzayankhule pa guwa. Ine ndimawerenga Lemba penapake. Ndipo ine—ine ndalengezapo nthawi zambiri kuti ndikupita ku guwa, ine ndikalalikira phunziro linalake, kukafika pamenepo, Mzimu Woyera nkunditembenuza ine kubwerera mozungulira, kundipangitsa ine kuchita chinachakenso.

Ine ndayeserapo izo kawiri kapena katatu kulemba zolemba ndi kulalikira pa zolemba. Mochuluka pamene ine ndikuyang'ana pa zolemba zimenezo, ine ndimachotsa malingaliro anga pa Mulungu. Kotero ine ndimangopitirira ndi kuzipinda izo ndi kuziponyera izo pansi ndipo basi chirichonse chimene Iye anena. Nthawizina ine ndimayambira mu Genesis ndi kudzathera mu Chivumbulutso, ine . . . Kotero ine sindiri mochuluka kwambiri—mtumiki basi woti—ku . . . Ine ndimayenera kutenga mauthenga anga kuchokera Kumwamba.

Ndipo ine—ine ndimawerenga Lemba, monga ine ndinanena, pa chilemba cha chirombo. Ine . . . Mkazi wanga, amayi anga, ndi iwo amene amadziwa, apongozi anga aakazi akhala apawa, amene ali kwathu pa kanthawiyi, ine basi, pafupifupi firii koloko masana, ine ndimayamba kupemphera. Ine ndimakalowa mkati, ndimakayamba kupemphera. Ndiye ine ndimangopita pansi, ine ndimaganiza, "Chabwino, ine ndinati ndiyankhula usikuuno pa *Chilemba Cha Chirombo*." Ine ndimadutsamonso. Ndipo ndabweretsa, usikuuno, kwa yankho ko—konkodansi ya Cruden. Ndipo kuti ndipezemo mayankho, kapena, osati—osati mayankho, koma inu mukudziwa chimene konkodansi ili: iyo ndi mawu onse amu Baibulo atalembedwa. Kotero, ine ndimangosaka konkodansi kuti ndipezemo, nthawizina, pamene funso la munthuyo liri.

Koma pokhala nthawi zambiri, pamene ine ndikuwona mmodzi wa amzanga pano amene ndinakumana naye mu sitolo, kapena pafupi ndi sitolo masana uno, iye . . . ife timayankhula za mafunso awa, ndi zina zotero, monga choncho.

Tsopano, moyo wanga onse umene ine ndakhala nawo, chikhalireni mtumiki, ine ndimachita kumenyera pafupifupi ndi chirichonse. Ine sindinapite ku sukulu ya seminare iliyonse. Ndipo chinthu chokhacho chimene ine ndaphunzira chakhala

chimene Iye amandiuza ine. Ndiyeno ine ndimangokhala pa icho ndi—ndi kukhulupirira icho. Ndipo ndimayenera kumenyera pafupifupi chirichonse chimene ine—ine ndimakhulupirira, kuzungulira dziko. Ine . . . Iwo . . . Uko ku Afrika, mmalo osiyanasiyana ndi malo akutali, iwe umakapezako timalingaliro timene America sanaganizirepo. Ndipo zimenezo zaponyedwera pa iwe. Koma chinthu chenicheni ndichakuti ine nthawizonse ndayesera kuima basi pa Mawu awa, pomwe apa; mwaona, osati basi pa Lemba limodzi, izo ziyenera kubwera njira yonse kudutsa mu Baibulo.

Tsopano, iwe ukhoza kutenga Lemba limodzi ndi kulipanga ilo kunena chirichonse. Kodi inu mukudziwa kuti achikunja amagwiritsa ntchito Baibulo ili ngati bukhu lawo la zotsutsana? Zedidi. Koma izo ziyenera kukhala zofanana njira yonse. Tsopano, ngati inu mungakhululuke kufotokozako (ine ndingati, basi, kotero, mwanjira ya maphunziro kwa ife), Baibulo liri ngati mkuluwiko wopiringizika umene wadulidwa. Ndendende. Ndipo iwe uyenera kuyang'ana kwa Khristu Yesu, Ndondomekoyo, kuti udziwe mmene ungaziikire izo pamodzi. Ngati iwe sutero, iwe umatenga lingaliro lako lako, iwe umakhala nazo mwakuwona kwako kwako, ng'ombe ikudya udzu pamwamba pa mtengo, chinthu choyamba iwe ukudziwa. Izo sizigwira ntchito molondola. Koma ngati iwe utangolola Mzimu Woyera; basi osagwiritsa ntchito malingaliro ako pamene iwe ukuwerenga Baibulo. Ngati iwe uyesera kugwiritsa ntchito nzeru zako kapena malingaliro ako, iwe ndithudi udzatembenuzidwa mozungulira nthawi iliyonse. Mukuona?

Pakuti monga Khristu anati, "Ine ndazibisa izo kwa maso a seminare, anzeru ndi aluntha, ndipo ndidzaziulula izo kwa makanda otere amene angaphunzire." Mwaona. "Ine ndazibisa izo." Kotero kulibeko masukulu, ndi magulu, ndi—ndi magulu a mpingo, ophunzitsa Lemba mmene ilo liyenera kukhalira. Tsopano, ndicho chinthu chopambana kuti tichinene. Iwo akhoza kukhala ndi choonadi chochuluka, koma Mzimu Woyera umaulula izo kwa anthu pawokha pawokha. Chotero, Mzimu Woyera ndi wa aliyense payekha payekha. Ndicho chifukwa chake bungwe limawachotsa anthu pa mzere wa Mulungu nthawi zonse. Chifukwa Mulungu amapereka chinachake chatsopano nthawizonse, Iye akuyendabe monga choncho. Ndipo, koma awa nthawizonse ndi maziko. Penyani ndipo muwone izo pamene zikukungunuka mu Baibulo, muyang'ane pa izo mmene zikukungunukira mu nthawi. Ndiye inu mukhoza kuwona komwe inu mukupita.

Tsopano, mu mayankho awa, monga ine ndanenera, ndine mphunzitsi wosatha. Koma ine ndikufuna kunena izo zimene ine ndikudziwa za izo, ine ndikufuna kuti—kuti ndifotokoze izo kwa ena. Ndipo ngati inu mutsutsa ndi kuti, "Chabwino, M'bale Branham, ine basi sindikuzikhulupirira izo mwanjira

imeneyo," izo nzabwino, izo sizimatilekanitsa ife kukhala abale nkomwe, mwaona. Ndife abale basi. Ine . . . Ngati inu mukufuna kuti mukhale a—a—a . . . kukhala wa mu kachisi wopitirira, inu mukudziwa, zimenezo nzabwino ndi ine. Mwaona. Ndipo ngati inu mukukhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu, ife tikhalabe abwenzi ndi kumayendera limodzi. Ndipo—ndipo ine ndikukhulupirira kuyeretsedwa kwabwino-kwachikale kukupangitsani inu kumverera moteromo za izo. Sichoncho inu? Uko nkulondola, zitipanga ife kugwirizana.

Monga mwamuna uyu ataima usiku wapitawu, ataima pomwe pano, ndi udindo wa mtundu umenewo. Ndipo—ndipo ine ndakumana . . . Pano pali wansembe waku India pano, pa anthu opitirira mamillioni foro handiredi ndi sevente. Ndipo iye anabwera, ndipo iye anadzamva za izo ndipo iye anabwera kuno, iye anati, "Kodi izi ndi choonadi?"

Ine ndinati, "Izo ndi choncho."

Iye anati, "Ine ndingalandire bwanji Mzimu Woyera?"

"Kusanjika kwa manja." Ndinaika manja pa iye, ndipo Mzimu Woyera unabwera pa iye.

Iye anaima mu Chicago, kuno, masabata pang'ono apitawo, ku msonkhano waukulu wa a Christian Business Men, anati, "Ine ndinali ndi makadinolo onse ndi china chirichonse ataika manja pa ine kumeneko; amuna aakulu, ma bishopu aakulu, ndi ena otero, ataika manja pa ine pamene iwo ankandidzoza ine kukhala arkibishopu waku India, arkibishopu wa Episcopalian ya India ndi purezidenti wa Christian Fellowship of India." Chikhomo chachikulu kwambiri cha chipembedzo mu India. Ndipo iye anati, "Panalibe chirichonse chimene chinachitika pamene iwo anaika manja awo pa ine." Anati, "Ine ndabwera kuno kwa munthu amene sakudziwa ma ABC ake, nkomwe, ndipo iye waika manja ake pa ine, ndipo ine ndalandira Mzimu Woyera." Uko nkulondola. Izo nzachilendo, sichoncho izo? Mwaona.

Kotero, izo sizimabwera mwa maphunziro kapena nzeru; izo zimabwera modzichepetsera wekha pamaso pa Mulungu. Uko nkulondola.

Ndiyeno, umu ndi mmene iwe ungadziwire kuti ndiwe Mkhristu: Ndi zipatso zimene iwe ukubala. Tsopano, osati mmene iwe ukufuulira. Ine ndimakhulupirira mu kufuula, koma izo sizitengera kuti wafuula, kapena ayi, ine . . . kapena—kapena kaya iwe wayankhula ndi malirime, kapena ayi. Uko . . . Ine ndimakhulupirira mu kuyankhula ndi malirime. Izo sizitengera kuti wachiritsa odwala, kapena ayi. Ine ndimakhulupirira mu machiritso. Koma apa pali zipatso za Mzimu: chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza, ubwino, ukoma, chipiliro. Izo ndizo chipatso cha Mzimu. Mukuona? Ndipo ngati zizindikiro

zimenezo zikutsatirani inu, ndiye ine—ine ndikukhulupirira kuti ndizo zimene Yesu anandiuza ine kuti ndiziziyang'ana.

Iye anati, "Ndi ichi anthu onse azadziwa kuti ndinu akuphunzira Anga, pamene inu mukhala . . . " [Osonkhana akuti, "Mukondana wina ndi mzake."—Mkonzi.] Uko nkulondola. "Pamene inu mukondana wina ndi mzake." Ngakhale munthuyo akhoza kutsutsana ndi inu, komabe inu muzimukonda iye chimodzimodzi basi. Mukuona?

Oh, ngati inu mungowakonda iwo amene akukondani inu, inu muli ndi mphotho yanji? Ochimwa amachita chinthu chomwecho. Mukuona? Mukuona? Koma inu muyenera kuwakonda iwo amene amakudani inu, osati kungodzipangitsa kuwakonda iwo, koma kuwakonda iwo kwenikweni. [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Ganizirani za zimenezo. Uko nkulondola. "Ameni" kulondola. Mukuona? Ngati munthu akudani inu kwenikweni, ndipo watsimikiziridwa kuti iye amakudani inu, ndipo komabe mu mtima mwanu inu mukumukondabe iye, inu mukuyandikira pafupi ndithu ku Ufumu. Uko nkulondola.

Tsopano osati kungomukonda iye, nkuti, "Chabwino, ine ndikudziwa ine ndikuyenera kuti ndizichita zimenezo." Koma mumukonde iye mulimonse. Ngati inu simukumukonda iye kuchokera mu mtima mwanu, ngati inu munena kuti mukumukonda iye pamene inu simukutero, inu mukudziwa chimene icho chimakupangani inu? Wachinyengo. Mwaona. Kotero inu musapite ndi kukamuuza iye kuti mukutero pokhapokhapo ngati inu mukutero kwenikweni. Ndipo ngati inu simukumverera mwanjira imeneyo, ingokhalani pomwe pano mpaka inu mutamverera mwanjira imeneyo. Chifukwa ine ndikutsimikizirani inu, pali chisomo chokwanira choti chikupangitseni inu kumva moteromo. Uko nkulondola. Icho ndithudi chidzatero.

Tsopano—tsopano, mafunso awa . . . Ndipo kumbukirani tsopano, izo ziri ngati mmisonkhano, zinthu zonsezo sizikulunjikidwira kwa mpingo wa aliyense, chikhulupiriro cha aliyense, si choncho ayi. Ine ndangokhala mu kachisi wanga wamng'ono pano ndikungowonetsera kumverera kwanga pa maphunziro awa. Mwaona.

Ndipo tsopano, ngati inu mukutsutsana, izo nzabwino. Kodi inu mukudziwa kuti palibepo, nkomwe, awiri aliwonse a ife pano, ndipo palibepo aliyense wa ife pano amene ali ndi chala chofanana. Palibe amene ali ndi mphuno zofanana. Ine ndikuganiza inu ndi okondwa kuti mulibe yofanana ndi yanga. Koma—koma ndiyo . . . Koma palibepo pano aliyense ali wofanana. Mukuona? Ndiyeno ife tikhala osiyana. Tsopano, ine ndikhoza kukonda chitumbuwa cha nthuza ndipo inu mukonda apulo, koma ife tonse tikudya chitumbuwa.

Ndizo basi chi—chinthucho. Kotero, ife . . . Ndiro lingalirolo. Bola ngati ife tikuwakonda Ambuye Yesu, ndipo tinabadwa mwatsopano mwa Mzimu wa Mulungu, ndife Mkhristu. Tsopano, tchalitchi sichingathe kukuchitirani inu zimenezo. Yesu akhoza kukuchitirani inu zimenezo. Mwaona.

Tsopano, mu mafunso awa, kuyang'ana apa, muli zobaya zina mmenemo. Ndipo kotero, poyankha iwo tsopano, aliyense atenge kufufuza kwenikweni kwa izi, mwaona, muzilembe izo: Ine ndikungoyankha izo mwa kupambana kwa kudziwa kwanga ndi Mawu a Mulungu. Mukuona? Ndipo ngati iwo sayankhidwa molondola kwa inu . . . ndipo inu, nkukhala ndi funso lina, bwanji, ndinu . . . Ine ndingakonde kuti inu muliyikenso ilo pa nsanja kapena mudzabwere kudzayankhula ndi ife za izo, kapena chirichonse chimene ife tingakhoze kuchichita. Ndipo mwinamwake M'bale Neville ndi ine pano, ife tikhoza kuwona zinthu zomwe ife sitikugwirizanapo.

Ndipo—ndipo Bambo Baxter, mmodzi wa othandizana naye wapafupi kwambiri mu msonkhano wanga. Bambo Baxter, ife takhala tiri limodzi kwa zaka; ndipo iye ndi wofotokoza weniweni wa Baibulo, koma iye samakhulupirira mu Zakachikwi. Ndipo ine ndikabwera, ndipo ine nkuti, "M'bale Baxter, inu muchita nalo bwanji Lemba ili?" Ine amalumphira mbali imodzi, ine nkuti, "Tsopano, usachite ngati chitete. Iwe ukhazikike." Mwaona. Ndipo ine nkuti, "Ndipo iwo anakhala ndi kulamulira ndi Khristu zaka chikwi pa dziko lapansi." Nkuti, "Nanga bwanji zimenezo?"

Iye anati, "Ine ndikukhulupirira zaka chikwi zimangotanthauza danga linalake."

Ine ndinati, "Tsopano, dikirani miniti, inu mukutenga nzeru. Baibulo linati, 'zaka chikwi.'" Uh-huh. Iwo—iwo ankangolumphalumpha. Koma iwo, mwaona, ife sitinatero, koma, ife sitinadane kaya kuli zakachikwi kapena ayi; ife tikupita kwathu Kumwamba, pamodzi, chifukwa iye anabadwanso mwatsopano ndipo ali ndi Mzimu Woyera.

Kotero umo ndi m'mene ine ndikufuna kuti inu mumverere za mafunso awa: Awa ali basi kupambana kwa nzeru yanga kwa inu.

Ndiye ngati ine nditawona winawake atakhala apa, ndipo iwo akukhulupirira kuti Yesu adzabwera atakwera kavalo woyera, ndipo ine nkumakhulupirira kuti Iye adzabwera mu mtambo woyera; tsopano, ngati ine nditati "kavalo woyera" basi chifukwa chakuti mzangayo akukhulupirira kavalo woyera, komabe, Mwamalemba, ine ndikukhulupirira Iye adzabwera atakwera mtambo, ine ndingakhale wachinyengo. Uko nkulondola. Ine ndiyenera kuti ndidziwonetsere ndekha basi mmene izo ziliri ndi kupereka chifukwa changa.

Paulo anati, "Mukhale okonzeka mu—mu nyengo zonse, mukhale achangu, mu nyengo yake, ndi kunja kwa nyengo; okonzeka kumupatsa munthu yankho la chiyembekezo chimene chiri mkati mwanu." Mwaona. Ndipo izo ndi zimene ife tikuyesera kuti tikhale.

Tsopano, ine ndikumverera kuti Malemba awa, ena a iwo pano, angokhala ndemanga pang'ono chabe, ndi zina zotero, ndipo ine ndiyesera kuti ndiwayankhe iwo poyamba, chimene ine ndayesera kuzipatula izo. Ndipo ine ndiyenera kuti ndikhale ndi izi, ndigwiritse ntchito konkodansi kwa kanthawi pang'ono kuti ndipezemo zina za izi. Ndiyeno, umu, ngati ine ndiwerenga mophonyetsa kapena chirichonse, inu mwangwiro mudzangoitanitsa tcheru changa, inu mukuona, ndipo mudzandilembere ine kolemba, ndi kundiuza ine.

Tsopano, ife tisanayesere kuti titsegule izi . . .

Tsopano, chifukwa chimene ine ndikuchitira izi, abwenzi. Ine ndikuuzani inu, ndi kwa cholinga. Nonse a inu mukudziwa zimenezo. Msonkhano uno unali pa cholinga. Ine ndikukhulupirira Mulungu anandipotoletsa ine, mu mkuntho wa chisanu uja, kujaku, ndipo anandibweza ine pa cholinga ichi pano pomwe. Ndipo pakhala pali chinachake chaching'ono basi cholakwika kuzungulira pa Kachisi kuno kwa nthawi yaitali. Ine ndikufuna kuti ndichipeze icho. Pamene ine ndachipeza icho, ndiye ine ndiwona ngati ine ndingakhoze kuchita chinachake pa icho. Uko nkulondola. Ndipo ine ndikufuna mpingo kuti uziyenda limodzi mu chiyanjano. Ndipo pali chinachake chaching'ono basi cholakwika, chifukwa inu simukupita patsogolo. Inu mukupulumutsa anthu, izo nzoona, izo nzodabwitsa, koma inu simukupita patsogolo momwe inu mukadamachitira. Ife tikadamayenera tizitulutsapo alaliki ndi chirichonse. Uthenga uyenera kuti uzipita patsogolo.

Ine ndinali ndi m'bale wathu, m'busa, panjapo, ndipo ife tadutsa mu mpheroyi limodzi, M'bale Neville ndi ine tatero. Ndipo ine—ndipo ine ndikufuna kuti ndiwone ngati . . . Monga mmodzi wa azibusa anu, ndi—ndi ntchito yanga. Ndipo usiku wathawu . . . Basi pamene ine ndiwona chirichonse chimene chiri mu mpingo tsopano, ndicho chifukwa ine sindinaulengeze konse msonkhano uno. Ine ndangowupereka iwo apa; basi, bwanji, aliyense ali wolandiridwa. Zedidi, ife tikufuna kuti inu mubwere. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] Ndipo, koma, zangokhala mu mpingo uno.

Ndipo ine ndinaganiza, "Ngati ine nditi ndiphunzitse pa usiku woyamba, chimene mpingo lero . . . ndi m'badwo, mwapamalo, mu Baibulo, pamene ife takhala mwapamalo, ndiye mpingo ndithudi uwuka pa izo. Ndipo kenako ndidzayankhula pa 'chilemba cha chirombo,' ndi kuwalola iwo kuti awone chomwe icho chiri; ndipo kenako 'Chisindikizo cha Mulungu.'"

Ndizo zoyenera ndi zosayenera tsopano, uwo ndi mdima ndi Kuwala tsopano, uwo ndi mwina mkati kapena kunja tsopano, ndipo icho ndi chinthu chofunika kwambiri kuti chiziphunzitsidwa tsopano.

2 Ndipo ine ndikukuuzani inu, abwenzi, ine ndikunena izi kuchokera mu mtima mwanga, pamaso pa Mulungu, modzichepetsa, ine sindinayambe ndamvererapo kudzoza kwa Mzimu Woyera kuti ndiyankhule mawu momwe ine ndawayankhulira mu mausiku atatu apitawa. Uko nkulondola. Koma izo zangonditengera ine kutali. Ine ndikapita kunyumba, sindimakhoza ngakhale kugona ndikafika kunyumba, kudzoza koteroko basi!

3 Tsopano, ine ndiponyera *izi* umo poyembekeza kuti ndipeza chinachake penapake. Mukuona? Ndipeze—kumverera kwa anthu onse pa chidutswa cha chipepalachi apa. Ngati ine sindizipeza izi mwanjira iyi, ndipo Ambuye akapanda kuululira izo kwa ine, ine ndizipitirirabe mpaka ine nditazipeza izo. Ndipo Mulungu adzazipereka izo kwa ine. Ndiko kulondola. Ndipo chotero ndiye pamene ife tizipeza izo, izo zikhoza kungokhala mwina zapang'ono chabe, chikho chakale chitabisidwa penapake, koma Akani anali nacho chimodzi, nayenso. Inu mukudziwa, ife tiyenera tichichotse chinthu chimenecho, tikatero ife tidzabwera apo ndi kumasuntha chamtsogolo mu Ufumu wa Mulungu.

4 Tsopano, Ambuye akudalitseni inu. Ndipo tsopano ife tisanatsegule Mawu . . . Ndipo tsopano—tsopano, mmodzi aliyense wa inu amene amakhala ndi Sande sukulu mmawa, ndithudi, muli . . . ine—ine sindingakufunseni inu kuti muphonye Sande sukulu yanu, a—awo ndi malo anu antchito ku tchalitchi kwanuko. Uko nkulondola. Koma, tsopano, ngati inu simupita ku Sande sukulu, dzabwereni ndi kudzatiwona ife mmawa. Ndiyeno ngati tchalitchi chanu sichikhala ndi misonkhano mawa usiku, Lamlungu, ndinu wolandiridwa. Ife tidzakhala okondwa kudzakhala nanu inu pa nthawi iliyonse. Ndipo kotero Ambuye akudalitseni inu. Ndipo mukandipatsire moni Akhristu onse; ine sindimabwerabwera kuno mochuluka kwambiri.

5 Ine ndinali kungoyang'ana mchipinda uko, pepala laling'ono limene ine ndinalemba umo likadali umu ngati chikumbutso kwa mpingo uno. Ndipo ine ndinati, "Ambuye akundiitanira ine kwina," ndipo ife tonse tinalira ndi misozi. Ine ndikukumbukira usiku woyamba womwe ndinapita. Inu nonse mukukumbukira kuitanidwa kwanga koyamba, aliyense pano? Inu nonse munaikapo ndalama kuti munditumize ine ku St. Louis uko, kumene Betty Daugherty wamng'ono anakachiritsidwa. Ine ndinakhala . . .

6 Mukukumbukira, ine ndinabwereka chikhoto cha winawake kuno kuti ndivale. Ine ndinalibe chikhoto chirichonse

choti ndivale. Ndipo ine ndinapita uko ndi kukakhala mu mpando wakale wa galimoto kuti ndizipita ku St. Louis. Inu mukuikumbukira nthawiyo? Ndipo ine ndinabwereka chimodzi cha zikhoto za abale, icho chinali chachikulu kwambiri kwa ine, ine ndinachinyamula icho pa nkono wanga; chifukwa kunali kukuzizira ndipo ine ndinalibe chikhoto.

7 Ndiyeno ife tinapita uko, ndipo ine ndinapita ku St. Louis ndipo ine ndinakakomana naye M'bale Daugherty uko. Mtsikana wawo wamng'ono, madokotala onse cha kumeneko, ndi akatswiri ndi zipatala, anali atamulephera iye. Iye anali ngati wamisala wowopsya. Atumiki kuzungulira mzindawo anali . . . konsekonse, kumeneko akumupempherera iye. Ndipo ine ndinapita ndi kukamupempherera iye, ndipo anthu osaukawo ankangowoneka otuwa kwambiri. Ndipo msungwana wamng'onoyo mmenemo, akukuwa ndi kufuula, akumenya.

8 Ndi—ndipo iye samakhozanso kupanga phokoso monga munthu, ankamveka ngati chinyama, iye anali atasasa mawu kwambiri . . . o, pafupi miyezi itatu kapena inai. Iyo inali meninjaitisi ya munsana kapena . . . ayi, dansi ya Saint Vitus, mu—mu nsana. Ndipo milomo yake yaing'onoyo yonse inali itadyedwa, ikuwukha magazi. Ndipo zala zake zazing'ono izo zikungowukha paliponse, pamene iye anali kuziluma zala zake, ndi zinthu monga choncho, ndipo ankangokuwa ndi kumapitirira nazo.

9 Ndipo ine ndinapemphera, ndinapita ku tchalitchiko. Ndinakadikirira maora pambuyo pa maora. Ndinakakhala mu galimoto yakale ndipo ndinadikirira. Ine ndinali woti sindilisiya vutolo mpaka ine nditamva kuchokera Kumwamba. Ndipo nditakhala pamenepo mgalimoto, masomphenya anatseguka patsogolo panga, anati, "Pita ukawauze bambo ake, ndipo abambowo . . . " Anati, "Iwe pita ukamuuze mkaziyo kuti tsiku lina, kumusi kwa mzinda, iye anagula ketulo yaing'ono, yoyera. Iyo siinayambe yaikidwamo madzi ndi kale lomwe." Ndipo anati, "Ukamuuze iye kuti akayang'ane mu kabati yachitatu ndipo iye akapezamo mpango wammanja womwe uli mu chidutswa cha pepala, womwe sunayambe wagwiritsidwapo ntchito kale. Ukamuuze iye kuti akaidzazitse iyo ndi madzi. Ukawaimitse bambowo ku dzanja lako lakumanja, ndi agogo aamuna ku dzanja lako lakumanzere, ndipo ukabwereze, 'Atate athu, Omwe muli Kumwamba . . . ' Ndipo pamene iwe uzikayamba izo, ukamulole iye apukutire kampangoko pa nkhope yake. Ndiye mkati mwa pempherolo ukamulole iye kuti akagwire manja ake, kenako mapazi ake. Ndiye ukaime ndi kuti, 'PAKUTI ATERO AMBUYE!'"

10 Inu mukudziwa zomwe zinachitika, sichoncho inu? Iye anachiritsidwa pomwepo. Ndipo ife tinaika manja athu pamodzi ndipo tinayenda chotsika msewuwo ndi kumwa zotsekemera za soda, limodzi. Uko nkulondola. Uko nkulondola. Izo

zinaikondoweza St. Louis; msonkhano wanga kumeneko, zikwi fortini usiku woyamba. Uko nkulondola. Ku St . . .

11 Ndi zoipa kwambiri basi kuti ine ndinachokako uko; kupita ndi kukangoyambitsa kuti iwo azibwera kudutsa mu mzere, basi mmodzi pambuyo pa winayo, pambuyo pa winayo. Kungopita kunyumbayo ndi kukakhala uko mpaka izo zitatha, ndi kumabwerera kwathu, ine ndikukhulupirira izo zikanakhala bwinoko kusiyana ndi mu misonkhano.

12 Chabwino, tiyeni tiweramitse mitu yathu pamene ife tikuyankhula kwa Mwini wa Mawu awa, tsopano.

13 Mu chifundo cha Ambuye wathu Yesu Khristu, ife tikukuyandikirani Inu, Atate athu. Ndipo mu Dzina Lake ife tikupempha chifundo Chaumulungu, kuti Inu mutikhululukire machimo athu ndi zokulakwirani Inu. Ndipo ngati pali tchimo lirilonse mu mpingo waung'ono uno usikuuno, ife tikupemphera, Ambuye, mo—monga wantchito nditaima pano, monga m'busa pa nkhosa . . . Monga Baibulo linati, "Mvetserani kwa nkhosa zomwe Mzimu Woyera wakupangani inu woyang'anira pa izo, kuti inu muzizidyetsa izo." Ndipo tsopano, Atate, ine ndikuwapembedzera iwo, kuti Inu muwadalitse iwo ndi kuwachotsera machimo awo onse. Chizani matenda omwe ali pakati pa anthu. Ndipo, Atate Akumwamba, ine ndikupemphera kuti zifundo Zanu zikhale pa ife tsopano.

14 Apa ziri patsogolo pa ine, zolembedwa pa pepala, kuchokera ku nyumba zambiri ndi anthu ambiri, pali zopempha, mafunso okuya enieni a Baibulo omwe akupita kupyola kuphunzira wamba. Ndipo ife tikusowa thandizo Lanu, Ambuye Yesu. Ndipo ndangozitenga izi tsopano, poyenda kulowa mu chipinda, kukhala ndi pemphero, kutulukamo, kuwalekanitsa iwo pano, ndi kuikapo iwo omwe ayenera kuti ayankhidwe tsopano ku mbali imodzi, ndi ena omwe ayenera kuti apite mu Lemba, ku inayo. Ndimo momwe ine ndikuzidziwira izo pa nthawi ino, Ambuye.

15 Ndipo ine ndikupemphera kuti kuyambira pakali pano Inu mutenge kuchokera apa kupitirira, ndipo adzozeni anthu Anu pano usikuuno, milomo ya woyankhula, makutu a womvetsera. Ndipo mulole Mzimu Woyera ubwere ndi kudzawagwira Mawu tsopano ndi kuwapititsa Iwo mpaka mu mtima uliwonse, ndipo mulole Iwo akalandiridwe mwa mzimu wachifundo, ndipo mulole Iwo aperekedwe chimodzimodzi. Ndipo mulole, pamene msonkhano utha usikuuno, mulole ife tipite kwathu, tikuti, "Kodi mitima yathu siinali kutentha mkati mwathu chifukwa cha Kukhalapo Kwake ndi madalitso Ake?" Ambuye, posadziwa choti nkunena, ine ndikudzipereka mwiniwanga kwa Inu ndi mafunso awa, mu Dzina la Yesu Khristu, pofuna yankho. Ameni.

16 Zikomo, abwenzi, chifukwa cha kulemekeza kwanu. Ine ndikungofuna kuti ndikusonyezeni inu zomwe ambiri, ochuluka

a mafunso awa anali.

M'bale Bill, chonde pitirirani nazo mpaka sabata yamawa.

Chonde mukhalepo sabata lina.

Chonde mukhalepo motalikitsa pang'ono.

M'bale Bill, chonde mukhalepo sabata yamawa, motalikitsapo pang'ono, miyoyo yathu ili ndi njala kufuna mtundu uwu wa Chakudya.

Kodi mpingo uno umaphunzitsa kuti...Ilo lango...Ilo linagwera mmenemo. Ilo liri pa malo olakwika.

Ine ndiri nawo anyamata awiri, awusinkhu wa ziwiri... Izo ndi, ine ndazisakaniza izo, ine ndikulingalira, pa izo. Tsopano, apa, ine kulibwino ndizitengere izo uku, apanso, izo ndi zokhudza za payekha.

M'bale Bill, kodi inu—kodi inu mungakonde sabata imodzi inanso? Ife tikanakonda sabata imodzi inanso ya kuphunzitsa kwa Uthenga uku.

Chopempha changa ndicho kuti inu mukhale sabata ina. Ine ndikanakonda mochuluka kwambiri kuti inu mukhale motalikirapo pang'ono, inu mukudziwa ife timakhala nthawizonse...ife tikhoza nthawizonse kuphunzira zochulukirapo.

Tsopano, kodi inu mungakhalepo utali wa sabata ina yokha, chonde?

M'bale Bill, chonde mutilalikire sabata imodzi ina ife. Ife tikuzisowa izi.

M'bale Bill, pemphero langa ndi lakuti Mulungu asinthe malingaliro anu ndi kukupangitsani inu kukhalapo sabata lina.

Funso langa liri: Kodi mbale zouluka ndi chiani, ndipo kodi izo ziri chinachake chochokera kwa Mulungu chitatumizidwa kuno mwa chizindikiro? Ndipo ine ndikukupemphani inu kuti mukhale sabata lina.

Chonde mukhalepo sabata lina.

17 [M'bale Branham akuyankhula ndi M'bale Neville—Mkonzi.]

18 Tsopano, apa panali mmodzi wina yemwe anati ine ndinga...i—ine ndikuyamikira kufunsa uku. Ndipo Mulungu Wamphamvuzonse Yemwe ali Wondiweruza wanga, nditaima pano tsopano mu malo opatulika awa...ine ndisanachoke kunyumba, Mzimu wa Ambuye unandiuza ine, unati funso ili lidzakhala liri apa usikuuno. Ine sindimadziwa kanthu za izo, koma ine ndimadziwa kuti ilo likanadzakhala pano:

Kodi Mboni za Yehova ndi kagulu kabodza?

19 Onani, winawake . . . Ndipo Mzimu Woyera, pa malo a . . . nditaima mu ku bafa, ndisanabwere kuno; Mulungu, Yemwe ali Woweruza wanga wakachetechete, anandiuza ine, "Kuti lidzakhala liri pa nsanja," ndipo anati ine ndisati ndidzanene "kanthu pa izo; ndizidzangopitirira nazo basi." Mwaona? Chotero ine . . . Inu mukudziwa zomwe ine ndinanena usiku watha, sichoncho inu? Chabwino, izo ndi zomwe zinali.

20 Chabwino, tsopano ife tiyambira cha apa pa zina za izi.

21 Ine sindimangokonda kutchula chinthu china chirichonse, ndi kutchula munthu wina kapena munthu payekha monga chomwecho. Ine ndimangokonda kuziphunzitsa izo mwanjira basi ya . . . kuponyera chinthu chonsecho palimodzi. Ndi—ndipo inu mukumvetsa, sichoncho inu? Ngati ine ndingaime pano ndikuti, "Tsopano, M'bale Neville ndi *wakuti-n-wakuti* ndi chinthu *chakuti-n-chakuti*" . . . Ngati ine ndikanakhala nacho choti ndinene za iye, ine ndikanapita kunyumba kwake ndi kumuitana iye ndi kuyankhulana naye iye pa izo. Mwaona, ine—ine ndikanamuuza M'bale Neville.

22 Koma tsopano, pano pali mafunso ena. Tsopano, ine sindikudziwa kuti ndiyambire pati, wangokhala mulu wa iwo omwe ali apa. Ilo likuti:

25. Ndi chilumikizano chotani chimene inu mumatanthauza kuti mpingo wa Chiprotestanti uli nacho ndi mpingo wa Katolika?

26. Kodi "fano la chirombo" limatanthauza chiyani?

23 Tsopano, ilo linali limodzi la mafunso kuchokera ku wathawo . . . mwinamwake linali pa anthu . . . Tsopano, ine ndiyesa mwa kukhoza kwanga, mwa kuthandizidwa ndi Mulungu, kuti ndiwayankhe iwo mwakupambana kwa kudziwa kwanga. Tsopano ngati Iye ati andipatse ine chidziwitso, chifukwa Mulungu akudziwa i—ine ndinangowatola iwo, pa nsanja pano.

Tsopano, ndi chilumikizano chotani chimene inu mumatanthauza kuti mpingo wa Chiprotestanti uli nacho ndi mpingo wa Katolika?

24 Tsopano, ine ndiyankha ilo poyamba, Mulungu andithandize. Ine ndinanena kuti mpingo wa Katolika unali . . . Ife tikupeza kuti chilemba cha chirombo, usiku wa dzana, chimayenera kubwera kuchokera ku Roma. Ndi kulondola uko? Icho sichingakhoze kubwera kuchokera ku dziko lina ayi kupatula Roma. Uko ndi kumene icho chiri, uko ndi kumene icho chinaikidwako. Ndipo ine ndinati ine ndiribe kanthu kotsutsa anthu a Katolika, ndiribe kotsutsa aliyense. Ndife tonse zivundi tikuyesera kuti tikafike Kumwamba.

25 Papa ndi munthu mmodzi yemwe amaphunzitsa, arkibishopu waku Canterbury ndi winanso, ndi wina, ndi

wina, ndi wina; ndipo ine ndine basi mmodzi wa aphunzitsi, ndizo zonse. Iwo angaphunzitse ndi kumati, mwinamwake, ine ndinali wotentheka ndipo ine ndinali kulakwitsa, ndi zina zotero. Ndipo ine ndiri nawo ufulu . . . ngati ine ndingakhoze kutsimikizira izo mwa Lemba. Kapena ngati iwo angakhoze kutsimikizira izo mwa Lemba kuti ndine wotentheka, ndiye ndine wotentheka. Koma ngati ine ndingakhoze kutsimikizira mwa Lemba kuti iwo akulakwitsa mu dongosolo lawo, ndiye nkulakwitsa; Lemba likulondola. Ndipo inu sikuti muli nawo malo amodzi tsopano, izo ziyenera kubwera njira yonse kudutsa mu Baibulo, kulikonse.

26 Tsopano, ine ndinati, "Mpingo wa Katolika unali manthu wa mpingo," ndipo izo ziri ndendende zolondola. Mpingo wa Katolika ndi manthu mpingo, pamene izo zifika ku mabungwe a mpingo. Mpingo wa Katolika unali mpingo woyamba umene unayamba wapangidwapo, cha pafupifupi . . . mbiriyakale yapamwamba, inu muli nazo izo pafupifupi A.D. 606, penapake cha kumeneko pamene makolo oyambirira, kuzungulira kwachiwiri kapena kwachitatu, kwa atumwi. Iwo anali atafa ndipo anayamba kumwazikana mu timalingaliro tating'ono. Ndipo Aroma, pokhala atatembenuzidwa, Ufumu wa Chiroma unkalamulira pa boma, ndipo kenako mpingo ndi boma zinalumikizana palimodzi ndipo anayambitsa chipembedzo chotchedwa "chipembedzo cha konsekonse." Ndipo mawu akuti *Katolika* amatanthauza "konsekonse." Iwo anaupanga bungwe mpingo, yomwe inali nthawi yoyamba yomwe chipembedzo, chipembedzo cha Chikhristu, chinayamba chapangidwa bungwe mu mbiriyakale yonse ya mdziko.

27 Chipembedzo cha Chiyuda sichinali konse bungwe. Iwo anali anthu aufulu. Iwo anali nayo mipingo, koma iwo analibe bungwe. Pakuti, Mulungu ankachita ndi fuko, osati bungwe. Ilo linali fuko.

28 Ndipo tsopano. Ndipo, ndiye, mpingo wa Katolika unali bungwe loyamba. Kenako ife tinazitenga izo mu Baibulo kuti tikapeze chomwe bungwe ilo linali. Ndipo molingana ndi Mawu a Mulungu, ilo linkayenera kuti lizilamuliridwa ndi munthu mmodzi, munthu mmodzi. Ndipo munthu ameneyo anali woti azikhala mu mpingo umene unaikidwa pa mapiri asanu ndi awiri mu Roma, molingana ndi Baibulo. Palibe ayi . . . Ndipo iye ankayenera kuti akhale ali ndi mphamvu zolamulirira mu fuko lirilonse mu dziko, mphamvu yolamulirira mwachipembedzo. Palibe inanso mu dziko.

29 Ndi—ndipo Chikominisi, ife tinapeza kuti, sichinali si—si wotsutsakhristu yemwe Yesu ankamukamba. Chikominisi si—si fuko, monga Russia. Chikominisi ndi mzimu. Amereka wadyedwa nawo iwo. Iwo uli mu mipingo, iwo uli mwa anthu, iwo uli mu zintchito, iwo uli paliponse. Chikominisi, mzimu wakewo, uli mu masukulu, uli mmanyumba, konsekonse.

30 Ndiyeno—kenako pamene iwo anapanga bungwe mpingo uwu chomwe chinali chosiyana. . . Ndipo tsopano ife taitenga Mibadwo ya Mpingo Isanu Ndi Iwiri, ndi uneneri, ndendende momwe Mulungu anawadutsitsira iwo mu Baibulo apa kwa ife. Ndipo ife tinazipeza mwa mbiriyakale ndi Baibulo, kuti m'badwo uliwonse unkabweramo basi molingana ndi Baibulo, molingana ndi mbiriyakale; uliwonse unkabweramo basi pa nthawi yake, kudutsa mibadwo ya mdima. Ndipo zitatero mpingo wa Katolika unapangidwa mu M'badwo wa Mdima.

31 Ndiye kukonzanso kunabwerapo, yemwe ali Marteni Lutera. Ndipo Marteni Lutera anali nako kuwala, kuwala kwakuti "Olungama azikhala moyo mwa chikhulupiriro; kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro," mu—mu kukonzanso. Wansembe wachi German yemwe anakana ndipo ananena kuti kudya mgonero pamene iye anaugwirizira iwo. . . Ndipo iwo ankayenera kumanena kuti "*ili* ndi thupi la Khristu," ndipo iye anauponyera iwo pansi ndipo anati, "Ili *si* thupi la Khristu; ndi kokulumunya!" Ndipo kotero iye anaukana mpingo wa Katolika, pa kuchita motero, ndipo anatulukamo mu kukonzanso koyambirira. Marteni Lutera anachita zimenezo, ndipo uko kunali kusuntha kodabwitsa.

32 Tsopano, kulakwitsa, pamene Lutera anapangira kulakwitsa kwake, Lutera anapanga bungwe gulu lina monga momwe mpingo wa Katolika unachitira, anawapanga bungwe anthuwo.

33 Zitatero, molunjika, kuwala kwatsopano kunabwerapo. Ndipo pamene kuwala kwatsopano kunabwerapo, Mulungu anatuluka ndi anthu Ake. Anthu omwe anadzipanga bungwe mu mpingo wa Lutera, iwo anayenera kutsala ndi mpingowo polinga kuti akhale ndi. . . Izo ndi chimodzimodzi basi monga momwe Akatolika ankayenera kukhala ali, koma ambiri a Akatolika anatulukamo ndipo anali Achilutera. Chabwino, ndiye pamene Wesile anabwera motsatira ndi uthenga wa kuyeretsedwa, ndiye ambiri a Achilutera sakanakhoza kuwusiya mpingo wawo; koma ambiri a iwo anatero, ndipo anapanga mpingo wa Wesile.

34 Ndiye pambuyo pa kulungamitsidwa ndi kuyeretsedwa, motsatira kunadza Chipentekoste. Ndiyeno Chipentekoste, ambiri anatuluka mu Methodisti, ndi mwina motero, ndipo anadzakhala Achipentekoste chifukwa kumeneko kunali kuwala kokulirapo. Tsopano Chipentekoste chapanga bungwe mofanana basi monga aliyense wa iwo!

35 Tsopano, Baibulo limanena kuti. . . Awa ndi mawu osabisa, koma ine ndikuwawerenga iwo kuchokera mu Baibulo. Ndipo inu mumamvetsera kwa dokotala wanu, kapena ena otero, akamanena izi, ndipo ndine m'bale wanu ndikuphunzitsa kuchokera ku Lemba. Baibulo linawutcha mpingo wa Katolika, "wachiwerewere, hule, h-u-l-e." Ndipo Iye anaitcha mipingo ya Chiprotestanti yomwe inautsatira iwo, azimayi. . . kapena

iwo anali "timahule ta mayi uyu." Ndipo chinali chilumikizo chotani, kuti mpingo wa Katolika unapanga bungwe chinthuchi ndipo unawapangitsa anthu onse kukhulupirira mwa kuwala komwe iwo anali nako pamenepo, kapena zomwe iwo anali nazo apo. Achilutera anachita chinthu chomwecho. Ndipo Baibulo linanena kuti iye anali mkazi wamkulu wa mtundu umenewo.

36 Tsopano kodi ndi mtundu wanji umenewo wa mkazi? Ndi mkazi yemwe amakhala ndi kumachita chigololo. Ndipo mipingo ikuchita ziwerewere zauzimu ndi—ndi anthu. Mukuona? Iyo ili—iyo ili...Pano pali Baibulo limene limaphunzitsa Izi, ndipo iwo amapanga kamtolo ka tizikhulupiriro ndi zina zotero zimene ziribiretu kanthu kochita ndi Baibulo. Ndipo, pakuti, izi ndi pafupifupi zaka twente *ndichakuti* ine ndakhala ndikuima pomwe pano ndipo ndafunsapo mtumiki aliyense, pa nthawi iliyonse, kuti abwere ndipo atenge...osati bukhu lanu la zolewerenga, kachikhulupiriro kanu, koma mubwere mudzatenge Baibulo, mwa Kuwala kwa Baibulo, ndipo mudzalitsimikizire kuti Ilo ndi lolakwika. Mukuona? Uko nkulondola.

37 Ndipo pa zotsutsana, iwo amati, "Nzotsutsana!" Ine ndaperekapo kuchuluka kwa malipiro a miyezi iwiri ngati winawake angandiwonetse ine kutsutsana kumodzi mu Baibulo. Iko mulibemo umo. Inu mukuganiza kuti kulipo mmenemo, koma iko mulibemo. Ngati Baibulo limadzitsutsa Ilolokha, ilo si labwino nkomwe, inu simungakhoze kulikhulupirira ilo. Mawu aliwonse ndi owuziridwa ndipo mulibe kutsutsana mu Baibulo.

38 Tsopano mpingo wa Chiprotestanti, mu chipembedzo chake, uli (molingana ndi Mawu a Mulungu) wolumukizana nacho chinthu chomwecho ndi mpingo wa Katolika.

39 Tsopano, ine ndiribe kanthu kotsutsa anthu a Chikatolika. Ena a abwenzi anga okondedwa kwambiri akhala pomwe pano tsopano, ndi mphukira za anthu a Chikatolika. Pano, usiku wa dzana, pamene ine ndinapereka uthenga wolimba mwa Mzimu Woyera, pa Chiprotestanti ndi Chikatolika, Akatolika anayenda nadza pompano pa guwa ndi kudzagwira dzanja langa. Iwo ndi anthu chimodzimodzi monga momwe ife tiriri.

40 Inu simungakhoze kukambirana ndi ansembe a Chikatolika, chifukwa iwo samalikhulupirira Baibulo ili kuti lonselo ndi Mawu. Iwo amati, "Ndi mpingo." Ife timati, "Ndi Baibulo!"

41 Akatolika amati, "Ife Akatolika tizipita ku tchalitchi kukapembedza. Inu Achiprotestanti muzikhala kunyumba ndi kumawerenga Baibulo."

42 Ine ndinati, "Eya, inu mumapita ku tchalitchi ndi kukapembedza, komano chiyani?" Ndicho chinthu chotsatira, mwaona.

43 Tsopano, koma Mulungu anati Iye ali mu Mawu Ake. Awa ndi Mawu a Mulungu ndipo ine ndimawakhulupirira Iwo. Ndine

wopembedza Baibulo. Ndicho chifukwa ine sindigwirizana ndi Chiprotestanti ndi—ndi njira ya—ya bungwe la mpingo basi, chifukwa iwo amaphunzitsa zinthu zomwe siziri Mawu a Mulungu. Chotero ine sindingakhoze kusiya kuwatsutsa. Ine sindimalekana nawo iwo; ayi, bwana, iwo ndi abale anga. Ndipo ine sindimalekana nawo iwo, koma ine sindimagwirizana nawo iwo chifukwa ine ndimayenera kuti nditenge chimene Mulungu akunena ndipo china chirichonse chidzikhala bodza. Mukuona?

44 Ndipo tsopano ndicho chilumikizo chimene. . . Ndipo tsopano Baibulo linanena kuti mayi uyu, mpingo wa Katolika, umene ukuyenera kuti udzitchedwa, mu Baibulo, Chivumbulutso mutu wa 17. "Hule," ndipo iye anali, "MAYI WA TIMAHULE." Ndipo ife tikuona kuti Baibulo linanena kuti *mkazi* ankaimira "mpingo." Chotero ndiye ngati iye anali nawo ana aakazi omwe ali timahule, iwo sakadakhoza kukhala ali anyamata; iwo amayenera kukhala ali ana aakazi, kotero iyo inayenera kukhala ili mipingo. Ndipo Chiprotestanti chinabadwa kuchokera mu Chikatolika.

45 Ndipo tsopano chotsatira, chirombo. . . Kapena, chinthu chotsatira chimene ili likunena:

Kodi "chifano cha chirombo" chimatanthauza chiyani?

46 Ndi—ndi funso lolumikizana kwa ilo, ndipo munthu yemwe anafunsa iloli ali ndi funso labwino. Chomwe chikupangidwa tsopano, ngati. . . Baibulo mwachimvekere limaphunzitsa kuti mpingo wa Katolika ndiwo—chirombo. Baibulo linanena kuti *chirombo* chimatanthauza "mphamvu." Nkulondola uko? *Chirombo,* Baibulo limanena kuti *chirombo* chimatanthauza "mphamvu." Ndipo *chirombo* chinali "Mzinda wa Vatikani," "ulamuliro wolowezana wa Chikatolika." Chabwino. Ndipo, tsopano, imeneyo inali mphamvu ya mpingo imene inali chirombo.

47 Ndiye mpingo wa Chiprotestanti unatuluka kuchokera mu mpingo wa Katolika, ndipo anadzipanga bungwe iwoeni, kamphamvu kakang'ono. Icho ndicho chifano.

48 Ngati chirichonse. . . Ngati chinachake chinapangidwa mwa chifanizo changa, icho chikanati chiziwoneka monga ineyo. Ngati chinachake chipangidwa mwa chifanizo cha mpingo uno, icho chiyenera kuti chiziwoneka ngati mpingo.

49 Chinachake chinapangidwa, chirombo. . . chinapanga fano kwa chirombo ichi, chimene chinali Chi-lutera, Chi-methodisti, Chi-baptisti, Chi-pentekoste, Chi—holiness, timalingaliro tonse ito tinapangidwa mu bungwe ndipo tinapanga fano mofanana monga chirombo. Ndi izo apo!

50 Tsopano, "Kodi inu mukunena tsopano, M'bale Branham, kuti Achikatolika onse, Achimethodisti onse, ndi Achibaptisti onse akupita. . . ?" Ine sindinanene choncho.

51 Ziripo zikwi ndi zikwi ndi makumi a zikwi za Akhristu obadwa kachiwiri mu mipingo imeneyo. Koma, mu bungwe lawolo, iwo akuyesera kumawatsogolera iwo ku kachikhulupiriro, ndipo iwo sangaime nazo izo. M—mpingo, pamene iwo upanga bungwe, iwo umadza pansi pa kachikhulupiriro.

52 Ndipo ine ndiribe kachikhulupiriro koma Baibulo. *Ili* ndi Kachikhulupiriro ka Mulungu, ndipo Mzimu Woyera ndiye wotanthauzira wake wa Ilo, ndipo Iye amalibweretsa Ilo mopitirira kuchokera ku Kuwala kumodzi kupita ku kumzake. Uthenga umene ine ndikuulalikira lero, ngati ine nditi ndidzakhale moyo kuti ndidzawone zaka zina zana, ngati ife tikadadzatero, pakanadzakhala pali kuwala kochulukirapo. Komangopitirirabe, Iko nthawizonse kumabwera.

53 Inu munkakwera mu ngolo ya ng'ombe, agogo a agogo anu aamuna, pamene iwo ankapita kukawona agogo aakazi. Adadi ankapita kukawaona amayi mu T.-Model. Koma tsopano ife timapita pafupifupi mu ndege ya jeti. Mwaona, ife tiri kusunthira mtsogolo; sayansi, ikusunthira mtsogolo; maphunziro akusunthira mtsogolo; Uthenga ukusunthira mtsogolo. Ndipo Baibulo linati iwo akadadzatero, anati, "Iwo azidzathamangira kuno ndi uko, ndipo chidziwitso chidzachulukira." Chotero ndiko kulumikizikako. Ndi chifukwa chake pali . . .

54 Mipingo ya chipembedzo ya Chiprotestanti ndiyo fano la chirombo, chifukwa yadzipanga chipembedzo basi ndendende momwe Chikatolika chiri. Ndipo Mulungu sanalamulirepo konse Mpingo Wake kuti udzapangidwe bungwe mu m'badwo uliwonse, koma wakhala nthawizonse akuzitsutsa izo mowawitsa! Tsopano kodi inu mukuzimvetsa izo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Osati anthuwo; mpingo!

55 Pamene iwo akuyesera kuwabweretsa anthu pansi p—pa kuwala kwa . . . Apa, bwanji ngati anthu atamayesera kukupangitsani inu kuti mupite mmbuyo ndi kukayamba kumakathamanga uko mu ngolo ya ng'ombe? Inu simukadachita izo; ife tikukhala mu m'badwo wabwinoko. Umo ndi momwe izo zinaliri kumbuyo uko. Ngati winawake atayesa kumandiuza ine, "O, chinthu chokha chomwe inu muyenera kuti muchite ndi *ichi, icho*." Ine ndikukhala mu m'badwo wina! Ine . . . Ilo ndiro vuto ndi atumiki, iwo nthawizonse amayang'ana mmbuyo.

56 Kuno, wasayansi wa Chifaransa anati, mochepera zaka firii handiredi zapitazo, "Ngati munthu akadadzatha kupangapo liwiro lowopsya la sate mailosi pa ora, kukoka kwa dziko kukadadzamchotsa iye pa dziko lapansi. Mailosi sate pa ora!" Chabwino, kodi inu mungaganize kuti sayansi ingamalozere mmbuyo kwa izo lero? Zikhale kutali izo! Ayi, bwana. Iwo amufikitsa iye pomapita pafupifupi naini kapena mailosi teni

handiredi pa ora. Eya, kapena nthawizina mu roketi, ndiyeno ndi mailosi sikisitini handiredi pa ora. Ndipo akupitirizabe kumutengera iye mtsogolo!

57 Sayansi yamutengera munthu patsogolo, patsogolo mochuluka, mu zinthu zokulirapo ndi malingaliro ake kuposa chimene . . . Ndipo icho ndi chinthu chokha chimene iye ali nacho, ndi mtengo wa chidziwitsowo. Patalipo kuposa momwe atumiki akumutengera iye ndi Mzimu Wake, umene ulibe malire. Koma pano ndi chomwe chiri. Sayansi siili kuyang'ana mmbuyo ku chimene sayansi inkanena zaka zingapo zapitazo; sayansi ikumatenga chimene iwo ali nacho tsopano ndi kumasunthira mtsogolo kupita ku chinachakenso.

58 Koma inu mumufunse mlaliki, "Chabwino, ife tiwona chimene Moody ananena pa Izo, ife tiwona chimene Wesile ananena pa Izo." Ine sindikusamala chimene iwo ananena pa Izo. Ine ndikudziwa chimene Mulungu wanena pa Izo *tsopano*. Ichi ndicho, ndipo ine ndikadali kuyang'anira chokulirapo! Ndi zimenezotu. Ndicho chifukwa . . .

59 Baibulo linati, "Mizimu yonyansa itatu inatuluka kuchokera mkamwa ya chirombo." Kodi inu mukudziwa chiyani? "Mizimu yonyansa," linati, "yonga achule." Kodi inu munayamba mwazindikira momwe chule amawonekera? Chule nthawizonse amayang'ana cha mmbuyo, iye samayang'ana konse cha mtsogolo; kuyang'ana mmbuyo, nthawizonse mmbuyo, kuyang'ana mmbuyo.

60 Koma zirombo zinaizo zomwe zinali ndi mitu inai yosiyana, mu Ezekieli, zinali kuyang'ana kutsogolo ndipo izo sizikanakhoza kupita cha mmbuyo. Izo zinali kusunthira mtsogolo nthawi zonse. Kulikonse komwe zinkapita, izo zinali kupita mwachindunji kutsogolo. Mukuona kusiyanako?

61 Tsopano, uko ndiko kulumikizana kumene Chiprotestanti chiri nako ndi Chikatolika.

62 Chotero inu nthawizonse mukumaziponyera pa Achikatolika, koma "mpoto sungatche ketulo 'kuda.'" Ndiko kulondola.

63 Ine ndikati, "Kodi ndinu Mkhristu?"

64 "Ine ndikupatsani inu kumvetsa kuti ndine wa mpingo wa Chibaptisti." Eya. Izo ziribenso chochita ndi Izo monga kunena kuti inu ndinu wa kuno ku . . . famu kwinakwake.

65 "Bwanji, ine ndine wa mpingo wa Katolika." Izo sizikupanganibe inu apobe Mkhristu. Kukhala mu mpingo wa Chibaptisti kapena Chimethodisti sikumakupangani inu Mkhristu.

66 Pali njira imodzi yokha yokhalira Mkhristu. Mawu oti *Mkhristu* amatanthauza "Wonga-khristu." Ndipo inu simungakhoze kuchita izo, inu simungakhoze kuzichita izo mwa

inu nokha, palibiretu njira nkomwe yomwe inu mungachitire izo. Inu muyenera kudziiwala nokha, kufa kwa inueni, ndi kumulola Khristu kuti alowemo ndi kumakhala moyo wa Khristu mkati mwanu.

67 "Kupatula munthu. . ." Apa pali chimene Yesu ananena, "Kupatula ngati munthu abadwa mwa Mzimu ndi mwa madzi, iye sadzalowa mwanjira iliyonse mu Ufumuwo." Kaya iye ndi wa Chikatolika, Chimethodisti, Chibaptisti, kaya nchiani, inu mudzayenera kuti mubatizidwe mmadzi ku kuchotsa kwa machimo anu ndi kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera, kapena inu mwataika. Awo ndi Mawu a Yesu mwini. Chotero tsopano ngati inu muli wa Chimethodisti, ndipo munalandira ubatizo wa Mzimu Woyera, munabatizidwa mmadzi, Yesu anati inu mudzalowa Kumwamba. Ngati muli wa Chikatolika ndipo mwachita chinthu chomwecho, inu mudzakalowa Kumwamba.

68 Koma ngati inu mwangogwiritsa ku kachikhulupiriro ako ka mpingo wa Katolika, kapena Methodisti, kapena mpingo wa Baptisti, inu mukanali wotaikabe. Ndipo ndi chifukwa chake ife tafika mu chikhalidwechi mu dziko, chomwe tiri nacho lero, pakuti anthu ali ndendende basi. . .Iwo amati, "Izo ndi zotsutsana ndi chikhulupiriro changa."

69 "Kodi inu mumakhulupirira mu machiritso Auzimu?"

70 "Izo ndi zotsutsana ndi chikhulupiriro changa." Izo ndi zotsutsana ndi mpingo wako; kachikhulupiriro ka mpingo wako kanakapanga iko, mwaona, inu mumayenera kuti muzichita zomwe mpingo wanu umanena. Ndiyeno inu mumafuulira pa Achikatolika; icho ndi chinthu chomwe chomwecho chimene iwo amachita. Ndipo icho ndi chirombo ndi fano la chirombo! Ndipo Baibulo limati, "Aliyense amene angatenge icho sangakhoze kulowa mu Ufumu wa Kumwamba, koma adzaponyedwera kunja kumene agaru ndi anyanga, ndi ena otero, ndipo azikadzunzidwa ndi moto ndi miyala yamoto, mu kukhalapo kwa Angelo oyera ndi Mwanawankhosa, kwanthawi za nthawi." Tuluka mu izo, mzanga! Konza zinthu ndi Mulungu! Inde, bwana.

71 Ndipo tsopano ndiloleni ine nditenge ili. Chabwino, ife tizichotse izo panjira. Tsopano, winawake anandifunsa ine lero; kawiri kapena katatu ine ndakhala ndikufunsidwa izi.

27. M'bale Branham, kuyankhula za "chilemba cha chirombo," kodi inu simukukhulupirira kuti iwo azidzadinda nambala mmutu mwako, kapena kudinda chinachake pa dzanja lako? Ayi, bwana! Inu musayembekezere konse zimenezo.

72 Icho chidzakhala kukanizidwa! Ndithudi! "Palibe munthu azidzatha kugula kapena kugulitsa kupatula iye atakhala wa mchitaganya cha mipingo." Izo nzoona. Tsopano, icho chidzadza monga chigwirizano kugwirizanitsa chinthucho, kuchibweretsa icho mpaka pa chipembedzo chogwirizanitsidwa. Gwirani mawu

anga, icho sichiri kutali kwambiri! Inu mudzachiona icho, iye ali cha pa ngodya pomwepa.

73 Chifukwa chimene inu simukuzidziwira zinthu izi, inu nthawizonse mumakhala muli kwanu kuno. Mudzanditsatire ine uko mu maiko awa kumene Chikatolika chiri ndi ulamuliro, nthawi imodzi, ndi kudzawona zomwe zimachitika. M'bale, iwo amawauza iwo onsewo choti azichita ndi choti asamachite.

74 Ndipo apa Baibulo likunena kuti United States, ife tinazitenga izo mu uneneri, anadza apo ngati *mwanawankhosa*, "ufulu wa chipembedzo," ndipo molunjika iwo anazilumikiza zinthu zimenezo palimodzi, ndipo iye anayankhula ngati chinjoka ndi kumachita ndi mphamvu yomweyo imene chinjoka chinali nayo asanadze iye. Ameneyo ndi U.S.A.! Uko nkulondola.

75 Mtumiki ananena kwa ine osati kale litali, bwenzi la ine, anati, "M'bale Branham, Mulungu sadzamulola konse United States kuti agwe, chifukwa cha maziko a makolo ake oyambirira, okhazikitsidwa pa chipembedzo."

76 Ine ndinati, "Iye anawalola Ayuda; zedi kuti atengedwere kutali, ndipo iwo anali nako kuima kwabwinoko kuposa komwe ife tiri nako." Uko nkulondola. Mulungu si wolemekeza kam'badwo kenakake kamene kanapita; inu kapena muziyenda mu mzerewo kapena inu muli kunja kwa Ufumuwo, ndizo zonse. Zoonadi! Izo nzokakala ndithu, koma izo nzabwino kwa inu. Uko nkulondola. Ilo ndi Lemba. Ndipo ife tiyenera, ife . . .

77 Vuto lake ndiro, lero . . . Ena a inu anthawi-zakalenu mukudziwa izi. Ife tiri ndi ulaliki wa Hollywood wochuluka kwambiri. Uko nkulondola. Zochuluka kwambiri za izo ndi phokoso lochuluka kwambiri ndi kupitiriza, zochuluka zokongoletsa ndi chirichonse monga choncho, ndi kuliza malipenga, ndi zina zotero; ndipo, "Ndani ati aimirire ndi kumulola Khristu ngati Mpulumutsi wake? Mulungu akudalitse iwe, m'bale, iwe upita Kumwamba pakali pano." Ilo ndi bodza! Ilo ndi bodza!

78 "Kupatula munthu akhale atabadwa kachiwiri!" Ndipo ngati iye akhala atabadwa kachiwiri, Mdalitso womwewo umene unabwera kwa iyeyo uko ubwera kwa iyeyu kuno. Ndipo ife tadutsa mu izo, mobwereza bwereza, ndi kudutsa mu Malemba sabata lathali. Ndipo tinapeza kuti kwa anthu Akummawa, pamene Mzimu Woyera unagwera pa Ayuda, amene anali akummawa kalelo, anthu a Kummawa, Mzimu Woyera unagwa ndi zizindikiro zazikulu ndi mawonetseredwe. Baibulo linati pakadadzakhala pafupifupi a—nthawi pamene sakanati ngakhale kuitcha, ngati mdima kapena usana. Ilo likanakhala monga tsiku lamitambo, kubwerapo mpaka kugawo lotsiriza la usiku. Ndiyeno dzuwa likadadzatuluka mphindi zochepa potsiriza, madzulo. "Kudzakhala kuli Kuwala mu nthawi ya

madzulo." Kodi uko nkulondola? Chabwino, awo ndi anthu Akumadzulo, Amitundu, akulandira Mzimu Woyera womwewo umene Ayuda anaulandira mmbuyomo uko, ndi zizindikiro zomwezo ndi mawonetseredwe. Ndi zimenezotu.

79 Ndipo, ndithudi, anthunu, dziko lidzikutchani inu "otengeka, ozelezeka mmutu." Baibulo, Yesu anati iwo akadamadzachita izo. Ndinu anthu achilendo, ndipo ndinu osamvetsetseka chifukwa Iwo ndi wosiyana kwambiri zedi.

80 Ine ndimaziwona izo mwa oyandikana nawo anga omwe kwathuko, anthuwo kumeneko. Iwo, ngakhale ana anga ang'ono; ife timayesera kuwasunga iwo mwaukhondo ndi kumakhala molongosoka momwe zingathekere, koma inu mukhoza kuwona oyandikana nawo akupangitsa kusiyana pa ana. Mukuona? Iwo amapangitsa kusiyana.

81 Ndipo ine ndikudziwa, ine ndiri nayo njira yodziwira zinthu (ndipo inu mukudziwa izo, inu mwaziwonapo izo mu msonkhano), ndimadziwa kuti abusa amu mzindawu amati, "Chabwino, tsopano, Billy ndi mnyamata wabwino, ife tiribe chotsutsana naye iye. Koma, inu mukuona, ilo ndi gulu lina basi la anthu osiyana ndi chomwe ife tiri." Zithokozani Mulungu! Uko nkulondola. Zithokozani Mulungu! Ndicho Chirembacho. Apo pali Chiremba chimene ife tikuchikambacho.

82 Yang'anani, usiku watha, pamene Mzimu Woyera unaneneratu, zaka naini handiredi Ayuda asanalandire Mzimu Woyera, ndipo unawauza iwo chimene iwo ukadadzakhala uli. "Nyanga yolembera, munthu wokhala ndi cholembera cha nyanga anapita pakati pa Yerusalemu ndipo anakaika chizindikiro mu mphumi zawo." Nkulondola uko? Anayankhula za Iwo mpingo usanaweruzidwe ndi Mulungu. Ndipo Tito anazinga zipupa za Yerusalemu, mu A.D. 96, ndipo anauyatsa mzindawo. Ndipo panalibe mwala umodzi umene unasiidwa pa umzake, molingana ndi uneneriwo. Ndipo, lero, chinthu chokha chomwe iwo ali nacho chinasiyidwa pa kachisiyo ndi chipupa chakale chiri apo pamene iwo anaunjikapo miyala, ndipo icho chakhulukhutizidwa mokongoletsa pamene Ayuda amalirapo ndi kubuma pa chipupa chobumirapocho, chinthu chokha chomwe chatsalira pa kachisi. Ndipo Mzikiti wa Omar ukuimirira pa malo omwewo.

83 Ndipo Yesu anati, "Monga zinayankhulidwa ndi mneneri Daniele; pamene inu mudzawona chonyansa chimene chikupanga chopululutsa chitaima mu malo Woyera," ndiye Iye walemba mzere mmusi, mopatula, "(iye amene awerenga adzazindikire.)" Mukuona? Uko nkulondola. Apo izo zinali. Ndipo Iye ananena kuchuluka kwa tsiku . . . nthawi yomwe iti idzakhale mpaka Amitundu adzakhale ali . . . nyengo kudulizidwa; iwo akanati azidzaponda pa makomawo, kenako Mulungu akanati adzabwerere kwa Ayuda. Ndipo ife tiri pa

nthawi iyo yomwe! Ndi awa pano Ayuda akubwerera uko, mwa zikwi, mu zaka zingapo zapitazi. Ndipo inu mukudziwa momwe ife tinadutsira izo usiku wathawu, momwe Lemba mwangwiro . . . basi ngati kuti ukuwerenga nyuzipepala, ndi momveka bwinonso kwambiri chifukwa inu mukuzimvetsa mochulukirapo mu Izo ndiyeno.

84 Koma, ngakhalebe, Chizindikiro chimene chinaikidwa pa mutu wawo sichinali chodindidwa. Kodi icho chinali? Kodi Icho chinali chiani? Ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo kodi Chilemba chimene chiti chikhale cha tsiku lomaliza ili ndi chiani? Baibulo linati, "Chisindikizo cha Mulungu chinali ubatizo wa Mzimu Woyera, kwa anthu a mtsiku lotsiriza." Tsopano palibepo . . . Aefeso 4:30, "Chotero musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu." Baibulo likuyankhula. Ndipo Aefeso 1:13 amanena chinthu chomwecho, malo ena ambiri, kuti, "Mzimu Woyera ndiwo Chisindikizo cha Mulungu."

85 Kodi chisindikizo ndi chiani? Chisindikizo sichingakhoze kuikidwa pa chinthu chirichonse mpaka icho chitatsirizidwa. Achilutera sanasindikizidwe, tsiku la nyengo ya chisomo linali lisanamalizike; iwo ankalalikira kulungamitsidwa. Amethodisti sanasindikizidwe. Ine ndikubwera ku funsoli apa; ife tifikabe kwa ilo pang'ono—posachedwa pang'ono. Sanali osindikizidwa, chifukwa iyo inali isanatsirizidwe. Koma ubatizo wa Mzimu Woyera ndiwo kutsirizitsa kwa ntchito za Mulungu!

86 Iye anati "Alipo atatu amene amachitira umboni Kumwamba: Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, ndipo atatu awa ndi Mmodzi." Inu simungakhoze kukhala ndi Atate popanda kukhala ndi Mwana, Mwana popanda Mzimu Woyera, iwo ndi Mmodzi.

87 Iye anati, "Alipo atatu amene amachitira umboni pa dziko lapansi: madzi, Magazi, Mzimu, ndipo izo siziri chimodzi koma zimagwirizana mu chimodzi," ndi zimenezotu, "mu kusindikiza kumodzi kwathunthu." Kulungamitsidwa pansi pa Lutera, madzi; kuyeretsedwa mwa Magazi.

88 Kulungamitsidwa kunali Aroma 5:1, "Chotero pokhala titalungamitsidwa ndi chikhulupiriro ife tiri nawo mtendere ndi a . . . Mulungu kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu." Kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro!

89 Kuyeretsedwa kudzera Mmagazi, Ahebri 13:12 ndi 13, "Yesu anavutika kunja kwa chipata kuti Iye akakhoze kuwayeretsa anthu kudzera mMagazi Ake Omwe."

90 Luka 24:49, "Taonani, ine nditumiza lonjezo la Atate Anga pa inu, koma kadikirireni inu mu mzinda wa Yerusalemu mpaka inu mutadzazidwa ndi Mphamvu yochokera Kumwamba." Machitidwe 1:8, "Zitatha kuti Mzimu Woyera wafika pa inu, ndiye inu mudzakhala mboni za Ine mu Yerusalemu,

Yudeya, Samaria, ndi ku magawo akutali a dziko lapansi." Ubatizo wa Mzimu Woyera unali woti udzikhalapo mpaka Yesu adzabwere kachiwiri! "Kanthawi pang'ono ndipo dziko silindiwonanso Ine, komabe inu muzindiwona Ine pakuti Ine ndizikhala ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka ku mathero a dziko; kumachita zi—zinthu zimene Ine ndimazichita, inu mudzazichita nanunso." Kupyolera mu Mzimu Wake ukugwira ntchito kudzera mu Mpingo! Iye anati, "Inu muzidzasekedwa." Anati, "Iwo ananditcha Ine, Bwana wa panyumba, '*Belezebule*, "mfumu ya ambwebwe,"' anati, "ndi mochuluka bwanji momwe ati adzawatchere iwo a mnyumba Yake tsopano?" Amati, "Odala muli inu pamene munthu azidzanena mtundu uliwonse wa zinthu zokhudza inu, sangalalani ndi kukondwera kwakukulu, chifukwa yaikulu ndi mphotho yanu Kumwamba; pakuti chomwecho iwo anawazunza aneneri amene analipo musanakhalepo inu."

91 Ilo ndilo Lemba, mwaona. Ndi Izo apo. Chotero, inu mukuona, inu mukungoyenera kuti mukhale nawo Iwo, mzanga. Tsopano inu mukuyenera kuti mupange kusankha kwanu; ndinu wodzisankhira nokha.

92 Koma icho ndi chilumikizano chake ndi mpingo wa Chiprotestanti ndi mpingo wa Katolika. Palimodzi iwo ali onse, molingana ndi Baibulo . . . omwe amangogwira kwa mpingo; osati Yesu, tsopano, kwa mpingo. Anthu mu mpingo omwe akugwira kwa Yesu Khristu ndi kumapemphera kuti Mulungu atsegule njira ndi kuwapangitsa iwo . . . kuwapatsa iwo Kuwala, munthu ameneyo ndi wopulumutsidwa, ine sindikusamala mpingo wanji womwe iye alimo. Uko nkulondola. Koma ngati iye akungogwiritsa ku chipembedzo chake, iye watenga chilemba cha chinyengo, chimene chiri kutenga malo a ubatizo wa Mzimu Woyera. Zosiyana! Ndipo Katolika ndi Protestanti, onsewo ali ofanana, Baibulo linati, "Iye anali hule; iwo anali timahule, ana ake aakazi." Kodi izo zikumveka tsopano? Chabwino.

28. Kotero Woyera . . . Kodi Mzimu Woyera ukumaperekedwabe pa kusanjika kwa manja? Ophunzira ankachita izi, Petro, Paulo, ndi ena otero, ndipo kodi izo zikadali zothekabe? Paulo Anaulandira Iwo mwa kachitidwe aka.

93 Inde, m'bale wokondedwa, mlongo, yense yemwe analemba pe—pepalali. Mzimu Woyera mwamtheradi ndi woti uzilandiridwa mwa kusanjika kwa manja.

94 Tsopano, anthu ambiri amanditcha ine . . . momwe ine ndakhala ndikutengedwera ngati wa Chipentekoste, kumanena kuti ine ndinali wa chipentekoste. Ine sindinakhalepo konse wa mu bungwe la Chipentekoste. Ndine mwamtheradi mfulu ku mabungwe onse, ndipo mwathandizo la Mulungu ine ndikulinga kukhala mwanjira imeneyo, chifukwa ine ndikhoza kuima

pakati pomwe nkuti, "Ndife abale! Bwerani kuno, tiyeni tibwere tidzalingalire palimodzi."

95 Pamene ine ndinayamba koyambirira mmbuyomo uko, mwa chisomo cha Mulungu . . . Ndipo anthu inu kuno, ndi alembi anga ndi enawo ali panowa akudziwa, ine ndikanakhoza kukhala ndikukumana ndi anthu mamilioni khumi, kapena kuchulukirapo, mu dziko lero. Bungwe lake lomwe likanakhoza kuyambitsidwalo! Mukuona? Uko nkulondola. Koma ine sindikufuna bungwe ayi, izo ndi zotsutsana ndi Baibulo. Ine ndikuyesetsa mwakukhoza kwanga kuti ndiwatengere anthu poti apulumutsidwe omwe ali mu bungwewo. Ndicho chinthucho. Ndipo kukopa kumene Ambuye andipatsa ine ndi anthu, ine ndithudi ndizikugwiritsa ntchito iko kwa ulemelero Wake mmalo mokuika iko pa bungwe linalake. Ine ndikuika iko pa Yesu Khristu pomwe pali pa malo ake. Palibe bungwe lomwe lingakhoze kukupulumutsani inu; izo zimatengera Magazi a Yesu Khristu.

Koma tsopano, mu kusanjika kwa manja, tsopano, ine ndikuti ndisiyane ndi . . .

96 Tsopano, inu anthu okondedwa Achipentekoste, tsopano musati mundinyanyalire ine. Koma tsopano pamene inu mukufika pa malo onena kuti, "Ife tikupita kuti tikadikirire Mzimu Woyera," mawu akewo omwe akhala akugwiritsidwa ntchito mu Chipentekoste!

97 Ndipo ine ndinena ichi mwa chimene . . . osati kukupweteketsani kumverera kwanu. Thandizo lalikulu kwambiri lomwe ine ndiri nalo ku mundako ndi la anthu Achipentekoste, chifukwa iwo amakhulupirira uthenga wa machiritso Auzimu ndi mphamvu ya Mulungu. Ena onse a iwo amakweza mphuno zawo mmwamba kwa Izo.

98 Koma amodziamodzi okha ochokera mu mpingo, omwe anakonzedweratu ku Moyo Wamuyaya, iwo adzabwera. Ndiwo onse. Koma iwo amene sali, sangakhoze kubwera; ndipo Mulungu ananena chomwecho, anati, "Iwo anakonzedweratu ku chitsutso." Iye sali kufuna kuti wina adzawonongeke, koma, pokhala Mulungu, Iye anawona kuti iwo akadadzatsutsa Icho. Kotero ndicho—ndicho zonse, Iye anaziwoneratu izo. Ndipo uko ndi komwe kudziwiratu kwa Mulungu kuli, kuwona pa zinthu zimenezo. Ndipo Iye ananeneratu Mpingo basi pomwe iwo ukanati udzakhale utaima mpaka ku tsiku lomwe lino. Ndipo Mulungu ankazidziwa izo kuchokera kuchiyambi. Asanaikidwe maziko a dziko, Iye ankadziwa kuti mpingo ukadadzakhala basi momwe iwo uliri lero. Iye anadziwa asanaikidwe maziko a dziko kuti ine ndikadadzakhala nditaimirira mu guwa lino usikuuno. Iye ndi Mulungu; Iye amadziwa mapeto kuchokera ku chiyambi.

99 Tsopano, tsopano, anthu Achipentekoste aphunzitsapo . . . Tsopano, ine mwinamwake ndilandira nkhonya zambiri pa

Ichi, koma ine ndiyenera kuti ndikhale woona mtima ngati ine ndikuyenera kuti ndibwere ku Mawu. Palibe chinthu choterocho ngati "msonkhano woyembekezera." Inu mwakhala muli mu cholakwika. Tarry samatanthauza "kupemphera." *Tarry* amatanthauza "kudikira." Kukwera mmwamba kutachitika, Yesu Khristu atatha . . . kupachikidwa, kuyeretsa kwa kachisi. Ndipo litapita tsiku Lachitetezero, chiukitsiro . . . Tsiku Lachitetezero, pamene Iye anaphedwa, ndiyeno ndi masiku makumi anayi mpaka pa kukwera mmwamba, ndipo kenako Pentekoste. Mawu oti *pentekoste* amatanthauza "fifite," iwo amatanthauza masiku fifite chitachitika chopereka cha Chitetezero.

100 Ndiyeno pambuyo pa kuperekedwa kwa Chitetezero, chirichonse chinkayenera kuti chibwerepo mwangwiro, momwe zinalembedwera, mwapamalo, chirichonse ndendende monga momwe Mulungu ananenera. Ndipo Pentekoste, iyo inali nthawi yachisangalalo, pamene iwo ankabweretsa umo zipatso zoyamba za zokolola ndipo ankakhala ndi chisangalalo.

101 Tsopano, zipatso zoyamba za—za Mpingo, Mpingo wa Mzimu Woyera, mpingo umene ukanati ukhalepo zaka zikwi ziwiri izi mpaka Yesu atadza, chipatso choyamba chinabwera pa Pentekoste. Awo anali masiku teni nthawi ya Pentekoste isanafike; awo anali masiku forte kutachitika kuyeretsa, kutachitika kupha kwa nsembe, mpaka pa kukwera mmwamba kwa Yesu Khristu. Iye anati, "Pitani uko ku Yerusalemu ndipo kadikirireni mpaka inu mutavekedwa ndi Mphamvu yochokera Kumwamba." Machitidwe 1 . . .

102 Machitidwe 2, "Ndipo pamene Tsiku la Pentekoste linafika kwathunthu, iwo anali mu chiyanjano chimodzi, mu malo amodzi. Ndipo mwadzidzidzi apo panadza kuchokera Kumwamba phokoso longa mphepo yamphamvu ya nkokomo, inadzaza nyumba yonseyo momwe iwo anali atakhala. Ndipo iwo onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo anayamba kuyankhula ndi malirime ena, momwe Mzimu unkawapatsira iwo mayankhulidwe."

103 Ndiyeno dziko lachipembedzelo, kunjako, mipingo yaikulu ya chiorthodox, inadza apo ndipo inawawona anthu awo akudzandima ndi kumachita ngati anthu oledzera. Ndipo iwo anadza apo ndipo ankawaseka iwo ndipo anali kuwatonza iwo, ankati, "Taonani gulu ili la Agalileya! Iwo onse aledzera!" Mukuona kusamvetsako?

104 Ndipo kwa mzanga wa Katolika, Maria namwali wodalayo anali limodzi nawo. Ndipo ngati Mulungu sakadamulola iye kuti adze Kumwamba popanda kulandira Mzimu Woyera ndi kukhala wonga choncho, kodi inu mukuganiza inu mudzakafika uko ndi chirichonse choperewerapo, mlongo? Ayi. Chotero tiyeni ife titsikepo pa kavalo wathu wapamwambayu, tiyeni titsikepo.

105 Musati mudzitcherera khutu ngakhale ku chimene dziko liri nacho kuti linene. Ziyang'anani pa chimene Mulungu ali nacho kuti anene! Awa ndi Mawu a Mulungu. Ife tiyenera kuti tizimanga izo molingana ndi ndondomeko *imeneyi,* chifukwa Iye anati kwa Petro, "Pa thanthwe ili ine ndidzamangapo Mpingo Wanga ndipo zipata za gehena sizingakhoze kuwugonjetsa Iwo." Chinthu chirichonse chizidzachitika. Izo zikusonyeza kuti zipata za hade zidzakhala zikulimbana nawo Iwo, koma izo sizidzagonjetsa. Ndipo anthu akuganiza kuti iwo angakhoze kuuletsa Iwo? Inu mukhoza kuliimitsa dzuwa mofulumirirapo. Uko nkulondola. Inu simungakhoze kuuletsa Iwo. Mulungu anawudzoza Iwo kuti uzisunthabe chitsogolo

106 Kuno pamene ine ndinatembenuka koyamba, ngakhale amayi anga *osauka* mmbuyo umo ankaganiza kuti ine ndachita misala. Apongozi anga aakazi anati, "Iye akuyenera kuti atumizidwe ku malo a amisala." Alaliki amu mzindawu anati, "Iye azirala posachedwa pomwepa." Ine ndakhala ndikuyaka nthawi yaitali. Iko ndi kuyaka kwauzimu, mwabwinoko nthawi zonse. Bwanji? Iwo sungakhoze kuzirala ayi, Iwo ndi Mulungu! Mmalo mwa kuzirala, Iwo wafalikira kuzungulira mdziko tsopano.

107 Chinthu chomwecho basi chimene Iye ananena pamene ine ndinkabatiza cha kumusi konkuno pa Mtsinje wa Ohio, ambiri a inu munali mutaimirira pamenepo, zaka twente-firii zapitazo, pa Mtsinje wa Ohio pomwepa. Kuwala uko, Mngelo, anadza mpaka pansi kufika pomwe ife tinalipo, ndipo anati, "Monga Yohane M'batizi anatumidwa kudzakhala wotsogolera kudza koyamba kwa Yesu Khristu, Uthenga wako ubweretsa Kudza Kwachiwiri kwa Yesu Khristu." Ndi iwo wazichita izo. Ziri . . . Iye sanabwere panobe, koma taonani chomwe uwo wachita, iwo wafalikira mdziko, kuzungulira. Mukuona? Ndipo lero tsopano, tangoganizani, ndipo ku—kulimbikira kumene kwapitapo, kwakhala kwenikweni mamilioni.

108 Ngakhale *Sunday Visitor* ya Katolika inayankhula za izo, za mamilioni angati amene adzamo mozungulira, kulimbikira kokhako.

109 Ena amamva, iwo amati, "Icho ndi Choonadi! Ine ndiri wokonzeka kudzigulitsiratu tsopano, pa zinthu izi za mdziko, ndi kupita kumakalalikira Uthenga weniweni."

110 Ndipo icho ndi chifukwa chake iwo amatitcha ife "a Uthenga wamphumphu," iwo amautonza Uthenga wamphumphu. Koma, m'bale, ine sindikufuna theka la chinthu china, ine . . . chiyenera chikhale chiri chinthu chonsecho, kwa ine. Ngati gawo la icho chiri chabwino, chotsalira chonse cha Icho ndi chabwino. Uthenga wamphumphu!

111 Tsopano, zindikirani, Mzimu Woyera unabwereranso uko. Anthu a achipentekoste anadikirira, "Ndipo apo mwadzidzidzi

linabwera phokoso lochokera Kumwamba monga mphepo yamphamvu ya mkokomo, inadzaza mnyumbayo momwe iwo anali atakhala."

112 Palibe nthawi imodzi yomwe iwo ankayenera kuchita kudikira pambuyo pa apo. Pamene Petro anali akuyankhula Mawu awa kwa Amitundu, Mzimu Woyera unagwera pa iwo, ngakhale iwo asanabatizidwe nkomwe. Nkulondola uko? Akadali, Machitidwe 10:49 . . .

> Koma *pamene Petro anali kuyankhula mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa . . . iwo amene ankamva mawuwo.*
>
> *Ndipo iwo akumdulidwe . . . ochuluka omwe anabwera ndi* Petro anadabwa, *chifukwa . . . pa Amitundu . . . panatsanuliridwa mphatso ya Mzimu Woyera.*
>
> *Pakuti iwo anawamva iwo akuyankhula ndi malirime, ndi kumukuza Mulungu. Ndiye anati Petro,*
>
> *Kodi munthu angaletse madzi,* poona kuti *awanso* ayenera . . . *alandira Mzimu Woyera* momwe ife tinachitira pachiyambi?
>
> *Ndipo iye* anayembekezera ndipo anab- . . . *anawalamulira iwo kuti abatizidwe mu dzina la* Yesu Khristu! . . .

113 Uko nkulondola; popanda kudikirira, popanda kuyembekezera. Njira ya utumwi, Mulungu analibe lamulo loikidwa; pamene mtima uli wanjala, Iye akupatsani inu chimene inu mukuchimvera njalacho. Ngati inu mukuufuna Mzimu Woyera, Iwo ukhoza kugwera pa inu pakali pano.

114 Petro, pamene iye anapita kwina kukalalikira, Petro anali nawo mafungulo aku Ufumu. Ine ndiri ndi funso kuti ndifike ku zimenezo mu maminiti ochepa. Iye anali nawo mafungulo ku Ufumu. Iye anawatsegulira Iwo ku nyumba ya Korneliyo. Iye anawatsegulira Iwo, kuja kwa Asamaria, iye anawatsegulira Iwo cha kuno; koma kumbukirani kuti Filipo anali atapita uko ndi kukalalika kwa iwo ndi kuwabatiza iwo mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo Petro anabwera uko ndipo anadzaika manja pa iwo. Ndipo, tsopano, iye anachita chinachake, kwa wanyanga uja kumene kuja . . . Iwo anali ndi Simoni wanyanga, anati, "Ine ndikupatsani inu ndalama zina, kuti inu mundipatse ine Mphatso imeneyo, kuti pa yense yemwe ine ndiziika manja anga azilandira Mzimu Woyera." Ndi kulondola uko? Chinachake chinachitika! (Osati ena a ma aliki-bishopu awa okhala ndi kolala yawo yotembenuzira kumbuyo, kudza cha pamenepo ndi kuika manja pa iwo, kuti, "Ine ndikupatsani inu dalitso la utumwi.") Chinachake chinachitika pamene Petro anaika manja ake pa iwo; ndi pamene iwo akuzichita panobe.

115 Ine ndawaonapo iwo akungogwa ngati ntchentche monga choncho, pamene Mzimu Woyera umawakantha iwo, mwa kuika kwa manja. Inde, icho ndicho chi—chiphunzitso chautumwi cha kuika kwa manja. Mulungu akudalitseni inu. Ngati inu muli wosiyanako pang'ono ndi zimenezo, mungondilembera ine kapepala mawa usiku. Chabwino.

29. Ngati magawo awiri pa atatu a anthu a mdziko anamva . . . sanamvepo Uthenga panobe, Mawu a Uthenga, ndi ochuluka bwanji omwe a . . .

Ndikupempha chikhululukiro chanu. Ilo lalembedwa ndi inki, ndipo ine ndakhala ndikuchita thukuta pano ndipo ilo layenderera pa ilo. Tiyeni tiwone.

Ngati magawo awiri pa atatu a anthu a mdziko sanamve Uthenga panobe, angathe bwanji Ambuye wathu kubwera tsopano, pokhala kuti iwo sanamve Uthenga, magawo awiri pa atatu a iwo?

Chabwino, izo ndi ndendende kulondola. Ine ndikuuzani inu zomwe ine ndikuganiza.

116 Kuno osati kale kwambiri, pamene Dokotala Reidhead, Purezidenti wa Mishoni ya ku Sudani, wamkulukulu wa mphumphu . . . wamkulukulu wa utumwi . . . Ayi, ine ndikupempha chikhululukiro chanu. Mishoni yaikulu kwambiri ya chikhazikitso mdziko, mishoni ya ku Sudani. Dokotala Reidhead, ali ndi madigirii ochuluka kwambiri mpaka iye sanali kudziwa ngakhale madigirii angati omwe anali pa iye, anabwera ku nyumba yanga kumtunda uko, kupitirira pang'ono chaka ndi miyezi sikisi yapitayo. Ndipo anaimirira mu nyumba yanga, iyeyo ndi Hyman Appleman uyu, mtumiki wa Baptisti uyu amene walandira Mzimu Woyera tsopano ndipo akumalalikira uko mu Mexico. Ndipo iye anabwera ku nyumba. Iye anati, "M'bale Branham," anati, "kodi inu mumachita ndi Achipentekoste?"

Ndipo ine ndinati, "Inde, bwana."

Ndipo iye anati, "Ine ndine Dokotala Reidhead."

Ine ndinati, "Ndine wokondwa kukudziwani inu. Inu mungalowe mkatimu?"

Iye anati, "Inde, bwana."

117 Iye anakhala pansi, anati, "Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake." Anati, "Ine ndamva kuti inu munadzozedwa mu mpingo wa Baptisti."

118 Ine ndinati, "Uko nkulondola." Ine ndinati, "Ndi komwe ine ndinatulukako," Ine ndinati, "chifukwa ine sindikadakhoza kupirira nazo izo. Ine—ine ndimakhulupirira kulalikira chimene Baibulo limanena, osati chimene mpingo wa Baptisti umanena. Ndipo ine ndiribe chinthu chotsutsa mpingo wa Baptisti, iwo ali chimodzimodzi basi monga mpingo wina uliwonse." Ndipo

ine ndinati, “Ine ndinatuluka mwa iwo kuti ine ndidzakhoze kukhala mfulu.”

Iye anati, “Chabwino, ndithudi, inu mukudziwa ife ndife a Baptisti.”

Ndipo ine ndinati, “Inde, bwana.”

119 Ndipo iye anati, “Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake. Nanga bwanji za ubatizo wa Mzimu Woyera uwu?” Anati, “Ine ndakhalapo mmenemo ndi kuwaonamo iwo akumenya ndi kugubuduza mipando ndi kumapondetsa mapazi ndi kufuula ndi kupitiriza zochita.”

120 Ine ndinati, “Ine ndaziwonapo zonse izo, nanenso.” Koma ine ndinati, “M’bale, kuseri kwa izo zonse, kuli nkhani yeniyeni yoona ya ubatizo wa Mzimu Woyera.”

121 Ndipo iye anati, “M’bale Branham, kodi ine ndingakhoze kuulandira Iwo?” Iye anati, “Ine ndiri ndi maulemu ochuluka kwambiri!” Iye anati, “Ine ndine Dokotala, ndine *ichi*, ine ndiri nayo Ph.D. yanga, ine ndiri nayo Digirii ya Ubatchala yanga, ine ndiri nawo mtundu uliwonse wa digirii ndi madigirii aulemu kuchokera konsekonse ku maiko onse, ndi zinthu zonga izo,” anati, “ndipo nanga alikuti Yesu Khristu?”

122 Ine ndinati, “Chabwino, m’bale, Iye ali momwe muno mu chipindachi.”

123 Iye anati, “Ine ndinaimirira ndipo ndinayankhula ndi wa Chimuhamadi weniweni, anali atangophunzitsidwa kumene mu Amereka, ndipo ine ndinati, ‘Mukane mneneri wako wakale wakufayo ndi kulandira Ambuye Yesu woukitsidwayo.’ Iye anati, ‘Bwana wachifundo, ndi chiyani chimene Ambuye Yesu wanu woukitsidwayo angandichitire ine mochulukirapo kuposa chimene Muhamadi wanga angakhoze kuchita?’ Anati, ‘Awiri onsewo analemba Mabaibulo, ife timakhulupirira izo.’ Anati, ‘Awiri onsewo anafa.’ Ndipo anati, ‘Ndipo awiri onsewo analonjeza moyo pambuyo pa imfa, kwa ife, ndipo ife timazikhulupirira izo.’”

124 Iye anati, “‘O, koma, inu mukuona,’” anati, “‘ife Akhristu tiri ndi chimwemwe.’”

125 “Anati, ‘Chomwechonso ife.’ Anati, ‘Ine ndikhoza kuwonetsera kuwerenga maganizo kochuluka basi monga momwe inu mungathere.’” Ndipo uko nkulondola. “Iye anati, ‘Chabwino, tapenyani, Muhamadi wathu. . . Inu mumati Ambuye Yesu wanu anauka kwa akufa.’”

126 Ndipo Dokotala Reidhead anati, “‘Bwanji, Iye anaterodi!’”

127 “Anati, ‘Tsimikizirani izo!’ Anati, ‘Tsimikizirani izo!’ Anati, ‘Inu mwakhala nazo zaka zikwi ziwiri zoti mutsimikizire izo, ndipo pafupi gawo limodzi lokha pa atatu a mdziko ndi omwe anamvapo konse za izo.’ Anati, ‘Siyani Muhamadi wathu auke kwa akufa ndipo dziko lonse lidziwa za izo mu

masiku awiri.'" Iye akulondola. "Iye anati, 'Muhamadi wathu sanatilonjeze konse ife kalikonse koma moyo pambuyo pa imfa.' Iye anati, 'Ambuye Yesu wanu anakulonjezani inu, ndi inu aphunzitsi, kuti zinthu zomwezo zimene Iye ankazichita inu muzidzazichita inunso.' Ndipo anati, 'Tiyeni tikuwoneni inu aphunzitsi mukuchitanso izo tsopano, ndipo,' anati, 'ife tikhulupirira kuti Iye anauka kwa akufa.'"

128 Iye anati, "M'bale Branham, ine ndinapondetsa phazi langa mu dothi monga *choncho* ndipo ndinaisintha nkhaniyo." Ndiri nawo madigirii onse awo! Bwanji? Mulungu alikuti mu madigirii amenewo? Mulungu samadziwidwa ndi ma Ph.D., ndi ma D.D., ndi ma L.D., ndi zina zotero.

129 Mulungu amadziwidwa ndi chikhulupiriro chophweka, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndiyo njira yokhayo. Mulungu mkati mwanu, mpaka Iye abalepo inu "mwana wa Mulungu," asinthe chikhalidwe chanu. Ndipo chinthu icho chomwe, Mulungu Mlengi Yemwe anapanga zinthu zonse ndipo anayankhula kuti dziko likhalepo mwa Mawu Ake, Mzimu womwewo mkati mwanu, inu mukukhulupirira chirichonse chimene Mulungu ananena. Ndipo palibe chinthu chosatheka; inu mukuzikhulupirira Izo.

130 Inu simumaima kumbuyo kwa kachiphunzitso kamodzi kakang'ono nkumati, "Ine sindikukhulupirira, kulandira Izo. Ine sindingakhoze kukhulupirira Mulungu angachite *izi*. Ine sindingakhoze kukhulupirira." Inu mumampatsa malire Mulungu ndi kusakhulupirira kwanu komwe! Nzomwe ziri.

131 Chotero Dokotala Reidhead anaimirira pamenepo, iye anati, "M'bale Branham, kodi munthu angakhoze kuulandira, Mzimu Woyera, weniweni?"

132 Ine ndinati, "Inde, bwana, Dokotala Reed-, inu mukhoza."

133 Iye anati, "Ngati Mulungu akuudziwa mtima wanga; ndipo ine ndikukukhulupirirani inu, podziwa; ndipo pansi pa kudzoza pakali pano, ine ndikufuna inu kuti. . . Kodi inu mukukhulupirira kuti ine ndikunena zoona?"

Ine ndinati, "Ine ndikudziwa inu muli!"

Iye anati, "Kodi ine ndiyenera kuulandira Iwo chotani?"

Ine ndinati, "Gwadani."

134 Ndipo iye anagwada pamenepo pambali pa tebulo la khofi lakalelo. Ine ndinangoligula kuchokera pamtunda apo. Bambo ali kumbuyo uko amene analikonza ilo kanthawi kapitako chabe pa mtunda apa. Atakhala pamenepo, anaphwanya galasi la pamwamba pakepo pamene iye ankagwada pansi. Iye anati, "Mulungu, chitirani chifundo pa moyo wanga wochimwa kwambiri." Ndipo ine ndinasanjika manja pa iye, ndipo ubatizo wa Mzimu Woyera unadza pa iye apo pomwe. Uko nkulondola.

135 Ndipo iye wangowuika mpingo wa Baptisti uwo pa moto konsekonse tsopano, kwa onse aiwo cha kumeneko. Ndi zimenezotu apo. Inde, bwana.

136 Uthenga sungakhoze . . . Yesu sangakhoze kubwera mpaka . . .

137 Mvetserani! Ife tagawa matraki konse kuzungulira mdziko. Inu simungakhoze kupita ku ngodya iliyonse yaing'ono kosakhala kuli matraki akugawidwa, winawake kubwera cha uko ndi fioloje. Inu mupite kutsidya la nyanja lero ndi kukadzitcha inueni "amishonare," ndipo kawawoneni iwo akukusekani inu. Kayendeni mu India ndi kumakati, "Ndine mmishonare."

138 "Chabwino, kodi inu muzitiphunzitsa chiani ife?" Iwo amadziwa zochuluka za Baibulo ndiye . . . Ena a ana awo kumeneko amadziwa zochulukirapo za ilo kuposera ena a aphunzitsi awowo muno mu Amereka amalidziwira. Kuwonjezera apo, ili ndi Bukhu la Kummawa. Ndipo, kumbukirani, iwo anali nawo Uthenga mazana ndi mazana ndi mazana a zaka Amereka asanafike nkomwe pokhalapo. Tomasi Woyera, mpingo waukulu umene iye ankalalikiramo, uli chiimirebe lero mu India. Iwo sakusowa kuphunzitsa kwanu kulikonse, iwo amadziwa zonse za izo. Iwo anati, "Kodi iwe utiphunzitsa chiani ife?"

"Chabwino, ife ndife amishonare Achimereka."

139 "Kodi iwe uphunzitsa chiani kwa ife, momwe tingamamwere kachasu? Izo ndi zomwe inu nonse mumachita kuno mu mipingo mwanu! Kusuta ndudu? Mukuti mutiphunzitse ife momwe tingawasudzulire akazi athu, ndi zina zotero?" Anati, "Ngati inu muti muchite izo, ife sitikuzifuna izo." Ndipo anati, "Inu mukabwera mpaka kuno ndi fioloje ina yatsopano kapena chinthu chimzake china inu mukati muyesere kutiphunzitsa ife zina za Mawu, ife timawadziwa iwo mochuluka kuposa momwe inu mumachitira." Ndipo uko nkulondola. Iye anati, "Koma ngati inu mukubwera kudzawonetsera chimene Mawu amanena, ife tizilandira Izo." Ameni! Ndi zimenezotu. Icho ndicho chinthu chomwe iwo akumvera njala.

140 Gwirani Mawu anga, alembeni Iwo mu masamba a Baibulo lanu, pakuti Iwo ndi a PAKUTI ATERO AMBUYE, "Kumbukirani, pamene ife tikatera mu India, inu mukamva za makumi a zikwi kuchulukitsa ka zikwi za kukhala atapulumutsidwa." Mzimu Woyera wazinena Izo. Ine ndazilemba Izo pano mu Baibulo langa. Izo zalembedwa mu makumi a zikwi za ma Baibulo komwe kuno, monga chiukitso cha mnyamata wamng'ono, mwa masomphenya omwe Iye anati. "Muli zikwi mazana atatu a iwo mmenemo." Ndipo inu mukawona ngati izo si zoona! Umo ndi momwe Uthenga uti ukalalikidwe mwa usiku

wokha. Iwo ukangosesa monga choncho, kuchokera pamalo kupita kumalo.

141 Mu Afrika, kumene zikwi makumi atatu awo pa kuitanira ku guwa kumodzi kokha analandira Mulungu, ine ndinati, "Kwezani manja anu ndi kulandira Mzimu Woyera." Ine ndinati, "Musati muyembekezere mmishonare wina wa Chimereka kuti abwere kuno ndi kudzakuphunzitsani inu zinenero mmipingo umo." Ndi amayi ochapa pa matabwa, kuti atumize mmishonare kumeneko ndi kumadzakwera uku ndi uko galimoto yabwino yaikulu, kumakhala moyo ndi zonona za mdzikolo; zedi, kugawa timathiraki tingapo ndi kubwererako. Iwo samafuna zimenezo; ndinatsimikizira izo.

142 Ine ndinanena komwe kuno ku Chipatala cha Chiyuda uko, mausiku angapo apitawo mu msonkhano ndi atumiki ndi madokotala, pa phunziro la machiritso Auzimu; ine ndinati, "Inu mwanditcha ine woyera wodzigudubuza, ndipo inu munanena kuti ine ndinali ndi maloto oyipa pamene ine ndinakuuzani inu. . . Mngelo wa Ambuye." Ndipo ine ndinati, "Ndipo mpingo wathu womwe watumiza zikwi ndipo waononga mamilioni a madola, pa kutumizira mamishonare ku Afrika; ndipo pamene ine ndinafika uko, iwo anali akunyamula timafano tadothi tating'ono, kumayesera kuti azipeza thandizo kuchokera ku fano ladothilo, ndi kumadzitcha okha 'Akhristu.'" Ndipo ine ndinati, "Ndipo chimene inu mukuchitcha 'zotengeka' chinapindulira miyoyo yochulukirapo kwa Khristu mu maminiti faivi za nthawi kusiyana ndi mamilioni athu a madola ndi zomwe zikwi za mamishonare achita mu zaka handiredi fifite zapitazi." Iwo anatseka pakamwa, izo zinali choncho! Ndi izo ziri apozo. Ine ndinanena kwa inu, amuna awo, ine ndinati, "Mu—musati inu muziyesera kukhala ophunzira, ingotengani Uthenga uwu ndi kupitirira kupita uko mu—mu dziko obadwirakowo kumene mzungu sangakhoze kupitako nkomwe, kuwopa matenda."

143 Ndipo ine ndiri nazo zolembedwa, kuchokera mu pepala ya ku Durban yomwe, iyo inati, "Ngakhale mwamuna wokalamba mmodzi yekha wosakhoza ngakhale kudziwa lomwe liri dzanja lamanja ndi lamanzere, analandira ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo anali kubatiza mosaperewera chikwi pa sabata." Umo ndi momwe Uthenga uti uzipitira, mu kanthawi pang'ono chabe, Iwo ukungosowa pafupi miyezi isanu ndi umodzi kuti ukwanire padziko ponse. Chabwino.

30. Kodi inu mungafotokoze za Christian—Christian Science?

144 Chabwino. Ine. . . Pano pali. . . ine sindiyankhula za chipembedzo chanu, m'bale wanga kapena mlongo, yense yemwe waika funsoli. Christian Science ndi kuwerenga maganizo. (Ndipo machiritso Auzimu ndi mphamvu ya Mulungu!) Christian science imaika malingaliro pa zinthu; Christian Science imawakana Magazi a Yesu Khristu. Christian

Science . . . O, ine ndiri nawo mabuku a Akazi a Edd uko, ndipo ndinawawerenga onse a iwo. Mukuona? Uko nkulondola, Christian Science imaukana Umulungu wa Yesu Khristu, ndipo imamuika Iye ngati "mneneri." Yesu Khristu sanali munthu; Iye anali Mulungu! Iye anali Waumulungu! Ndipo iwo amaganiza kuti ndi malingaliro pa chinthu.

145 Ngati ine ndiri ndi kuwawa mu dzanja langa kapena mmimba mwanga, kapena . . . kapena kupweteka mmutu mwanga, ine ndiri ndi kudziwa kokwanira kuti ndidziwe kuti iwo ukupweteka, ndipo izo siziri ngati ine ndikuganiza kuti iwo ukupweteka. Koma ine ndikudziwa kuti mphamvu ya Mulungu ingakhoze kukuchotsapo iko, osati ku . . . ine poganiza za iko. Mukuona? Chotero, Christian science, ine ndinganene kuti limodzi ndi lina lomwe linafunsidwa kwa ine, ndi kamodzi ka maganizo amakono, ndipo ndi kulakwitsa kwakuya, mwakuda. Uko nkulondola. Osati kukupweteka kumverera kwako, mzanga, yense amene analilemba ilo, koma ine ndiyenera kukhala woonamtima. Chifukwa inu amene munalilemba ilo, ndi ine, palimodzi, tidzaima tsiku lina mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu kuti tidzalongosole, ndipo ine ndidzayenera kuti ndidzayankhire pa chimene ine ndikunena. Tsopano, ine sindikadati ndiyankhe kupatula ine ndikanamadziwa. Chabwino.

31. Tsopano**: Pamene ife ti . . . Pamene ife timakhala kutali ndi kuno kuti tingamasonkhane nawo . . . Ife timakhala kutali kwambiri ndi kuno kuti tingamasonkhane ku kachisiyu. Kodi inu mungavomereze kuti ife tidzikasonkhana kuti, tidzikasonkhana limodzi nawo, powona kuti mipingo ikutsatira manthu mpingo, kapena, Chikatolika?**

146 M'bale wanga wokondedwa kapena mlongo, yense yemwe walilemba ili, ine sindingati ndikuuzeni inu tchalitchi choti inu muzikasonkhanako. Koma chimene ine ndikanachita, ndi ichi, m'bale wanga, mlongo, ine . . . Ngati inu mulibe ubatizo wa Mzimu Woyera, mwaona, chabwino, inu mulandire ubatizo wa Mzimu Woyera ndiyeno inu muzipita ku gulu lina kumene kuli anthu ena amene ali nawo ubatizo wa Mzimu Woyera. Inu muyenera . . . muzikasonkhana nawo anthu a mtundu umenewo!

147 Ine ndinaona mwamuna, kuno osati kale kwambiri, amene anabadwa zaka khumi chiyambireni iye . . . kapena, osati kubadwa, ine ndikupempha chikhululukiro chanu, zinali zaka khumi kuchokera pamene iye anawona chochipenya chirichonse. Iye anali wa mu mpingo waukulu, ndipo iye ankakhala mu Kennett, Missouri. Ndipo iye analin . . . iye anali a—anali wosoka nsapato zaka zapitazo, ndipo anachita khungu. Ndipo mwamunayo anabwera pa nsanja, ndipo Mzimu Woyera unamuuza iye yemwe iye anali ndi chimene chinali cholakwika ndi iye, unamuuza iye za utali umene iye anali wakhungu, ndipo unamuuza iye za zochita zina zazing'ono, zonyansa zimene iye

anali atazichita. Iye anati, "Ngati Mulungu andilora ine kukhala kuti ndikafike uko, ine ndikachikonza icho." Ndipo, pamene iye ananena izo, maso ake anatseguka; ndipo mu Baibulo lomweli, iye anawerenga mutu pambuyo pa mutu kuchokera mu Ilo.

148 Iye anabwerera ku tchalitchi chake ndipo anali akupereka matamando. Ndipo abusa anamuuza iye, "Izo zikanadzachitika mulimonsebe. Bwanji, iwe unangopangitsidwa kutengeka nazo, kunalibe kanthu kwa izo. Kunalibe kanthu kwa zimenezo, ndi za mdierekezi!"

149 Ine ndikutsutsa aliyense kuti andisonyeze ine Lemba limodzi pamene mdierekezi angakhoze kuchiza. Ngati inu mudzandisonyeze ine pamene mdierekezi angakhoze kuchiza, ine ndikutsimikizirani kuti mdierekezi ndi atate wanu; uko nkulondola, ngati inu mungachite izo. Izo siziri mu Mawu a Mulungu. Izo sizingakhoze kutsimikiziridwa. Ndipo inu mukhoza . . . inu mukhoza kufuna kuti muyesere izo, inu muli olandiridwa. Koma izo zakumanidwa ndi mabishopu ndi china chirichonse, m'bale, chotero musati munene izo.

150 Penyani! Ndipo bambo yemweyo anafika, mu mtima mwake pokhulupirira izo. Ndipo miyezi itatu kenako iye anali mu misonkhano yanga, wakhungu basi momwe iye analiri mmalo oyamba aja. Ndi zimenezotu.

151 Chotero khalani kunja kwa timalingaliro ito! Zisonkhanani naye winawake yemwe amakhulupirira, mudziyanjana nawo. Baibulo linati, "Musadzimange goli pakati pa osakhulupirira." "Khalani inu olekanitsidwa," atero Mulungu. Tulukani umo! Baibulo linati, "Tulukani kuchokera pakati pawo, ndi kukhala . . . musamakhudze zinthu zosayera zawo, ndipo Ine ndidzakulandirani inu. Ine ndine Ambuye Amene amaima mkati mwa mpingo." Uko nkulondola. Tulukani umo! Musati muziyanjana ndi zoterozo!

152 Koma mulole . . . dzifikitseni nokha pakati pa mpingo winawake, mpingo winawake wabwino. Methodisti, Baptisti, Presbateria, Campbellite, uliwonse womwe iwo ungakhale uli, izo sizimapanga . . . Kumene okhulupirira owona enieni ali mmenemo, omwe samasamala chimene kachikhulupiriro ka mpingo kamanena, iwo amapita kwina kukakomana ndi abale awo ndi alongo ndi kumakampembedza Mulungu, palimodzi. Chabwino.

32. Usiku watha inu munayankhula za "unyinji waukulu umene palibe munthu angakhoze kuwuwerenga, ochokera ku mtundu uliwonse, fuko," amene ali—akutchulidwa mu mutu wa 7 wa Chivumbulutso. Kodi ine ndinakumvetsani inu, molondola, kunena kuti "Iwo ndiwo Mkwatibwi wa Khristu"? Inde, inu munandimvetsa ine. Iwo ndiwo Mkwatibwi.

153 Tsopano ngati inu mungazindikire, ndendende basi mu Chivumbulutso 7, iye anawaona handiredi forte foro sauzande. Tsopano, ine sindiri kukuimbani inu mlandu pa ichi, m'bale wanga, koma handiredi . . . Kawirikawiri a Mboni za Yehova ndi omwe amakhulupirira kuti handiredi forte foro sauzande adzakhala ali Mkwatibwi. Ndipo uko nkulakwitsa! Yohane anawadziwa aliyense wa iwo, ndipo anawatchula iwo ndi dzina. Iwo anali aliyense Ayuda. Iye anati, "Thwelofu sauzande a Gadi, thwelofu sauzande a Zabuloni, thwelofu sauzande a Benjamini, thwelofu sauzande a Yuda." Nkulondola uko? Ndipo pali mafuko thwelofu a Israeli, ndipo thwelofu kuchulukitsa ka thwelofu . . . ndi handiredi forte foro sauzande. Nkulondola uko? Iye anati, "Onsewo, ana a Israeli." Yohane anawazindikira iwo.

154 Ndiye iye anayang'ana ku mbali *iyi*, ndipo iye anati, "Bwanji, kuno kwaima unyinji waukulu umene palibe munthu angakhoze kuuwerenga, wa mitundu yonse, zinenero, ndi mafuko; anaima ali ndi miinjiro yoyera, mmanja mwawo . . . ndi makhwatha, ndi kumaikupiza, ndi kufuula, ndi kuimba mahosanna ndi . . . kwa Mfumu." Iye anati, "Ndi ndani amenewo?"

155 Iye anati, "Awo ndi amene atuluka kuchokera mu chisautso chachikulu ndipo atsuka miinjiro yawo mu Mwazi wa Mwanawankhosa. Iwo ali pamaso pa Mulungu, ndipo iwo azitumikira Mwanawankhosa mu Kachisi Wake limodzi ndi Iye. Usana ndi usiku, iwo sadzamusiya Iye." Ndi uyo Mkwatibwi, mwaona, Mkazake, Mkwatibwi wa Amitundu.

156 Kumbukirani, Mkwatibwi ndi wa Amitundu. Iye anati, "Iye adzabwera nadzatenga anthu kuchokera kwa Amitundu kuti akhale Ake" (a chiani?) "a Dzina lake."

157 Tsopano, muli madona aang'ono ambiri mdziko. Koma ine ndinatenga mkazi mmodzi, ndipo ameneyo anali Meda Broy, ndipo iye ndiye Akazi a William Branham tsopano. Iye ali ndi . . . Iye si Broy panonso; iye ndi Branham tsopano. Mukuona?

158 Ndipo umo ndi momwe ziriri, inu mumatengera Yesu Khristu pa inu ndi kukhala Mkwatibwi, ziwalo za Mkwatibwi.

33. Kodi mawu Achilatini ndi chiani amene ali pa Mzinda wa Vatican? Ife tikufuna kuti tidziwe momwe iwo amakwanirira mpaka sikisi handiredi ndi sikisite-sikisi, ndi chomwe iwo amatanthauza.

159 Chabwino, iwo si pa . . . Chilatini—mawu Achilatini sali pa Mzinda wa Vatican; iwo ali pa mpandowachifumu wa papa, pamene iye amakhala pa mpando wake wachifumuwo. Iwo analembedwa pamwamba apo, "VICARIVS FILII DEI." Ngati inu mukufuna kutero, mmawa, ine ndidzazibweretsa izo zitalembedwa, chirichonse, ndi kuziika izo pa chidutswa cha pepala. Ndipo ngati inu mukuzifuna izo, ndiye, ine ndizibweretsa izo kwa inu mmawa. Pamene inu mukhoza

kuziwerenga izo mu zilembo za Chiroma, VICARIVS FILII DEI, mauwo amatanthauza "Mmalo mwa Mwana wa Mulungu"; iye ndiye wolowa mmalo mwa Mwana wa Mulungu.

160 Mpingo wa Katolika umakhulupirira kuti "Petro anali papa woyamba; iye anali wolowammalo mwa Yesu Khristu." Komwe kuli kulakwitsa! Chabwino. Ndiye iwo amanena kuti "Papa aliyense womutsatira iye ndi wolowammalo; ndipo papa tsopano, amene alipo tsopano, ndi wolowammalo mwa Yesu Khristu." Ndipo uko izo zinalembedwa apo, "*Wolowa Mmalo mwa Yesu Khristu,* 'VICARIVS FILII DEI,'" zinalembedwa pamenepo. Tengani zilembo za Chiroma ndipo mungozilemba (X kuimirira teni, V kuimirira faifi, ndi kupitirira motero monga choncho), pamene inu mukuwerenga "VICARIVS FILII DEI," ndi kulemba mzere, ndipo inu mupeza sikisi handiredi sikisite sikisi. Zilembeni apo izo ndi kupezapo.

161 Tsopano, ine ndiri nalo la *Facts Of Our Faith,* ilo limatchedwa, mu mpingo wa Katolika, pakuti makolo anga anali a Katolika achi Irish. Kotero ine ndikudziwa chomwe ine ndikuchiyankhula. Mukuona?

162 Ndipo izo mwamtheradi ndizo choonadi, uko nkulondola, kuti apo. . .Ndipo Baibulo linanena kuti "Iye akanati azidzakhala pansi mu tchalitchi, kapena ma—malo, kapena tchalitchi chimene chiri pa mapiri asanu ndi awiri mu Roma, ndipo mphamvu yake idzapita mdziko lonse. Ndipo iye akutchedwa wotsutsakhristu."

163 Ndipo kuchokera mu mpingo umenewo kunadza mipingo yaing'ono yomwe inabadwa pambuyo pa iwo, ndipo anati, "Iye anali hule, ndipo iwo anali timahule amene amamutsatira iye." Uko nkulondola. Ndi inu apo. Pakuti iwo anachita bungwe mu chinthu chomwecho, ndipo anali ndi tizikhulupiriro tawo ndi ziphunzitso. Zocheperapo pang'ono pokha, osati amphamvu monga iye aliri, koma iwo akadali nazo mphamvu. Ndipo *chirombo* chimatanthauza "mphamvu." Ndi inu apo. Kotero iwo ali ndi, Akatolika ali ndi mphamvu zazikulu kwambiri. Achimethodisti, ndipo kenako Achipresbateria, ndipo kenako Achilutera, ndipo kenako Achibaptisti, ndipo kenako ena otero, ndi kupitirira nazo pansi. Iwo ndi mphamvu zazing'ono, zopangidwa bungwe, "Mpingo wanga! Mpingo wanga! Mpingo wanga! Mpingo wanga!"

164 Koma wokhulupirira woona samanena kanthu za izo. Zimakhala "Khristu wanga! Khristu wanga! Khristu wanga!" Ndiko kusiyana kwake. Inu mumawadziwa bwanji? Mzimu Woyera umachitira umboni ndi zizindikiro ndi zozizwitsa.

165 Apa pali laling'ono, mtundu wa laling'ono lokuponyera mmbuyo. Ine ndikudana nazo kuziwerenga izi, koma winawake analiika ilo pano:

34. Inu munafunsa chifukwa chimene kachisi uyu samapitirira mtsogolo. Chifukwa chake, ndi chakuti ena mwa madikoni amakana mphatso ya malirime ndi machiritso. Ife tonse tikudziwa kuti Izo ndi zoona.

166 Ndiroleni ine kuti ndidziwe yemwe ali, pamene ine ndikadali pano pa—pa msonkhano wokopa uwu, ndipo ameneyo achotsedwa mofulumira.

35. Chonde fotokozani ngati Mkhristu amayenera kuchita za kutsuka mapazi, ndi ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu (Dzina) mmalo mwa dzina la "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." Chonde.

167 Chabwino. Ine ndinali nawo pafupi atatu a iwo muno amene anafunsa chinthu chomwecho.

168 Za kutsukana-mapazi, chabwino, ine mwina ndikhoza kungoyambira pa icho. Chabwino, tsopano inu mukhoza kusiyana, izo nzabwino ndithu. Ndiroleni ine ndingowerenga zochepa, mphindi yokha. Kapena ngati inu mukufuna kuti muziwerenge izo, pezani Yohane Woyera, mutu wa 13, mphindi yokha. Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake apa. Ndipo mvetserani ku chimene Yesu ananena, Mwiniwake, ndiyeno ine ndikutengerani inu chitsogolo uko mu Chipangano ndi kukakuwonetsani inu kuti chikusungidwabe mopitirira. Yambirani pa ndime ya 2.

> *Tsopano mgonero utatha, mdierekezi* ata . . . *ika* mu *mtima wa Yudasi Iskarioti, mwana wa Simoni, kuti ampereke iye;*
>
> *Yesu podziwa . . . Atate anampatsa zinthu zonse mmanja ake,* . . . iye anabwera *kuchokera kwa Mulungu, ndipo anapita kwa Mulungu;* (Iye anabwera kuchokera mu Mzimu, nakalowa mu thupi, ndipo anabwereranso mu Mzimu. Mukuona?)
>
> Ndipo *Iye anawuka kuchokera pa mgonero, ndipo anaika pambali zovala zake; . . . natenga chopukutira, . . . nadzimanga nacho iyemwini.*
>
> *Atachita izo iye* anatsanulira *madzi mu msambidwe,* nayamba *kusambitsa mapazi a ophunzira, ndi kumawapukuta iwo ndi chopukutira chimene iye anadzimanga nacho.*
>
> *Ndiye anadza iye kwa Simoni Petro: ndipo Petro* anati *kwa iye, Ambuye, kodi mutsuka mapazi anga?*
>
> *Yesu* . . . ananena *kwa iye, Chi—chimene ine ndikuchita* pano *iwe sukuchidziwa ayi . . . koma iwe uchidziwa kuchokera pano.*
>
> *Petro* ananena *kwa iye, Inu* musati *musambitse konse mapazi anga. Yesu anayankha* ndipo anati kwa *iye,*

Ngati ine sindikusambitsa iwe, iwe ulibe gawo limodzi ndi ine. (O, kodi inu mungalingalire izo! Chabwino.)

Simoni . . . ananena kwa *iye, . . . osati mapazi anga okha, koma . . . manja anga ndi mutu wanga.*

Ndipo *Yesu* anati *kwa iye, Iye amene wasambitsidwa . . . kupatula . . . asoweka . . . kuti asambe mapazi ake,* ndiwe *woyera paliponse: . . . koma osati nonse.*

Pakuti iye ankadziwa amene akanati amupereke iye; kotero iye anati, Inu *simuli oyera nonse.*

Chotero atatha iye kuwasambitsa mapazi awo, ndipo anali—atatenga zovala zake, ndipo anali *atakakhalanso pansi kachiwiri, iye ananena kwa iwo, Kodi inu mukudziwa chimene ine ndakuchitirani* kwa *inuchi*?

Inu mumanditcha ine Mphunzitsi ndi Ambuye: ndipo inu *mumanena bwino; pakuti ndi chomwe ine ndiri.*

Ngati ine ndiye, Mbuye wanu ndi Mphunzitsi, ndasambitsa mapazi anu; . . . inu *muyenera kumasambitsana mapazi a wina ndi mzake.*

Pakuti ine ndakupatsani inu chitsanzo, kuti inu *muzichita* kwa wina ndi mzake *monga ine ndachitira* kwa *inu.*

. . . inu mukhala okondwa ngati inu muzidziwa zinthu izi ndi *kumazichita* izo.

169 Cha mu Timoteo wachiwiri uko, Paulo anati, polembera kwa mpingo, "Musati muzilola kuti wamasiye azibweretsedwa mu mpingo mpaka iye akhale atasambitsa mapazi a oyera." Uko nkulondola. Kusambitsana-mapazi kunali kusungidwa konse kudutsa mmasiku a Baibulo. Ndipo mwa chithandizo cha Mulungu, ngati ine ndisunga malingaliro anga oyenera, ndipo Mulungu atandithandiza ine, ine ndizisungabe izo mpaka ine ndidzafe. Uko nkulondola. Uko ndiko ndendende kutuma kwa Yesu Khristu!

Tsopano, pano pakhala funso lobaya.

36. Nchifukwa chiani munthu angati azibatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu mmalo mwa "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera"?

Ine ndiri nawo awiri kapena atatu. Apa pali limodzi pomwe apa:

37. M'bale Bill, ndi ubatizo wabodza uti uja womwe inu mumaukamba usiku wathawu, ngati iwo uli wa madzi kapena Mzimu? Ngati iwo uli wa madzi, ndipo inu munati Dzina la Yesu Khristu, nchifukwa chiyani pa Mateyu 28:19, apo amati, "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera"? Chonde tafotokozani.

170 Tsopano, awa akukhala ngati obaya, koma ine ndikukhulupirira ine ndiri nalo limodzi lina pano penapake, chinthu chomwecho. O, izo ziri pafupi malo atatu. Ine ndiyesera kuti ndifike kwa ilo. Tiyeni tiwone. Kodi—kodi inu mungapirire nane kwa maminiti pang'ono? Chabwino. Tsopano, tiyeni ife tingoyamba tsopano ndi kuyankha mafunso awa. Mwinamwake ife tikhoza kuwaimitsa owerengeka a iwo, ndi kudzawatenga iwo mwina (otsala a iwo) mawa; ngati palibe ena, pa Sande sukulu, kapena nthawi ina. Koma anthu awa mwina . . . akufunsa izi, ndipo mawa ndi la ubatizo. Tsopano, njira iliyonse yomwe munabatizidwira, izo ziribe kanthu kwa ine. Koma ine ndikufuna kuti—kuti ndikuuzeni inu Chiphunzitso chautumwi cha Baibulo. Mukuona?

171 Tsopano, ife tinapeza izo, usiku watha, kuti pamene mpingo wa Katolika unapangidwa bungwe, kuti iwo unabwerapo ndi mgonero wabodza, kumanena kuti, "Pamene iwe ulandira Ukalisitiya woyera, kutanthauza mgonero woyera pamenepo, iwe walandira Mzimu Woyera." Umenewo si Mzimu Woyera; ako ndi kokulumunya.

172 Mpingo wa Chiprotestanti amagwirana chanza, amaika maina awo pa bukhu, ndi chomwe iwo amachitcha, "kuulandira Iwo."

173 Tsopano, koma njira yeniyeni youlandirira Iwo ndiyo ubatizo wa Mzimu.

174 Ndipo, tsopano, mpingo wa Katolika unabweretsapo katekisimu. Lutera anali naye, mpingo wa Methodisti unali naye, Achiepisikopu ali naye iye, ambiri enawo ali naye iye, katekisimu. Yambiri ya miyambo ya mpingo wa Katolika imakaniririrabe kwa mpingo wa Chiprotestanti; yomwe imawapanga iwo mkati mwawomo limodzi nawo, malingana ndi Baibulo.

175 Koma panalibe konse munthu, nkale lomwe, mu masamba onse a Baibulo, anayamba wabatizidwapo mu dzina la "Atate, Mwana, Mzimu Woyera." Panalibe konse munthu anabatizidwapo mu dzina la "Atate, Mwana, Mzimu Woyera" mpaka mpingo woyambirira wa Chikatolika. Iwo suli mu Baibulo, palibe pena! Ngati aliyense angakhoze kupeza chidutswa mmenemo, ndi kundiuza ine ndi kundisonyeza ine pamene munthu mmodzi anabatizidwapo pogwiritsa ntchito dzina la "Atate, Mwana, Mzimu Woyera" chonde ndiwonetseni ine, pakuti ine ndadutsamo ndi kudutsamo ndi kudutsamo Izo, kwa zaka zina twente foro zododometsa tsopano. Ndipo izo ndi zolakwika! Icho ndi kachikhulupiriro ka Chikatolika ndipo si lamulo la Baibulo.

176 Tsopano ife tipeza chifukwa chake, ife tikupita ku funso lanu, m'bale wokondedwa. Yohane Woyera . . . Ine ndikutanthauza Mateyu 28:19. Chabwino, tiyeni tibwerere uko.

Inu mutsegule nawo Baibulo lanu, limodzi nane, chotero inu mukhoze kuwerenga limodzi ndi ine. Awa ndi malo pamene izo zikuyankhulidwa. Malo amodzi mu Baibulo a . . .

177 Kodi Yesu sanati, "Mkamwa mwa mboni ziwiri kapena zitatu muzilola mawu aliwonse kukhazikitsidwa"?

178 Ine ndikhoza kukutengerani inu mu Baibulo pamene Ilo linati, "Yudasi Iskarioti anapita nakadzipachika yekha," ndipo, "Inu pitani mukachite monga choncho."

179 Ine ndikhoza kukutengerani inu pamene Yesu anati, "Pamene Mwana wa munthu," chimene Iyemwini anali, "amene tsopano ali Kumwamba, adzabwera kachiwiri," ndipo ataimirira komwe kuno pa dziko lapansi. Ndipo anati, "Mwana wa munthu yemwe tsopano ali Kumwamba," ndipo ataimirira komwe kuno pa dziko lapansi.

180 Inu mumayenera kumudziwa Mulungu kuti muziwadziwa Mawu Ake. Inu simungakhoze . . . Nzosadabwitsa kuti inu mumati, "Ilo limadzitsutsa Lokha." Ilo ndi losokoneza; chifukwa Mulungu anati Iye analilemba Ilo mwanjira imeneyo kuti alibise Ilo kwa ophunzira awa ndi ena otero. Ndipo mukalola anthu akhale odzichepetsa pa guwa, ndipo Mulungu amaliululira ilo kwa iwe.

181 Tsopano pano nali Lemba, Mateyu 28:19, malo okha mu Baibulo omwe anayamba atchulapo maudindo awa.

> *Pitani inu tsopano, ndi kukawaphunzitsa mafuko onse, nkumawabatizira iwo* mu *dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera:*

182 Tsopano, momwe inu munabatizidwira, ndi, "mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana, ndi mu dzina la Mzimu Woyera." Izo siziri konse mu Lemba! Koma izo ziri apa, "Kawaphunzitseni mafuko onse, nkukawabatiza iwo mu Dzina!" Tsopano yang'anani kumene mu Baibulo lanu ndi kuwona ngati ilo likuti "mu *maina*" kapena "mu Dzina."

183 Tsopano inu mukuti . . . Tsopano, kuno osati kale litali mu msonkhano, mnyamata anati, "Muli zotsutsana mu Baibulo!" Ndinati, "Ine ndikukhumba iwe ukanafotokoza izo kwa ine. Nchifukwa chiyani Yesu anawauza anthu kuti azibatiza mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera, ndipo Petro anatembenuka apo ndi kuwabatiza iwo mu Dzina la 'Yesu Khristu,' mu Machitidwe 2:38?" Anati, "Ngati izo sizikudzitsutsa zokha, ine sindikuziwona zotsutsanazo!"

Ine ndinati, "Chifukwa chokha chakuti inu simunamufune Mulungu molondola."

184 Iye anati, "M'bale Branham, kodi izo zimapangitsa kusiyana kulikonse ngati ine ndibatiza mwanjira *iyi* kapena mwanjira *iyo*?" Izo ndithudi zimapanga, ndipo ine nditsimikizira izo mwa Baibulo.

185 Bwanji ngati—bwanji ngati Mose. . . Mulungu anamuuza Mose, bwera ku chitsamba, anati, "Mose, vula nsapato zako, iwe uli pa malo Oyera."

186 Iye akanati, "Tsopano, Ambuye, ndine munthu wolemekezeka. Nsapato zanga ndi zovuta pang'ono kuti ndizivule, chotero ine ndingovula chipewa changa." Iye sanati konse "chipewa," Iye anati "nsapato!" Ndipo chimene Baibulo linena ndicho Choonadi. Tsopano ngati. . .

187 Pano, awa ndi masiku khumi, apa panali pa kukwera mmwamba. Ndipo pamene Yesu anali kutengedwera mmwamba, Iye anawatuma ophunzira Ake kuti apite mu dziko lonse ndi kukaphunzitsa mafuko onse, kumawabatiza iwo mu dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Ndipo masiku khumi kenako. . . Iwo anapita ku Yerusalemu ndipo anakadikirira mu chipinda chapamwamba mpaka Mzimu Woyera utabwera. Ndiyeno pamene iwo anayamba kulalikira ndi kumapitirira nazo. . . Iwo anati, "Kodi ife tingachite chiyani kuti tipulumutsidwe?"

188 Petro anati, "Lapani, aliyense wa inu, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu."

189 Kenako iye anapita ku nyumba ya Kornelio, iye anati, "Lapani, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu."

190 Iye anapita ndipo anakawapeza anthu ena omwe anali atabatizidwa kale, anati, "Inu muyenera kuti mubatizidwenso kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu!"

191 Ndipo anapita mpaka ku Samaria ndipo anati, "Abatizeni iwo mu Dzina la Yesu Khristu."

192 Ndipo palibe nthawi imodzi yomwe maudindo awo anayamba atchulidwirapo pa munthu. Palibe! "Tsopano, muli zotsutsana ndiye," inu mukuti. Ayi, mulibe. Ingopemphani Mzimu Woyera tsopano, ndipo mumuwone Iye akuwululira Izo kwa inu. Tsegulani mtima wanu.

193 Tsopano, musati mukhale oweruziratu. Ngati inu mutero, Mulungu sangakhoze kuyankhula kwa inu. Koma ngati inu mukhala osaweruziratu, munene, "Ine ndikufunafuna Choonadi chenicheni, M'bale Branham."

194 Ngati Yesu anawauza ophunzira, "pitani mukachite *ichi*," ndipo iwo anapita nakachita chinachake cha *uku* mosiyana, ndipo komabe Mulungu anachidalitsa icho, ndipo monse kudutsa mu Baibulo. Tsopano, kodi iwo anakachita zomwe Yesu anawauza iwo kuti asakachite? Ngati anatero, iwo sanamvere, ndipo Mulungu sadzalemekeza konse kusamvera. Ngati Iye akanatero, Iye bwenzi atamulemekeza Eva ndi kuleketsa chinthu chonsecho pachiyambi. Pamene Mulungu anena chirichonse, Iye amayenera kuti azisunga Mawu Ake; Iye ndi wochita mwayekha. Kotero ndiye mwina Petro analakwitsa. . .

195 "O," anati, "izo ndi zomwe atumwi ananena," Mnyamata wina anatero, "Izo ndi zomwe atumwi ananena. Ine ndipita kumakachita zomwe Yesu ananena."

196 Chabwino, ngati atumwi ankachita zomwe Yesu anawauza iwo kuti asachite, ndiyeno chiyani? Ndipo ngati atumwi omwe analemba Baibulo ili. . . Paulo analemba zonse izi, ndipo Paulo anali yemwe anawapangitsa iwo kuti abatizidwenso kachiwiri. Ndipo ngati Paulo analemba gawo lalikulu la Chipangano Chatsopano ichi, ndiye ndi Baibulo la mtundu wanji lomwe inu muli nalo litalembedwa limene inu mukuyesera kumaliwerenga?

197 Tiyeni tingolipanga ilo Ichi basi. Funsani moganiza bwino kwenikweni ndipo muwona zomwe Mawu akunena. Tsopano, izi nzoti tiphunzirepo, kuti inu muwadziwe Mawu a Mulungu.

198 Tsopano, ngati Petro ankabatiza mu Dzina la Yesu Khristu Yesu atamuuza iye kuti azikabatiza mu dzina la "Atate, Mwana, Mzimu Woyera," iye anachita mosiyana ndi zomwe Yesu ananena. Ndi zoona izo? Tsopano, payenera kukhala pali chinachake apo. Tsopano tiyeni tingochipeza, ndipo tiwupemphe Mzimu Woyera kuti utisonyeze ife. Tsopano, malo oyamba, tsopano tiyeni titenge—tiyeni titenge Lemba loyamba, Mateyu 28:19.

> *Pitani inu chotero, . . . mukawaphunzitse mafuko onse, nkumakawabatiza iwo* mu *dzina la Atate, . . . Mwana, . . . Mzimu Woyera:*

199 Tayang'anani apo pa Baibulo lanulo ndipo muwone ngati ilo likuti "mu *maina* a Atate, ndi a Mwana, ndi a Mzimu Woyera." Kodi likutero ilo? Ayi, bwana. Kodi ilo linati, "mu *dzina* la Atate, mu *dzina* la Mwana, mu *dzina la* Mzimu Woyera"? Ilo linati, "Mu Dzina!" Ndi kulondola uko? Chabwino, "dzina" linali limodzi. Nkulondola uko? Chabwino, ndi dzina liti lomwe Iye ankafuna kuti iwo azibatiza nalo, dzina la Atate, kapena dzina la Mwana, kapena dzina la Mzimu Woyera? Iye anati, "Mu Dzina!" Chabwino, moona, palibe ngakhale limodzi la iwo liri dzina.

200 Ndi atate angati ali muno, tiyeni tiwone dzanja lanu—dzanja lanu. Chabwino. Ndi uti wa inu dzina lake liri "Atate"? *Atate* si dzina; *atate* ndi "udindo." Ndi ana angati ali muno? Zedi, bambo aliyense, mwamuna aliyense, iwo ndi ana. Chabwino, ndi uti wa inu dzina lake liri "Mwana"? Si dzina; uwo ndi udindo. Kodi uko nkulondola? Si dzina; iwo ndi udindo. Chabwino, ndi uti wa inu dzina lake liri "Munthu"? Ndi anthu angati ali muno? Nonse inu. Chabwino, ndi uti wa inu dzina lake liri "Munthu"? Palibe chinthu choterocho; icho ndi chimene inu muli. Mzimu Woyera si dzina; ndi chimene Iwo uli. Ine ndine munthu. Chotero si ngakhale Atate, Mwana, kapena Mzimu Woyera ali "dzina"; iwo angokhala *maudindo* atatu omwe amapita kwa Dzina limodzi.

201 Tsopano mvetserani mwatcheru. Nchiyani . . . Penyani kuno! Ine ndizitenga izi basi ngati pa maziko a mwana. Ngati inu mukanati, chabwino, monga inu mukanati muziwerenga bu—bukhu la nthano, ndipo ilo likanati, "Yohane ndi Maria ankakhala mokondwa nthawizonse pambuyo pake." Ndipo inu mukanamadadwa ndiye, "Kodi Yohane ndi Maria ndi ndani?" Chabwino, njira yokha yomwe inu mukanadziwira yemwe Yohane ndi Maria ali, ndi kupita mmbuyo ndi kukawerenga koyambirira kwa nkhaniyo ndi kudutsa nayo. Ndi kulondola uko?

202 Chabwino, ngati Yesu ananena apa, "Kabatizeni mu Dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera," ndipo Atate si dzina, ndi Mwana si dzina ndi Mzimu Woyera si dzina, bwanji, kodi Munthu uyu ndi ndani? Ife tikufuna kuti tidziwe yemwe Iye ali. Tsopano, chinthu chopambana kuti tichite . . . Uwo ndi mutu wotsiriza wa Mateyu, ndime yotsiriza. Tiyeni titembenuzire mmbuyo ku mutu wa 1 wa Mateyu, ndi ndime zoyamba, ndipo tiyambire nazo, tipeze omwe awa Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ali. Tsopano, ine ndingofuna kuti ndichite izi chifukwa cha ana apo, kuti nawonso azimvetse izi.

203 Chinthu choyamba, ichi chikuwongolani inu pa "utatu" wanuwo, Atate, Mwana, Mzimu Woyera. [M'bale Branham akufotokoza ndi zinthu zitatu—Mkonzi.] Tsopano, mu malo oyamba, palibe malo amodzi mu Baibulo pamene *utatu* unatchulidwapo. Inu mukapapeze apo ndi kudzandisonyeza ine. Palibe chinthu choterocho. Ndi kulakwitsa kwa Chikatolika, ndipo inu Achiprotestanti mumagwadira kwa izo. Zindikirani. Tsopano, kodi *ichi* ndi chiyani? Ine ndinati *ichi* ndi Ndani? Atate. *Ichi* ndi Ndani? Mwana. Ndipo *ichi* ndi Ndani? [Osonkhana akuti, "Mzimu Woyera."] Tsopano, Atate ndi atate a Ndani? Mwana. Ndi kulondola uko? Tsopano, ichi ndi Atate a Yesu. Musati mufike pozisokoneza izo, tsopano. *Ichi* apa ndi Atate, *ichi* ndi Mwana, ndipo *ichi* ndi Mzimu Woyera. Nkulondola uko? Tsopano, anthu amawaika iwo, "Anthu atatu osiyana, Amulungu atatu osiyana, umunthu utatu wosiyana." Palibe zodabwitsa kuti Myuda sangakhoze kuzimvetsa Izo! Chabwino.

204 Mateyu mutu wa 1, akuyamba ndi mibadwo ya Yesu Khristu, "Abrahamu anabala Isaki, Isaki anabala Yakobo," mpakana, kutsika monga choncho, mpaka zikufika mmunsi ku ndime ya 18.

Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu . . .

205 Pano izo ziri, ndime ya 18.

Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu . . . (zinditsatirani ine ndi Baibulo lanu) . . . *kubadwa kwa* munthu uyu *Yesu Khristu kunali motere: Pamene . . . amayi ake Maria anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe, . . . iye anapezeka ali ndi mwana wa* . . . (Mulungu, Atate?)

Kodi ine ndawerenga Izo molondola? Kodi Ilo likuti chiyani? [Osonkhana akuti, "Mzimu Woyera!"—Mkonzi.] Anapezeka ali ndi mwana wa Ndani? ["Mzimu Woyera."] Ine ndimayesa winawake anati Bambo uyu anali Atate Ake? Baibulo lati Bambo uyu anali Atate Ake.

. . . iye anapezeka ali ndi mwana wa Mzimu Woyera.

206 Tsopano inu ndi mtundu wanji wa mwana yemwe muli naye? Ndipo Yesu momveka ankati Mulungu anali Atate Ake. Ndi kulondola uko? Mulungu ndi Atate Ake! Chabwino, ndiye Mzimu Woyera uli ndi chochita chanji nazo ndiye? Ngati Baibulo linati Mzimu Woyera unali Atate Ake, ndipo Yesu anati Mulungu anali Atate Ake; ndipo inu mukuti Mulungu anali Atate Ake, ndipo tsopano Baibulo likuti, cha apa. Ngati alipo atatu, anthu awiri osiyana, Mulungu analibe chochita nazo izo. Mzimu Woyera ndiwo Atate Ake.

207 Tsopano tiyeni tiwerenge mopitirira pang'ono.

. . . Yosefe mwamuna wake, pokhala munthu wolungama, sanali kulolera *kuti amuchititse iye manyazi poyera,* koma *analingalira* kuti *amusiye iye mwamseri.*

Koma, taonani, *pamene iye anali kulingalira pa zinthu izi, . . . mngelo wa Ambuye anawonekera* kwa *iye mu loto, nkuti, Yosefe, iwe mwana wa Davide, usawope ayi . . . kudzitengera kwa iwe Maria mkazi wako: pakuti icho chomwe chiri choyembekezeredwa mwa iye ndi cha Mzimu Woyera.* (osati Mulungu Atate; Mulungu Mzimu Woyera!)

208 Mukuona kumene lingaliro lanu la utatu likanati lipiteko? Ilo likanamuika Yesu ngati mwana wapathengo. Ndithudi. Uko nkulakwitsa! Palibe Lemba kwa izo. Tsopano, inu muyenera kuvomereza kuti Mulungu Atate ndi Mulungu Mzimu Woyera, ndi Munthu yemweyo, kapena Yesu anali ndi abambo awiri osiyana. Ndi kulondola uko? Ndithudi, uko nkulondola. Baibulo linati, "Mzimu Woyera unali Atate Ake," ndipo Baibulo linati, "Mulungu anali atate Ake." Tsopano, abambo Ake ndi ati? Mzimu Woyera ndi Mulungu ziri Mzimu womwewo; Ndi Chinthu chomwecho.

. . . zonse izi zinachitika, kuti chikakhoze kukwaniritsidwa chimene . . . chinayankhulidwa ndi mneneri, ndi Ambuye, *kuti,*

*. . . namwali adza*ima . . . ndipo *adzabala* mwana, *ndipo iwo . . . (*Mmodzi *uyu)*

. . . ndipo iwo adza*mutcha dzina lake YESU: pakuti iye adzawapulumutsa anthu ake ku machimo* awo.

Ndipo ichi chonse *chinachitidwa, kuti chikakhoze kukwaniritsidwa, . . .*

. . . ndipo *dzina lake* adzatchedwa *Emanuele, lomwe* liri mwa kutanthauzira, *Mulungu ali nafe.*

209 Tsopano, kodi Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ndi ndani? Kodi Petro anachita molakwitsa? Iye anachita zomwe Yesu anamuuza iye. Awo ndi maudindo atatu.

210 Ine ndine mtumiki, ndipo ine ndine bambo, ndipo ine ndine "M'busa," iwo amautcha iwo, udindo, koma apo palibe dzina langa. Dzina langa ndi William Branham.

211 Iye *anali* Atate, Iye *anali* Mwana, Iye *anali* Mzimu Woyera. Inu mukuyesera kupanga Amulungu atatu, mzanga; ndi kulakwitsa; ndi cholakwika.

212 Pali nyengo zitatu zomwe utatu unasokonezeka nazo. Mulungu, Atate, anali Mzimu umene unkaima pamwamba pa ana a Israeli mu Lawi la Moto. Ndi kulondola uko? Mulungu anali mmenemo. Ndiye Mulungu anapangidwa thupi nadzakhala pakati pathu (ndi kulondola uko?) mwa Mwana Wake. Tsopano Iye akudzichepetsa natsika mpaka Iye wabwera mu mtima wa munthu, mwa Mzimu Woyera.

213 Mulungu ali ngati muyezo wa mapazi atatu, kapena, muyezo wa mapazi-atatu, inde. Mainchesi thwelofu oyambirirawo anali Mulungu, Atate; mainchesi thwelofu achiwiri, Mulungu, Mwana, Mulungu yemweyo; mainchesi thwelofu achitatu anali Mulungu, Mzimu Woyera, Mulungu yemweyo. Yesu anati . . .

214 Inu mumati, "Chabwino, ife tiri nawo Mzimu Woyera mkati mwathu." Uko nkulondola.

215 Koma Yesu anati, "Kanthawi pang'ono, ndipo dziko silimandiwona Ine kenanso. Komabe inu muzindiwona Ine, pakuti Ine . . ." "Ine" puronauni yaumwini. "Ine ndidzikhala ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka ku mathero a dziko." Mzimu Woyera uli pati ndiye? "Ine sindidzakusiyani inu opanda mtonthozi; Ine ndidzabweranso ndi kudzakhala ndi inu." Ndi zimenezo.

216 Inu mukuona, inu mukumvetsa molakwika, mzanga. Ndi Mulungu mmodzi mu nyengo zitatu. Nyengo ya Utate, Umwana, ndi Mzimu Woyera, Ndi Mulungu yemweyo. Ndipo pamene Iye anati, "Pitani muzikawabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera," Ameneyo anali Yesu Khristu. Ndipo nchifukwa iye amabatiza mu Dzina la Yesu.

217 Tsopano tapenyani, tiyeni tipeze maubatizo apa. Nthawi yoyamba yomwe ubatizo unayamba watchulidwapo mu Chipangano Chatsopano, anali Yohane Mbatizi. Ndi kulondola uko? Ine ndiika *ichi* apa. Inu mukuwona, inu muyenera kuti muwuongole Umulungu wanu musanawuongole ubatizo wanu. *Uyo* ndi Yohane M'batizi, ubatizo woyamba.

218 Nthawi yachiwiri ubatizo unakambidwapo, panali pa Machitidwe 2:38, pamene iwo anabatizidwa mu Dzina la Yesu

Khristu, ku mpingo watsopano. Malo achiwiri anali ku nyumba ya Kornelio, kapena ayi . . . Ine ndikupempha kukhululukira kwanu, Asamaria, Machitidwe 7:48 ndi 49. Ndi Machitidwe 10:49 ndi pamene iye anawabatiza iwo ku nyumba ya Kornelio. Ndipo nthawi yotsatira ubatizo unayankhulidwa, ndi kutchula maina aliwonse kapena maudindo, panali uko pa Machitidwe 19:5.

219 Tsopano, pamene iwo ankabatizidwa pa Tsiku la Pentekoste, iwo anabatizidwa, Machitidwe 2:38, mu Dzina la Yesu Khristu. Ndi kulondola uko? Zilembeni izo, mukaziyang'ane izo apo.

220 Kotsatira, Filipo anapita uko, masiku awiri kenako, ndipo anayamba kulalikira kwa Asamaria; ndipo analalikira kwa iwo, ndi kuchiritsa odwala, ndipo anali ndi msonkhano waukulu kumeneko, ndipo anawabatiza iwo mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Petro anapita uko nakaika manja pa iwo; iwo analandira Mzimu Woyera.

221 Petro anapita pamwamba pa denga la nyumba paja masiku angapo kenako, anali ndi njala, iye anawona masomphenya. Mulungu anamutumiza iye ku nyumba ya Kornelio. Ndipo, "Pamene Petro anali chiyankhulire Mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa iwo," ndipo iwo anayamba kuyankhula mu malirime ndi kumapitiriza nazo momwe iwowo anachitira poyamba paja. Petro anati, "Iwo anali asanabatizidwe nkomwe apabe." Chotero iye anawalamulira iwo, aliyense, kuti abatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu.

222 Munthu aliyense mu Baibulo amabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Paulo . . . ine ndikutanthauza, ophunzira a Yohane sankabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, iwo ankabatizidwa kuloza ku kulapa. Tiyeni titembenuzire ku Akorinto Woyamba . . . ine ndikutanthauza, tiyeni titembenuzire ku Machitidwe, mutu wa 19, mphindi yokha. Ndipo tiwerenge izi mphindi yokha kuti inu muwone, abwenzi, kuti si—si . . . Iwo sali . . . Lemba silimadzitsutsa Lokha. Yang'anani apa.

> *Ndipo zinafika pochitika, kuti, pamene Apolo anali ku Korinto, Paulo . . . anadutsa ku chigwa cha kumtunda* cha . . . *Efeso:* iye anapezako *ophunzira ena,*
>
> *Iye anati kwa iwo, Kodi* inu *munalandira Mzimu Woyera kuyambira pamene* inu *munakhulupirira? . . . iwo anati* . . . Ife sitikudziwa konse *ngati pali Mzimu Woyera uliwonse.*
>
> . . . *iye anati* . . . ndiye inu *munabatizidwa* mu chiyani?
>
> O, iwo anati, ife tinabatizidwa.
>
> Anati, Motani?
>
> . . . *anati, Kwa* Yohane, Yohane . . .
>
> Iye anati, Yohane ankabatiza kuloza ku kulapa, kumanena *kuti* inu *mumukhulupirire iye* yemwe *amadza . . . ameneyo ndi, pa* Ambuye *Yesu Khristu.*

Ndipo *pamene iwo anamva izi, iwo* anabatizidwanso *mu dzina la Yesu Khristu.*

. . .Paulo *anaika manja ake pa iwo,* ndipo *Mzimu Woyera* unadza *pa iwo; ndipo iwo* anayankhula mu *malirime, ndipo analosera.*

223 Paulo Woyera wamkuluyo . . .

224 Mvetserani! Bwanji ngati inu mukanakhala kuti munabatizidwa ndi Yohane M'batizi, munthu yemweyo amene anamubatiza Yesu Khristu? Munthu woyera, amene Yesu anati, "Sipanayambe pakhala munthu wobadwa ndi mkazi, wamkulu monga Yohane M'batizi." Iye ndi mkulu wa aneneri onse. Iye anamutsogolera Yesu kukalowa mmadzi ndipo anamubatiza Iye mu Yordani momwe. M'bale, ngati ine ndikanabatizidwa ndi iye, ine ndikanamamverera mwabwino kwambiri nazo izo. Nkulondola uko?

225 Koma Paulo akutembenuka apo ndipo akuti, "Izo sizigwira ntchito tsopano!" Anati, "Inu muyenera kuti mubatizidwenso, kachiwiri."

226 "O, ife tinamizidwa, ngakhalenso, Paulo! Ife tinamizidwa ndi Yohane, uko komwe mu Mtsinje wa Yordani."

227 Iye anati, "Izo sizigwira ntchito tsopano. Inu muyenera kuti mubatizidwe kachiwiri."

"Motani?"

228 Anati, "Yohane ankabatiza kuloza ku kulapa. Uku ndi kwa kuchotsedwa kwa machimo, ndipo palibe dzina lina pansi pa Kumwamba lapatsidwa pakati pa anthu, Dzina la Yesu Khristu lokha." Ndipo iwo ankayenera kuti achite kubatizidwanso, kachiwiri, mu Dzina la Yesu Khristu.

229 Ndipo palibe malo amodzi mu Baibulo, kapena mbiriyakale yonse kwa zaka sikisi handiredi zoyambirira pambuyo pa imfa ya mtumwi wotsiriza, pamene iwo anayamba abatizidwapo mwanjira ina iliyonse kupatula mu Dzina La Yesu Khristu.

230 Ndipo pitani mukamfunse wansembe wa Chikatolika aliyense yemwe inu mukumufuna, afunseni iwo omwe anazisintha izo, ndi kukawona zomwe iwo ati akakuuzeni inu. Katengeni katekizimu ndipo mukaiwerenge iyo; amati, "Zedi, ena a Achiprotestanti adzapulumutsidwa chifukwa iwo anagwadira ku ubatizo wathu." Iwo anawusintha iwo. Iwo amati iwo ali nayo mphamvu ndi ulamuliro wochitira izo, ndipo inu mumakhulupirira izo! Ndi chimene iwo amanena, ndi chimene iwo amadzinenera, ndi chimene mpingo wa Chiprotestanti umagwadirako. Koma, Mwamalemba, izo ziri mwamtheradi zilibe nusu limodzi la Lemba pa izo.

Iwo ankayenera kuti abatizidwenso, mu Dzina la Yesu Khristu!

231 Tsopano mvetserani, mwamsanga tsopano, kuti ife tifike pomwe. . . Ine sindikufuna kuti ndikugwireni inu motalika kwambiri pa mafunso awa. Penyani, tsiku limene Yesu anatsika kuchokera pa Phiri la Chiwalitsiro ndi ophunzira Ake, Iye anati, "Kodi anthu amati ndine yani, ndipo kodi iwo amati chiyani?"

232 "Ena amati Inu ndinu 'Yohane Mbatizi,' ena akuti Ndinu 'Eliya,' ena amati Ndinu 'mneneri.'"

Iye anati, "Koma inu mukuti ndine ndani?"

233 Ndipo Petro anati, "Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo!"

234 Iye anati, "Wodala ndiwe, Simoni—Simoni Mwana wa Yona," anati, "pakuti thupi ndi mwazi sizinaululire izi kwa iwe. Iwe sunakaziphunzire izo mu mpingo wina, iwe sunakaziphunzire izo mu seminare ina. Koma Atate Anga awululira izi kwa iwe, ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga ndipo zipata za gehena sizidzawulaka Iwo."

235 Tsopano, mpingo wa Katolika umati, "Ameneyo anali Petro. Iwo anali ndi mwala pamenepo, ndipo iwo ukadalipobe uko ku Mzinda wa Vatikani." Ndipotu uko kunali ku Yerusalemu, kapena mu Palestina. Ndipo iwo ananena kuti uwo unali mwala.

236 Mpingo wa Chiprotestanti umati, "Anali Petro amene iwo anamangirapo Mpingo." Ngati izo ziri chomwecho, iwo unabwerera mmbuyo masiku angapo kenako. Siunali iwo.

237 Mpingo unamangidwa pa vumbulutso Lauzimu la Mulungu. "Thupi ndi mwazi sizinaulule izi kwa iwe, Petro, koma Atate Anga omwe ali Kumwamba awululira izi kwa iwe. Ndipo pa thanthwe ili, vumbulutso lauzimu la Mawu a Mulungu, Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzaulaka Iwo konse."

238 Ndi pamene ine ndikuti, Lutera, Methodisti, ndi chirichonse chomwe inu muli, chirichonse, Achipentekoste, ndi chirichonse chomwe inu muli, sizikupanga kusiyana kulikonse; pamene Mpingo wa Mulungu ukusunthira mtsogolo, mu mphamvu ya kudzoza, iwo uzisunthira mtsogolo momwe ndi mtsogolo ndi mtsogolo ndi mtsogolo. Ndipo palibe chipembedzo chingawuimitse Iwo, palibe chirichonse mu dziko chingawuimitse Iwo. "Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingakhoze kuulaka Iwo." Choonadi choululidwa, Mwauzimu!

239 Tsopano penyani tsopano motsatira, Iye akuti, "Ndipo iwe ndiwe Simoni, ndipo ine ndipereka kwa iwe," chifukwa iye anali nacho Choonadi choululidwa, mwauzimu. Ndi chifukwa chake iye anadziwa kusiyana kwa pakati pa Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, ndi Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Iye anali nalo vumbulutso lauzimu. Ndi chimene inu mukumvetsera usikuuno, pamene Mzimu Woyera ukutsegulira izo kwa ife.

240 Iye anati, “Iwe ndiwe Simoni, ndipo ine ndikupatsa iwe mafungulo aku Ufumu wa Kumwamba. Ndipo chirichonse chimene iwe udzamanga padziko lapansi ili, Ine ndidzachimanga icho Kumwamba. Chirichonse chimene iwe uchimasula pa dziko lapansi ili, Ine ndidzachimasula icho Kumwamba.” Kodi Iye ananena zimenezo? Mateyu Woyera, mutu wa 16, “Chirichonse chimene iwe uchimanga pa dziko lapansi, Ine ndidzachimanga Kumwamba. Chirichonse uchimasula pa dziko lapansi, Ine ndidzachimasula Kumwamba. Ndipo Ine ndikupatsa iwe mafungulo aku” (chiyani?) “Ufumu wa Kumwamba.” Kodi Ufumu wa Kumwamba ndi chiyani? Mzimu Woyera! Baibulo linati, “Ufumu wa Kumwamba uli mkati mwanu . . .” Ine ndikutanthauza, “Ufumu wa Mulungu,” mundikhululukire ine. “Ufumu uli mkati mwanu.”

241 Tsopano Iye anati, “Ena aima pano omwe sadzawona imfa mpaka iwo atawona Ufumu wa Mulungu ukudza mwa mphamvu.” Masiku pang’ono okha mtsogolomo, Pentekoste. Mukuona? “Ena aima pano,” mu mzere uwo womwe . . . chinthu chimene Iye anali kuchinena. “Ena a inu mwaima pano,” Iye anali atawalitsidwa, anati, “simudzawona imfa mpaka inu mutawona Ufumu wa Mulungu ukudza mwa mphamvu.”

242 Baibulo linati, “Ufumu uli mkati mwanumo.” Pamene Yesu anauka kwa akufa, kumbukirani, Iye anali nawo pambali Pake mafungulo a imfa ndi hade, osati mafungulo aku Ufumu, awo anaperekedwa kwa Mpingo. Tsopano, Petro anali nawo mafungulowo. Kodi inu mukukhulupirira Yesu akanakhoza kusunga Mawu Ake? Ngati Iye satero, m’bale, Iye sanali Mulungu! Ndizo zonse. Tsopano, Iye anati, “Petro, ine ndikukupatsa iwe mafungulo aku Ufumu,” mwa kulankhula kwina, “a Mzimu Woyera. Chirichonse chimene iwe umanga padziko lapansi, Ine ndichimanga Kumwamba.”

243 Tsopano taonani kulakwitsa kumene iwo anapanga, kupita uko ndi kumakakhululukira machimo, ndi zina zotero monga choncho. Kulakwitsa kwakeko! Tiyeni tiwone. Iwo anaika mafungulo pa iye. Tsopano, Iye analozetsa nkhope yake molunjika kumene ku Pente- . . . kapena molunjika kumene kupita ku Yerusalemu.

244 Iye anapachikidwa, anafa, anauka tsiku lachitatu, anali pa dziko lapansi masiku forte pakati pa anthu, anakwera kupita Kumwamba. Anawauza iwo kuti akadikirire mpaka iwo atawuona Ufumu wa Mulungu ukudza pa iwo, pa nthawi iyi Atate adzabwezeretsa Ufumu mwamaonekedwe auzimu kwa iwo. Iwo anapita ku mzinda wa Yerusalemu ndipo anakadikirira kumeneko kwa masiku khumi ndi usiku, ndipo, zonse mwadzidzidzi, ubatizo wa Mzimu Woyera, Ufumu wa Mulungu, unadza ndi mphamvu pa iwo. Nkulondola uko?

245 Tsopano penyani! Petro, wosaphunzira, sankakhoza

ngakhale kulemba dzina lake lomwe (papa? Eya, papa), anaima pa bokosi la sopo kapena chinachake ndipo anayamba kulalikira. Iye anati, "Inu anthu aku Yudea ndi inu okhala mu Yerusalemu, mulole ichi chidziwike kwa inu, ndipo mumvetsere kwa Mawu anga. Awa sanaledzere monga inu mukuganizira kuti ali, powona kuti ili ndi ora lachitatu la tsiku, koma ichi ndi chija chomwe chinayankhulidwa ndi mneneri Yoweli. 'Zidzafika pochitika mu masiku otsiriza,' akutero Mulungu, 'Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse. Ana anu aamuna ndi aakazi azidzanenera, ndi pa adzakadzi Anga ndi antchito aakazi Ine ndidzatsanulirapo Mzimu Wanga ndipo iwo azidzanenera. Ine ndizidzasonyeza zodabwitsa mmiyamba kumwamba; ndi pa dziko kupansi, moto, malawi a moto, ndi nthuzi za utsi.'" Mopitirira iye anapita nazo, ndi kuyankhula za Davide ndi ena otero. Ndipo pamene otsutsa awa anaima apo . . .

246 Anati ndiye, "Amuna ndi abale, ife tingachite chiyani kuti tipulumutsidwe?"

247 "O, samalira, Petro, iwe uli nawo mafungulo akulendewera apo tsopano." Ndi kulondola uko? Uthenga wosandulika thupi woyambirira!

248 Yesu, masiku pang'ono izo zisanachitike, Iye asanapachikidwe, anati, "Petro, Ine ndikukupatsa iwe mafungulo. Chirichonse chimene iwe uchimanga, Ine ndichimanga icho; chirichonse chimene iwe uchimasula, Ine ndichimasula icho. Tsopano, chirichonse chimene iwe uchita, Ine ndizichizindikira icho Kumwamba." Ngati Iye ali Munthu wa Mawu Ake, Iye azisunga Mawu Ake!

249 Ndipo apa iye waima apa, Mzimu Woyera unali utagwa kwa nthawi Yake yoyamba, ndipo Petro anafunsidwa, "Kodi tingachite chiyani kuti tipulumutsidwe?"

250 "Samalira apo, iwe ukulowetsa fungulo mu Ufumu kwa nthawi yoyamba. Yesu anakuuza iwe, masiku angapo apitawo, masiku khumi apitawo, anati, 'Pitani muzikawabatiza anthu mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.' Kodi iwe uchita chiyani? Koma Iye anakupatsa iwe mafungulo chifukwa iwe unali ndi vumbulutso lauzimu! 'Pamene Mpingo Wanga uti udzamangidwirepo, ndipo zipata za gehena sizidzakhoza kuulaka Iwo.'"

251 Ndipo tengani tizikhulupiriro tanu ndi mbalume, ndi chirichonse chimene ine mukukhumba kuchitenga, koma izo zidzalephera momvetsa chisoni (izo zakhala zikutero), koma mphamvu ya Mulungu wamoyo izisunthirabe chitsogolo, mpaka mu Muyaya. Monga kukhudza kwa rediamu, Iye amapitirirabe kuyenderera, zindikirani, mopanda kutha.

252 "Petro, iwe uli nawo mafungulo. Chirichonse chimene uti uchichite kuno, Mulungu ayenera kuti azichizindikira icho

Kumwamba." Ndi kulondola uko? "Kodi iwe ukuti chiyani, Petro? Kodi ife tichite chiyani kuti tipulumutsidwe?"

253 Petro anati...Musati muzipita mukumati, "*Tikuoneni Maria*," palibepo chinthu choterocho, kuchita *novena*. Musati muzibwera ndi kumadzagwirana chanza ndi kuika dzina lanu pa bukhu la mpingo ndi kuwalola iwo kuti akonkhe madzi pa inu; palibe chinthu choterocho. Iyo ndi mbalume ya Chikatolika imene mpingo wa Chiprotestanti ukugwadirako.

254 Iye sananene, "Nonse inu kazipitani...Tsopano, Yesu anandiuza ine, masiku pang'ono apitawo, kuti nonse inu mupite ndi kukabatizidwa mu dzina la 'Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.'" Osati munthu yemwe anali nalo vumbulutso lauzimu, sakananena zimenezo.

255 Iye anati, "Lapani, aliyense wa inu, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mulandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo omwe ali kutali kwambiri, ndi ngakhale kwa onse omwe Ambuye Mulungu wathu ati adzawaitane." Ndi zimenezotu. Ndiye fungulo linalowa mkati ndipo ilo linatseka, ilo linatseka Kumwamba!

256 Ndi chifukwa chake Paulo ananena kwa ophunzira a Yohane, "Inu muyenera kuti mubatizidwenso kachiwiri, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti mulandire ubatizo wa Mzimu Woyera."

257 Inu simumadziwa Izo kale, inu mwazidziwa Izo tsopano! Aha! Zonse ziri bwino. Izo ziri ndi inu. Izo nzoona. Koma autatu achikunja, ubatizo wautatu sunazindikiridwe konse mu Mpingo, Chipangano Chatsopano; mu mpingo wa Katolika wokha, ndipo mpingo wa Chiprotestanti umagwadira kwa izo. Penyani! Anthu ambiri angagwe kwa iwe chifukwa cha izo. Koma, m'bale, inu muyenera kuti mupange kusankha kwanu.

258 Tsopano inu mukuti, "M'bale Branham, ine ndinabatizidwa mu dzina la 'Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.' Ine ndiri nawo ubatizo wa Mzimu Woyera."

259 Ine sindikuwakaika mawu anu. Ine ndiribe chifukwa nkomwe kuti ndiwakaikire mawu anu; ine ndikuwakhulupirira iwo. Ine ndikukhulupirira Mulungu anawapatsa iwo Mzimu Woyera, kujaku iwo asanabatizidwe nkomwe; koma pamene Petro anawauza iwo zoti akachite, iwo anapita ndipo anakazichita izo. Ndiko kulondola. Tsopano inu mukudziwa zoti muzichita, ndiko kulondola; ndipo ngati inu mukana kuti muyende mu Kuwala pamene Kuwala kwabweretsedwa, inu mupita ku mdima. Kulondola! Ameni! Chabwino. Ndikhululukireni ine. Ine sindikufuna kuti mundikhululukire ine chifukwa chofuula "zikhale chomwecho" kwa Mawu a Mulungu. Ayi, bwana. Ine ndifuula "ameni" kachiwiri. Ndiko kulondola. Inde, bwana.

Chifukwa chiyani mumabatiza mu Dzina la Yesu Khristu, M'bale Branham? Chifukwa chiyani inu mumachita izo mmalo mwa "Atate, Mwana, Mzimu Woyera"? Chifukwa Baibulo limaphunzitsa zimenezo! Zamveka izo?

Chifukwa chiyani inu mumatsuka mapazi, M'bale Branham? Chifukwa Baibulo limaphunzitsa zimenezo. Ine ndimakhulupirira mu Uthenga wathunthu. Chabwino, tsopano.

Kodi ubatizo wabodzawo ndi uti umene inu mumaunena? Ndi umenewo. Ndiwo ndendende iwo. Palibe paliponse. . . Kawerengeni mobwereza mu Chipangano ndi kukapeza pamene munthu mmodzi. . .

260 Tsopano kwa inu anthu okondedwa, ine sindikupweteketsa kumverera kwanu, ine sindikufuna kuti nditero. Ine ndikukufunsani inu kuti mukhale odzichepetsa ndipo osati. . . Muchiyang'ane chinthu ichi mu nkhope, ndi kuwona momwe icho chikuwonekera. Chiyang'aneni icho mu nkhope ya Baibulo, osati mu mpingo wanu kapena chinthu china chopusa, chopepera chomwe winawake ali nacho modzikweza mmutu mwake, koma yang'anani pa Mawu a Mulungu. Zedi!

261 Kodi inu mukuganiza kuti Mulungu Wamphamvuzonse angandipatse ine utumiki womwe Iye ali nawo panowu monga chonchi, wokhala ndi zizindikiro zauzimu ndi zinthu zomwe sizinayambe zakhalapo chiyambireni cha Chipangano Chatsopano, ndi kundilola ine kuti ndiziyenda mu kulakwitsa monga choncho? Ndithudi ayi! Ndipo, m'bale, pamene ine ndidzabwerera kuchokera kutsidya kwa nyanja, ine ndidzaika gawo lalikulu la nthawi yanga osati pa machiritso Auzimu ndi zozizwitsa koma kulalikira Mawu a Mulungu. Ndizo ndendende kulondola. Zoona. Tsopano tiyeni tiwone.

38. Kodi mpingo uno umaphunzitsa kuti iwe umayenera kuti uyankhule mu malirime kuti ulandire Mzimu Woyera?

262 Ayi, bwana. Ayi, ife sitimatero. Kuyankhula mu malirime ndi mphatso ya Mzimu Woyera, mwaona, osati Mzimu Woyera. Ndi mphatso. Mtengo uwu umabala mitundu naini ya chipatso. Ndi kulondola uko?

263 Ngati inu muyang'ana pa mtengo wa apulo, ukakhala ndi maapulo, inu mumati ndi mtengo wa apulo. Mukayang'ana pa mtengo, womwe uli ndi mapeyala, inu mumati iwo ndi mtengo wa mapeyala. Ziribe kanthu ngakhale iwo utakhala ndi khungwa la nkhuyu pa iwo, ndipo iwo nkukhala ndi mapeyala pa iwo, moyo wa iwo ndi chiyani? Moyo wa iwo ndi moyo wa mtengo wa peyala. Ndi kulondola uko?

264 Tsopano, Mtengo wa Mulungu uwu umabala zipatso zauzimu naini. Nkulondola uko? Chabwino. Apo pali zosiyana zonse. . . Anati, "Wina anapatsidwa kuti aziphunzitsa-. . . chidziwitso, nzeru, kumvetsa, ndi kuyankhula mu malirime, kutanthauzira

kwa malirime," mphatso naini zosiyana zauzimu zimamera pa Mtengo uwu wa Mulungu. Nkulondola uko? Chabwino, tsopano, kungoyankhula mu malirime si chimodzi chokhacho, mulinso zina, umo.

265 Tsopano inu mukhoza kuyankhula ndi malirime ndipo nkusakhalabe nawo Mzimu Woyera. Tsopano, muzingokumbukira zimenezo. Ine ndakhala ndiri kumene . . . Ine ndawonapo afiti aakazi ndi aamuna akubwera akuyankhula mu malirime, ndipo iwo alibe Mzimu Woyera. Inu mukudziwa, ine ndawaonapo iwo akubwera akufuula ndi kumalumpha, ndipo iwo alibe Mzimu Woyera. Ine ndinaima mu kuvina kwa chimanga kuno osati kale litali, uko . . . ndi kumtunda pang'ono kuchokera ku Douglas, Arizona, kumtunda uko. Ndinawona kuvina kwa chimanga uko pamene iwo anali nako uko, ndipo mfiti iyo inabwera uko ndipo inatengeka moipa, ndi chirichonse, anatengeka ndi kumaponyera madothi pa iye kumeneko. Izo sizinkatanthauza kuti iye anali wopulumutsidwa. Munthuyo anali—msing'anga.

266 Ine ndinaima mu India . . . mu Afrika ndipo ndinawona asing'anga akubwera ndi kudzapikisana nane monga choncho, ndi matsenga awo, ndipo ngakhale ankamwa magazi kuchokera mu chigaza cha munthu. Ndiko kulondola. Iwe umayera kuti uzidziwa zomwe iwe ukuziyankhula pamene iwe ukumana nazo izo. Koma ine ndaiwona mphamvu ya Mulungu Wamphavuzonse ikumumanga bambo ameneyo mpaka iye sanakhoze kusuntha. Kotero ndiye, maso ake analenguka monga choncho, ndipo iwo anamunyamula iye kumuchotsapo. Inde, bwana.

267 M'bale, Mulungu ndi weniweni! Ndiko kulondola. Koma Mulungu ndi Mzimu, osati kungodzikanikizira ku kuyankhula mu malirime, kapena *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*. Ine ndikunena kuti munthu aliyense yemwe ali . . . Ndiro vuto mu mpingo kuno. Mwaona, inu . . . Achipentekoste anapenga pa chinthu chimodzi icho. Iwo apita kwa anthu . . . Mmalo mo—moyika manja pa iwo, ndi iwo kumalandira Mzimu Woyera, iwo amawafikitsa iwo apo paguwa ndikuyamba kumawamenya iwo pa nsana ndi kumafuula, "Yankhulani iwo! Yankhulani iwo! Yankhulani iwo!" Ndi kumanena mawu mobwereza bwereza, mpaka iwo amakhala ndi chisokonezeko ndipo osati malirime.

268 Ngati munthu wa Mzimu Woyera weniweni abadwa mwa Mzimu wa Mulungu, iye azikhala moyo waumulungu. Ena a amuna awo amakhala miyoyo yoipa, ndipo inu mumadziwa izo, ndipo zipatso zawo zimatsimikizira kuti iwo sanali. Yesu anati, "Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo." Ndipo chipatso cha Mzimu si kuyankhula mu malirime, iyo ndi mphatso ya Mzimu.

269 Petro sanati konse, "Lapani, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, inu mudzalandira Mzimu Woyera." Iye anati, "Inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera," pamene iwo anamva

malirime awa ndi anthu akuyankhula. Ndi imodzi ya mphatso za Mzimu Woyera yomwe iwo amalandira. Ameni. Chabwino. Ndiyenera ndifulumire.

39. Ine ndiri ndi anyamata awiri (wani, thuu; ndi wina, faivi), ndipo iwo anakonkhedwa. Kodi iwo ayenera kuti abatizidwe mwa kumizidwa?

270 Chabwino tsopano mlongo kapena m'bale, yense yemwe inu muli, izo ziri kwa inu. Ine ndiri naye msungwana wamng'ono . . . Mnyamata wanga wamng'ono, Billy Paul, anali usinkhu wa zaka sikisitini, ndipo ine ndinamubatiza iye mu Dzina la Ambuye Yesu pomwe pano. Msungwana wanga wamng'ono anali usinkhu wa zaka eyiti. Iye anabwera kwa ine ndipo anadzakhala mmanja mwanga, ndipo iye anati, "Adadi, ine ndikufuna kuti ndikhulupirire pa Ambuye Yesu Khristu, ndipo i—ine ndikufuna kuti ndibatizidwe." Ndipo ine ndinamubatiza msungwana wamng'onoyo ali eyiti. Pamene, ngati ana aang'ono awo akufuna kuti abatizidwe, abatizeni iwo. Ngati iwo siali, bwanji, ngati iwo ali . . . ingopitirirani, izo ziri ndi inu, chirichonse chimene Ambuye atanene.

40. Kodi ndi okhawo omwe ali ndi ubatizo wa Mzimu Woyera ati adzakhale mu Mkwatulo wa Mpingo, kapena kodi ndi okhulupirira onse ati adzasonyezedwe?

271 Ife sitiri . . . ife tiribe nthawi yoti tizilungamitse zimenezo. Koma, m'bale, Mkwatibwi wa Mzimu Woyera yekha ndi yemwe adzakhalepo mu Mkwatulo. Mukuona? Baibulo . . . ? . . . enawo sadzakhala otaika.

272 Penyani! N'ndani ati adzaweruze dziko lapansi? Oyera. Daniele anati, "Ine ndinamuwona Iye, akubwera kwa Wanthawi Zamakedzana, ndi—ndipo Iye anadza ndi zikwi khumi kuchulukitsa zikwi khumi za Oyera Ake." Nkulondola uko? Mkwatulo, Mpingo unali utapita kale. Ndiye iwo anabwera pansi, ndipo Chiweruzo chinayambika.

273 Ndipo Mabuku anatsegulidwa. Nkulondola uko? Ndipo Bukhu lina linatsegulidwa, lomwe linali Bukhu la Moyo, wokhulupirira woyeretsedwa yemwe anali asanalandile Mzimu Woyera.

274 Kodi Yesu sanaphunzitse kuti anamwali khumi anapita kuti akakomane ndi Mkwati? Ndipo asanu a iwo . . . kapena onse a iwo anali anamwali, angwiro, oyera. Ndipo iwo, *awa*, anayamba kugona ndipo sanalandire Mzimu Woyera; ndipo *awa* anali ndi Mzimu Woyera ndipo anali ndi Mafuta mu nyali yawo. Ndipo pamene Mkwati anadza, Liwu linadza, likufuula, iwo anati, "O, tiyeni ife tizipita. Tipatseniko ife ena a Mafuta anu!"

275 Iye anati, "Pitani kwa iwo omwe akugula, kapemphereni, kalandireni Iwo tsopano." Koma iwo sanakhoze. Ndipo pamene iwo anali atapita, a—anamwali anakalowa mu Mgonero wa Chikwati, ndipo iwo anakaponyedwa ku mdima wakunja,

kumene iwo anali kulira ndi kusisima ndi kukukuta kwa mano. Kodi Chivumbulutso, usiku watha, mu mutu wa 12, usiku wa dzana, sanaphunzitse kuti chinjoka chofiira chinalavula madzi kuchokera mkamwa mwake kuti chipange nkhondo ndi *otsalira a* Mbewu ya mkazi, omwe anali ndi chikhulupiriro mwa Mulungu ndipo ankasunga malamulo a Yesu Khristu?

276 Kwa inu akazi, pamene inu mumayala pansi patani. Ndi chidutswa chabwino cha nsalu, nsalu yomweyo apo, koma inu mumatenga monga *chonchi* ndi kuyala patani yanu basi momwe inu muti muidulire iyo. Ndiyeno inu mumaidula iyo. Izo ziri kwa inu. Koma inu mumatenga nsalu yomwe inu mwaidula, kuti mupange chovala chanu kuchokera pa iyo, ndipo ina yonseyo imagwiritsidwa ntchito. Iyo imakhala nsalu yabwino basi monga yonse iyo, koma mwa kusankha inu mwasankha *iyo*. Ndi kulondola uko? Yonse iyo ndi yoyera basi ndi yabwino basi, ndipo yodula basi monga yonse inayo, koma uko kunali kusankha kwanu.

277 Ndipo Mulungu walonjeza kuti ife tikupita mu Mkwatulo mwa kusankhidwa! Ndipo Baibulo linati, "Ndipo akufa ena onsewo sanakhalenso moyo kwa zaka chikwi chimodzi." Nkulondola uko? Kotero kokha . . . Inu simudzataika, koma Mkwatibwi wodzazidwa ndi Mzimu Woyera adzapita mu Mkwatulo. Ena onse a iwo adzabwera nadutsa mu Chiweruzo; pamene Awo sanatero.

41. Ngati iwe umayenera kuti ubatizidwe mu Dzina la Yesu, nchifukwa chiyani Yesu anati mu Mateyu 28, "Muzibatizidwa mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera"? Ndi lomwe ine ndangolitsiriza kulifotokoza, limenelo.

278 Chabwino, kodi inu mukuyamba kutopa? Ine ndikudziwa inu muli.

42. Koma kodi Mulungu samalemekeza ubatizo wa "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera"? Kodi palibe anthu amene akubatizidwa mu dzina, mu maina awa, analandira Mzimu Woyera? Kodi Yesu anabwera kuti adzawapatse ulemerero Atate? Kodi ubatizo uwu sungati uzizindikiridwa?

279 Inde, Yesu anabwera kudzawapatsa ulemerero Atate. Tayang'anani mu Yohane Woyera mutu wa 14. Ine ndiri pafupi . . . ine ndiyenera . . . Ngati inu mungodikirira pafupi atatu ena, ife tikhala titatsiriza izo, ine ndikukhulupirira. Tayang'anani, ndiye ife tidzatenga enawo mwatsopano mawa, ndiye, chifukwa ine ndipezadi ena atabwerera usikuuno, ine ndikukhulupirira. Zindikirani, uno ndi mpingo, ngakhalebe, uwu. Ife tikupitirira nazo.

280 Yang'anani, Yesu anabwera kuti adzawonetsere Atate. Penyani, pachiyambi, Mulungu anapanga munthu mu chifanizo Chake Chomwe. Ndi kulondola uko? Chabwino, kodi Mulungu

ndi chiyani? Mzimu. Yohane Woyera mutu wa 4, Yesu akuyankhula kwa mkazi pa chitsime, Iye anati, "Mulungu ndi Mzimu ndipo iwo amene amupembedza Iye ayenera azimupembedza Iye mu Mzimu ndi Choonadi." Nkulondola uko? Ngati Mulungu anamupanga munthu mu chifanizo Chake Chomwe, ndi munthu wa mtundu wanji yemwe Iye anamupanga ndiye? Munthu wamzimu.

281 Mu Genesis 2, panalibe munthu woti azilima mu nthaka, ndipo Mulungu anapanga munthu kuchokera mu fumbi la pa dziko lapansi; osati mu chifanizo Chake, koma mu chifanizo cha moyo wachinyama. Ndipo Iye anauyika mzimu wa munthuwo mwa chinyama ichi apa, ndipo iye anadzakhala solo yamoyo. Tsopano, uko ndi kusiyana pakati pa munthu ndi chinyama.

Nyama siimamanga magalimoto, ndipo iyo siimachita zinthu monga zothandizira kukhala moyo kwake, ndi zina zotero monga choncho. Iyeyo ndi chinyama, chakuthengo chosayankhula. Icho chiribe solo. Icho sichingakhoze kuwerenga ndi kulemba. Icho sichingakhoze kuyankhula, kunena. Icho ndi chakuthengo chosayankhula.

Koma munthu ali mu mnofu ngati chakuthengo, koma iye ali ndi solo ya Mulungu mkati mwake, yomwe imamupangitsa iye kukhala wachisavundi. Ndipo iye akhoza kuyambitsa . . . Taonani zomwe iye amakhoza kuchita! Iye ali, pafupifupi wofanana ndi Mulungu, chifukwa iye ndi mwana wa Mulungu ngakhale mu chikhalidwe chake chakugwacho. Iye ndi wodabwitsa! Tayang'anani pa iye! Mukuona? Nzomwe ziri.

282 Ndiye pamene munthu anagwa mu thupi . . . Ndipo ngati Mulungu akanatuma munthu wina pambali pa Iyemwini pansipa, Iye akanakhala kuti sanachite chilungamo. Njira yokha yomwe Mulungu akanachitira izo molungama inali potenga malo a munthuyo mwiniwake.

283 Bwanji ngati ine ndikanamupangitsa M'bale Neville kuti amufere mkazi *uyu* apa? Bwanji ngati ine ndikanamupangitsa mkazi *uyu* kuti amufere mkazi *uyu* apa, ngati izo zikanakhala choncho ine ndikadakhala ndi ulamuliro pa inu? Ine sindikanakhoza kukhala wolungama ndi kumachita zimenezo. Ngati ine ndinena kuti pakhale imfa, ndipo nkufuna kuti inu mukhale moyo, ine ndiyenera kuti nditenge malo anu kuti ndikulungamitseni inu.

284 Ndiyeno Mulungu, Yemwe anali mu chifanizo cha Mzimu . . . mopanda chifanizo, kani. Baibulo likuti, "Mulungu anali wopanda mawonekedwe." Chabwino. Ndiye Mulungu anachita kutenga mawonekedwe ena, ndipo Iye anamufungatira namwali ndipo analenga mwa iye khungu la magazi, popanda kugonana kapena chirichonse chochita nazo izo, ndipo analenga mkati mwakemo khungu la magazi lomwe linakula nkudzakhala Mwana wa Mulungu. Ndipo Mulungu anabwera pansi ndipo

anadzakhala mwa Mwana Wake, Khristu Yesu, kumupanga Iye kukhala Mulungu pa dziko lapansi.

285 Pamene, Yohane Woyera . . . Tomasi anati, "Ambuye, tisonyezeni ife Atate, ndipo icho chitikwanira ife."

286 Iye anati "Ine ndakhala motalika chotere ndi inu ndipo inu simukundidziwa Ine?" Iye anati, "Iwe ukunena bwanji, 'Tiwonetseni ife Atate'?" Bwanji, Iye anati, "Pamene inu mukundiwona Ine inu mukuwawona Atate. Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi. Atate anga akukhala mkati mwa Ine."

287 Dona kuno si kale litali, ine ndinali kuyankhula uko, analumpha apo, anati, "O, M'bale Branham," anati, "Ine ndikudziwa chomwe inu mukutanthauza. Iwo ndi amodzi, zedi iwo ndi amodzi." Anati, "Inu ndi akazi anu ndinu amodzi, inunso. Ndiwo mtundu wa umodzi womwe iwo ali."

288 Ine ndinati, "Ine ndikupempha chikhululukiro chanu," ine ndinati, "iwo siali." Ine ndinati, "Kodi inu mukundiwona ine?"

Anati, "Zedi."

Ine ndinati, "Inu mukuwawona akazi anga?"

Anati, "Ayi."

289 Ine ndinati, "Pamenepotu! Ndiye uwo ndi mu mtundu wosiyana wa umodzi kuposa chimene ine ndi mkazi wanga tiri." Mukuona? Ine ndinati, "Uko nkulondola."

290 Yesu anati, "Inu simungakhoze kundiwona Ine popanda kuwaona Atate." Ndithudi ayi! Ndi gawo lachiwiri la muyezo wa mapazi-atatu, muyezo womwewo. Ndi Mulungu. Yesu Khristu anali mwina Mulungu kapena wonyenga wamkulu kwambiri yemwe dziko linayamba lakhalapo naye.

291 Mvetserani! Mkazi anati kwa ine si kale kwambiri, anati, "Ine nditsimikizira kwa inu," mkazi wa Christian Science. Tsopano, mzanga wa Christian Science, khala molemekeza miniti yokha, mwaona. Iwo anati, "Ine nditsimikizira kwa inu kuti Iye sanali kanthu koma munthu." Anati, "Inu mumaika kubwekerera kochuluka kwambiri pa Yesu."

292 Ine ndinati, "Ngati ine nditamabwekerera usana ndi usiku ine sindingakhoze kumupatsa Iye zomwe zimayenera kwa Iye." Ine ndinati, "Palibe zodabwitsa . . . "

293 Chifukwa, Yesaya anayesera kumutcha Iye, iye anati, "Iye ndi Wodabwitsa, Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha." Zonse izo! "Iye ndi Alpha, Omega, Chiyambi ndi Mapeto, Muzu ndi Mphukira ya Davide, Nyenyezi Yowala ndi Yammawa; Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." "Mwa Iye munali chidzalo cha Umulungu mu thupi," linatero Baibulo. Chidzalo cha Mulungu chinali mwa Iye!

294 Iye anati, “Ine ndikuuzani inu, pamene Iye anapita kuti akamupempherere Lazaro, kuti akamudzutse Lazaro,” anati, “Ine nditsimikizira kwa inu kuti Iye anali munthu chabe.”

295 Ine ndinati, “Tiyeni tikuwoneni inu mukuchita izo!”

296 Anati, “Baibulo linati, ‘Iye analira.’ Ndipo izo zikutsimikizira kuti Iye anali munthu, Iye ankakhoza kulira.”

297 Ine ndinati, “Zedi, uyo anali Mwana yemwe anali kulirayo.”

298 Iye anali Mulungu-munthu. Iye anali chinthu chapatatu chimodzimodzi monga ine ndiriri, inu muliri; ife ndife solo, thupi, ndi mzimu. Iye anali Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, mu Umulungu wa Mulungu; ndi Chomwe Iye anali. Iye anali Umulungu Iwoweni! Iye akanakhoza bwanji kuchita china chirichonse apo pamene...Ana Ake omwe akulirira magazi Ake? Ngati zikanakhala chinachake...Awo anali ana Ake Omwe akulirira magazi Ake; palibe zodabwitsa Iye anawalirira iwo. Munthu angatani...ndi ana Ake omwe akulirira magazi Ake, Iye akanamverera chotani? Mwina kuwaweruzira iwo ku gehena kwanthawizonse, kapena kupereka moyo Wake; Iye anali Mulungu akupereka moyo Wake chifukwa cha ana Ake! Umulungu unkakhala mwa Iye! Ndi Chomwe Iye anali.

299 Mkazi anati, “Yang’anani,” anati, “Abusa a Branham, ine nditsimikizira kwa inu! Pamene Iye analira, izo zinatsimikizira kuti Iye anali munthu.”

300 Ine ndinati, “Dona, Iye anali munthu pamene Iye anali kupemphera-...kapena pamene Iye anali kulira, uko nkulondola. Iye anali munthu pamene Iye anali kulira, koma pamene Iye anawongola thupi lake lofookalo nanena kwa munthu yemwe anali atafa kwa masiku anai, ‘Lazaro, tulukamo!’ Ndipo munthu yemwe anali atafa kwa masiku anai, ndipo atavunda, ndi nyongolosi zamkhungu zikukwawa pa iye, chivundi chinamudziwa Mbuye wake ndipo solo inamudziwa Mlengi wake, ndipo munthu yemwe anali atafa masiku anai anaima pa mapazi ake ndipo anakhalanso moyo! Uyo anali woposa munthu!”

301 Iye anali munthu pamene Iye ankatsika kuchokera pa phiri usiku uja, wanjala, akuyang’anayang’ana mu mtengo chinachake choti angadye. Iye anali munthu pamene Iye anali kuyang’ana chinachake apo choti adye pa mtengo wa mkuyu uwo. Koma pamene Iye anatenga mabisiketi asanu ndi nthuli ziwiri za nsomba nadyetsa zikwi zisanu, uyo anali woposa munthu! Uyo anali Mulungu pamenepo! Mlengi mmodzi Yemwe ankakhoza kutenga nsomba yophikidwa ndi kuinyema iyo ndipo iyo inali yophikidwabe, anatenga mkate wophikidwa ndi kuwunyema iwo; kodi ndi mtundu wanji wa atomu womwe Iye anawumasula? Aleluya! Iye anali Mulungu, Mlengi wa maatomu ndi zinthu zonse! Uyo anali woposa munthu!

302 Iye anali munthu pamene Iye anali kunja kuja mu bwato lija usiku uja, pambuyo pa kulalikira tsiku lonse ndi kuchiza odwala, atatopa kwambiri, mpaka adierekezi zikwi khumi a mu nyanja analumbira kuti akanamumiza Iye. Bwato laling'ono lija kumeneko, likunjanja apo ngati chivinikiro cha botolo, mafunde aakulu akudumphira ku malo ndi malo, ndipo Iye atagona, atatopa kwambiri mpaka mafunde sanamudzutse Iye. Adierekezi anali akubangula, akuti, "Ife timupezeketsa Iye tsopano pamene Iye ali mtulo." Koma pamene Iye anadzuka, atadzuka apo, Iye anali munthu, Iye anali atatopa kwambiri. Koma pamene Iye anaika phazi Lake pa milomo ya ngalawayo, anayang'ana panja ndipo anati, "Khala bata!" ndipo mphepo ndi mafunde zinamumvera Iye. Uyo anali woposa munthu! Ameneyo anali Mulungu, Mlengi Yemwe anapanga Miyamba.

303 Nzosadabwitsa atumwi anati, "Ndi munthu wa mtundu wanji yemwe uyu ali woti ngakhale mphepo ndi mafunde zimamumvera Iye!"

304 Uyo anali woposa munthu. Ameneyo anali Mulungu. Iye anali munthu pamene Iye anakhomeredwa pa mtanda ngati Nsembe, kuti alichotse tchimo. Iye anali munthu ali ndi misomali yokhomeredwa mu dzanja Lake. Iye anali munthu ali ndi minga pa mutu Wake. Iye anali munthu ali ndi malovu a asilikari onyoza pa Iye. Iye anali munthu ali wotunduzidwa, wovulidwa, ndi wovulazidwa. Iye anali munthu! Iye anali munthu pamene Iye ankalira, "Mulungu Wanga, chifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine?" Iye anali munthu akulirira thandizo. Koma pa mmawa wa Chiukitsiro pamene zisindikizo za imfa zinamasulidwa pa manda paja, amene uja anali woposa, munthu! Iye anatsimikizira kuti Iye anali Mulungu.

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine; pakufa,
Iye anandipulumutsa ine;
Ataikidwa, Iye anandinyamulira machimo
anga kutali kwambiri;
Powuka, Iye anandilungamitsa mwaulere
kwanthawizonse:
Tsiku lina Iye akubwera, O tsiku
laulemererolo!

O, pakati pa miyala ikusweka ndi mlengalenga
mukuchita mdima,
Mpulumutsi wanga anaweramitsa mutu Wake
ndipo anafa;
Chotchinga chotseguka chinaulula njira
Ku chisangalalo cha Kumwamba ndi tsiku
losatha.

305 Nzosadabwitsa kuti Eddie Perronet anafuula:

Onse yamikani mphamvu ya Dzina la Yesu!
Lolani angelo agwe modzilambatitsa;

Bweretsanipo nduwira yachifumu,
Ndi kumuveka Iye akhale Ambuye wa onse.

306 Uyo ndi Munthu wamkulu uja, Ambuye Yesu. Iye anali Yehova, Mulungu ataphimbidwa mu mnofu. Baibulo linati, "Chirichonse chimene inu mungachite mu mawu kapena mu ntchito, muzichita izo zonse mu Dzina Lake." Baibulo linati, "Banja lonse Kumwamba limatchedwa 'Yesu,' ndipo banja lonse pa dziko lapansi limatchedwa 'Yesu.'" Tiyeni tizipemphera mu Dzina Lake, tizikhala moyo mu Dzina Lake, kuphunzitsa mu Dzina Lake, kufa mu Dzina Lake, kuikidwa mmanda mu Dzina Lake, kubatizidwa mu Dzina Lake, kuukitsidwa mu Dzina Lake, kupita Kumwamba mu Dzina Lake. Ilo ndi Dzina Lake, ndipo Mkwatibwi Wake amatchedwa "Abiti Yesu." Izo ziwatenga anthu kuchokera mwa Amitundu, akhale a Dzina Lake.

307 Ndipo ine sindine waumodzi. Ayi, bwana. Inu anthu autatu zichotseni izo kwa inu. Ine si waumodzi. Ayi, bwana. Ine si waumodzi, ngakhale wautatu. Ine ndimakhulupirira zomwe Baibulo limanena. Ndimo mwakukhoza. Ameni. Psyfuu! Ine ndakhalitsa kwambiri pa limodzi. Kodi ilo linali chiyani? Kodi ine ndinalitulutsa ilo? Kapena, tiyeni tiwone, kodi linali ilo? O, inde, uko nkulondola, za . . . momwe Atate anali mwa Khristu. Iye anali munthu, Iye anali Mulungu-munthu.

43. Kodi mpingo wa Chipentekoste sumabatiza mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera? Ena a iwo.

44. Ngati munthu afa wopanda ubatizo wa Mzimu Woyera, kodi iye adzataika?

308 Ayi, bwana. Ngati iye ali wokhulupirira, iye adzabwera mu chiukitsiro, chiukitsiro chachiwiri. Iye akakhala nawo ubatizowo, iye adzapita mu chiukitsiro choyamba. Tsopano, inu muyenera kuti mutenge mawu anga. Ngati izo sizikukukhutitsani, ndiye—inu mundifunse ine, ine ndikupatsani inu Lembalo. Chifukwa, ine ndikuyesera kuti nditenge awiri kapena atatu owonjezera pano, ndiye ife titsiriza.

45. M'bale Bill, kodi Baibulo limanena chirichonse za njuga?

309 Inde, Ilo limanena, koma ine sindingakhoze kupakumbukira apo pakali pano. Ine ndikudziwa asilikari anachitira maula pa zovala Zake, ndi zina zotero monga choncho, koma ine sindingakhoze kunena.

46. Kodi inu mungalongosole Akorinto Woyamba 15:29?

310 Tandipezerani inu pamenepo, ngati inu mungathe, M'bale Neville, Akorinto Woyamba 15:29. Ife tipapeza apo.

311 Tsopano, ndipo mwina mawa ine ndikhoza kudzakupezerani inu apo kachiwiri. Monga . . . Zilembo zija, momwe izo zimalembedwera, "VICARIVS FILII DEI." Ngati inu mukukhumba izo, lolani kuti ine ndidziwe.

47. Kodi ulosi wa Ezekieli 38 ndi 39 udzakwaniritsidwa usanachitike Mkwatulo?

312 Ine ndikuganiza ayi. Ine ndikuganiza chinthu chotsatira chomwe ife tikuchiyembekezera ndi Mkwatulo wa Mpingo. Ndipo zikatero, "pamene Gogi ndi Magogi akubwera uko," ndi ankhondo achi Russia omwe akubweramo pa . . .

313 Taonani, Bambo Bohanon anali woyang'anira kuno wa Public Service Company, bambo wabwino kwambiri wa Chikhristu. Ndipo iye akuyankhula kwa ine tsiku lina, iye anati, "Billy, ine ndinayesera kuti ndiwerenge, ndipo ine ndinayesera kuti ndiwafunse abusa anga kuti alongosole Chivumbulutso." Anati, "Ife tinafika apo ndipo ife tinafika pozisokoneza Izo zonse." Anati, "Yohane ayenera kuti anadya—chinachake usiku umenewo ndipo anali ndi loto."

Ine ndinati, "Bambo Bohanon, manyazi pa inu." Ine ndinati . . .

Iye anati, "Chabwino, palibe mmodzi yemwe angazimvetse Izo."

314 Ine ndinati, "Osati munthu wachibadwa, koma Mzimu Woyera ukhoza kuziwulula Izo."

315 Iye anati, "Chabwino, tayang'anani apa, Billy." Iye anati, "Mkwatibwi anali ataima pa Phiri la Sinai. Ndipo apa panali madzi akulavulidwa kuchokera mkamwa mwa chinjoka, kuti chikapange nkhondo—nkhondo ndi Mkwatibwi. Ndipo Mkwatibwi anali Kumwamba pa nthawi yomweyo. Tazilingalira izo apo!"

316 Ine ndinati, "Bambo Bohanon, chinthu chokha chomwe inu muli nacho, inu muli ndi zinthu zitatu zosiyana mutazisakaniza, nkumazitcha izo 'Mkwatibwi.' Inu mukuwatcha *handiredi forte foro sauzande*, omwe anaima ndi Mwanawankhosa pa Phiri la Sinai, 'Mkwatibwi.' Iwo sanali. Inu mukuwatcha (iwo analavulitsa madzi kuchokera mkamwa mwake, kuti apange nkhondo ndi) *otsalira* a Mbewu ya mkazi, omwe sanali Mkwatibwi; awo anali omwe anatsalira. Mkwatibwi anali *Kumwamba*; handiredi ndi forte foro sauzande *uko*; ndi Mkhristu mwadzina akupita kudutsa mu kuzunzidwa kuno. Ndipo uko nkulondola."

317 Werengani, m'bale, tsopano ngati inu muli napo apo. [M'bale Neville akuwerenga Akorinto Woyamba 15:29—Mkonzi.]:

> *Nanga adzachita chiyani iwo omwe amabatizidwira wa akufa, ngati okufa sauka konse? nchifukwa chiyani ndiye iwo amabatizidwira chifukwa cha okufa?*

318 Tsopano, tsopano, abale, alipo amodzi—anthu amodzi omwe amakhulupirira izo, iwo amabatizidwira kwa okufa, ndiwo a Mormon. Ndipo ine ndakhala ndiri mu makachisi awo, nthawi zambiri, iwo ndi anthu abwino kwambiri. Ndipo inu

mukhoza kukhala a Mormon, tsopano. Ine sindiri kuyesera kuti ndivulaze kumverera kwanu. Koma, mzanga wokondedwa, inu simungakhoze kubatizidwira kwa abambo anu; ako ndi kachitidwe komwe iye ankayenera kukachita. "Komwe mtengo wapendekera, ndi komwe iwo umagwera."

Paulo, akuyankhula apa, anali kuyankhula za "okufa," Yesu Khristu, "ngati okufa sauka konse, nchifukwa chiyani inu mukumabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu ndiye ngati okufa samauka?" Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ndiye ndinu. . . Iye anati, "Tiyeni ife tizidya, tizimwa, ndi kukhala osangalala, pakuti mawa tifa, ngati okufa sauka konse." Koma iye akupitirira nalemekeza Mulungu chifukwa cha chiukitsiro cha okufa. Ndipo ife timabatizidwira kwa Yesu Khristu, mwa imfa Yake, kuikidwa, ndi chiukitsiro. Ndi chifukwa chake ife timabatizidwira kwa "okufa." Chabwino.

Ine ndikukhulupirira, tsopano, ili ndi limodzi lokha lowonjezera pambuyo pa ilo.

48. M'bale Bill, chonde tandiuzani ine momwe ndi—ndingalandirire ubatizo wa Mzimu Woyera. Iwo uli mwa pemphero, moyo wodzipereka, kuulandira Iwo monga ife timachitira machiritso? Ine ndikudziwa chomwe chiri kuti ukhale ndi chikhulupiriro cha machiritso pamene inu munandipempherera ine kuno. Kodi inu mumapemphera ndi kuika manja pa iwo, ofuna ubatizo wa Mzimu Woyera? Ine ndinabatizidwa mu dzina la "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." Chonde ndiuzeni ine ngati ine ndiyenera kuti ndibatizidwenso mu Dzina la Yesu, monga inu munayankhulira posachedwapa.

Tsopano, mzanga wokondedwa wa Chikhristu, ine sindiri kukuuzani inu zoti muchite. Ine ndikungoika Lemba apo. Ndipo inu mudziwa chimene, momwe Mzimu Woyera ungakhoze kubwera pakali pano pamene ife tikadayankhula. Mzimu Woyera ndi mphatso ya Mulungu. Mwaona? Iyo ndi mphatso ya Mulungu. Iyo ikhoza kubwera pamene ife tikadayankhula. Ndipo ine ndikukuuzani inu, pamene. . . Ngati anthu akanaphunzitsidwa moyenera, . . .

Ena a inu a nthawizakale kuno, ndiroleni ine ndikufunseni inu chinachake, inu a nthawi-zakalenu omwe mwakhala muli mu kachisiyu. Zipenyani pamene ine ndikuwabatiza anthu. Ndipo inu atumiki muchitenge ichi ngati chitsanzo. Ine ndinkawaphunzitsa anthu awo mpaka iwo ankatsuka moyo wawo iwo asanakalowe mmadzi amenewo, ndipo ine ndinali nawo iwo akukhulupirira kuti Mulungu anali wokakamizika kuti asunge lonjezo Lake; mwamsanga pamene iwo ankabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, Mzimu Woyera unali apo pomwe kuti awulandire iwo. Ndipo pamene iwo

ankatuluka kuchokera mmadzi, iwo ankaulandira Mzimu Woyera. Uko nkulondola. Ngati inu basi . . .

319 Azibusa, ziziphunzitsani nkhosa zanu, zizitengerani izo mu Baibulo umu. [M'bale Branham akusasa Baibulo lake—Mkonzi.] Chokani ku bukhu lakale la mpingo wina ilo, ndi kufika kuno mu Baibulo ili kumene Mulungu amaphunzitsa, ndipo inu simumakhala nawo mavuto amenewo.

320 Inde, kusanjika kwa manja ndi momwe ife tingalandirire Mzimu Woyera, ndi munthu wina wodzozedwa akusanjikapo manja.

49. M'bale **Bill, izo ziri . . . Kodi ziri kunja kwa dongosolo kuti wina adzuke ndi kupereka mauthenga mu malirime pamene mlaliki akupereka . . . pa Mawu?** Munthu uyu ali ndi mafunso atatu apa.

49b. Ndipo limodzi lina ndiro**: Ndiponso, kodi ziri kunja kwa dongosolo kuti uchite monga chomwecho pamene kuitanira paguwa kukupangidwa?**

50. Lachitatu, lina lachitatu: **Ndiponso, kodi ziri kunja kwa . . . Kodi ziri kunja kwa dongosolo kuti winawake aimirire mu mpingo ndi kumutsutsa mlaliki chifukwa cha chinachake chomwe iye wanena kapena kuchichita ulaliki ukuchitika, ndipo iye ali kuseri kwa desiki lopatulikalo? Zinthu zonse izi zachitidwapo pa kachisiyu nthawi zingapo.**

321 Tsopano, ndiroleni ine ndifike kwa awa mofulumira ndithu tsopano, izi ndi za kwa mpingowu tsopano. Ine . . . Tsopano, kwa inu alendo mu zipata zathu, ine ndiyenera kuti ndiwupatse mpingowu kukwapula kwapang'ono tsopano, chotero inu—inu mungokhala ngati mwaima pambali kwa miniti, mwaona, ngati inu mungathe.

322 Mvetserani, ana anga! Mphatso zimenezo ndi zodabwitsa. Palibe yemwe amadziwa momwe ine ndimakuyamikirirani inu, ndipo ine ndimakukondani inu ndi chikondi chaumulungu. Koma mphatso zimenezo zikhoza kukhala zokupwetekani inu ngati inu simungazigwiritse ntchito izo mu malo oyenera.

323 Tayang'anani pa anthu lero, anthu abwino uko kuminda, akupempherera odwala ndi kumalipiritsa ndalama pa izo. Uko nkulakwitsa. Ngati munthu ali ndi chikhulupiriro cha machiritso ndi kupempherera odwala, iye ayenera kuti akhale njonda yokwanira kuti azipempherera anthu popanda ndalama. Thokozani Mulungu! M'bale, ine ndikufuna kunena izo, osati kwa inemwini, koma kwa ulemerero wa Mulungu, palibe nthawi imodzi yomwe ine ndinayamba ndatengapo ndalama kuchokera kwa anthu, kapena chirichonse monga choncho; ndipo ndakanapo, kwenikweni, millioni, madola faifi handiredi sauzande, mu chopereka chimodzi. Ndipo inu mukudziwa izo; zinali komwe kuno, mu pepala. Mukuona? Uko nkulondola. Si

za . . . Pamene inu muchita izo, inu mudzataya chikhulupiriro chanu uko ndi Mulungu.

324 Tsopano anthu inu omwe mumayankhula ndi malirime ndipo muli nazo mphatso za malirime, Mulungu akudalitseni inu. Inu mukusoweka mu kachisi uyu. Ine ndikukufunani inu muno. Koma, tsopano, a—chinthuchi chikhale mu dongosolo, musati muzichita konse izo pamene mlaliki akulalikira. Ngati inu mutero, inu mwachoka mu dongosolo. Mukuona? Inu simuyenera kuti muzichita izo. Pakuti Baibulo linati, "Mzimu wa mneneri umamumvera mneneri." Ndipo pamene munthu akulalikira, iye ali ndi malowo, iye ali ndi omumvetsera, Mzimu Woyera uyankhula kupyolera mwa iye. Pamene iye watsiriza, ndiye ndi nthawi ya uthenga, inu mukuona. Chotero musati muzichoka mu dongosolo; ngati inu mutero, ndiye inu mumasokoneza ndipo inu—inu mumawukwiyitsa Mzimu Woyera uli ndi uthenga womwe ukuperekedwa.

325 Kuno si kale litali, ine ndinali mu msonkhano cha kuno kwinakwake mu Washington, zikwi zambiri za anthu anali ali pamenepo. Ndipo manenjala wanga, yemwe ali wolongosola Baibulo kwenikweni, iye anali ataima apo akuyankhula za machiritso Auzimu, atadzozedwa, Mzimu Woyera unali ukuyankhula. Dona anauka apo ndipo anayamba kuyankhula ndi malirime, ndipo iye anayembekezera mphindi yokha, ndiye iye anayamba kupitiriza. Mzimu Woyera unayamba . . . kukwiyitsidwa, inu mumakhoza kuwuona iwo pakati pa anthu. Iye anayamba kuyankhula kachiwiri, ndipo iye ankaimirira. Iye anati, "Mlongo, khala pansi, mu Dzina la Ambuye." Anati, "Iwe uli kunja kwa dongosolo." Ndipo atumiki anamutengera iye pena nakamudziwitsa iye.

326 Tsopano, chomwe izo ziri, mphatso izo ziripo mu dziko, izo ziri mu mpingo tsopano. Mphatso ziri mu mpingo, koma ana aang'ono osaukawo amazitenga mphatso zimenezo ndipo samakhala kuphunzitsidwa kuti azidziwa momwe angazilamulire izo. Ngati inu mungati muzizilamulira izo molakwitsa, inu mumachita kuwononga kochuluka kuposa momwe mukanachitira bwino. Mukuona?

327 Monga ngati bambo kupita kwina, kukapempherera wodwala ndipo winawake nkuchiritsidwa, nkuti, "Tsopano, inu mukuyenera kuti mundipatse ine madola chikwi pa izo." Tsopano, iye wachitano kuwononga kochuluka kuposa ubwino womwe anawuchita. Zikanakhala bwino ngati bamboyo akanapitirira ndi kumwalira mmalo mobweretsa chitonzo choterocho pa cholinga cha Khristu.

328 Tsopano, pamene inu . . . Pamene m'busa kapena mlaliki, kapena aliyense yemwe ali, akulalikira, gwirani bata lanu. Paulo anati tizichita izo, inu mukuona. Tsopano, ndiyeno iye anati, "Inu nonse mukhoza kuyankhula, mmodzi ndi mmodzi." Izo

nzoona mokwanira. Ndipo iye anati, "Ine ndikanakonda kuti inu nonse muziyankhula mmalirime. Izo nzabwino."

329 Koma inu simungakhoze kuyankhula mmalirime kupatula ngati inu muli nayo mphatso ya malirime. Ndipo palibe kukaika konse koma kuti pali mphatso zambiri za izo mu mpingo uno pano. Muli mphatso zambiri za izo mu mpingo wa Methodisti, muli mphatso zambiri mu mpingo wa Chibaptisti, ngati izo zikanati zizingolalikidwa kuti mphatsozo zizifika pogwira ntchito.

330 Motani? Ngati inu muika mbewu mu nthaka ndi kusazilimira izo, nchiani chomwe chimachitika kwa izo? Mwaona, izo zingakhale mu fumbi louma ilo, ndi kuvundamo; izo sizichitira ubwino uliwonse. Mphatso izi zakhala ziri mu mpingo nthawi yonseyi, koma tsopano pano madzi ayamba kugwa, mvula ya chipentekoste, kuti izithirire izo ndi kumabalapo zipatso. Tsopano, ziigwiritsani ntchito iyo mu malo oyenera.

331 Tsopano, ilo likuti, chabwino, ine ndikukhulupirira funso lotsatira linali apo, munthuyo anandifunsa, anati:

Pamene a . . . pamene iwo akupereka kuitanira paguwa?

332 Ayi, ine sindikanati ndiganize apo. Ngati inu mutazindikira, ndi kutenga Akorinto ndi kukaziwerenga izo, ena a inu pano, nga—ngati inu muli ndi mphatso ya kuyankhula mu malirime, ndiye inu penyani. Mu Baibulo, pamene iwo anali . . . utumiki utatha, mdalitso wa Mulungu unkatsikira pa osonkhana, ndiye iwo ankayamba kuyankhula, ndiye iwo ankayamba kumukuza Mulungu. Ndipo, nthawi iliyonse, pamakhala uthenga wolunjika kwa winawake. Osati . . . Inu muyenera kuti muzizipenya izo tsopano. Mukuona? Izo si basi chinachake chamwathupi. Iwo uzikhala uli uthenga wa kwa winawake, kuti winawake achite chinachake, kapena chinachake choti chiumangirize mpingo. Icho chizikhala chinachake choti chiziupatsa mpingo ulemerero.

333 Apo ndi pamene anthu Achipentekoste abweretsa chitonzo ku dzina lawo. Dzina lomwe *Pentekoste*, iwe ukhoza kulitchula ilo ndipo anthu amakhoza kungochokapo nkuti, "Zamkutu," chifukwa iwo awona zochuluka za zopitiriza; zomwe, anthu pokhala ali mwakuona mtima koma anali asanaphunzitsidwe.

334 Paulo anati, "Pamene ine ndidzabwera ku mpingo wa Chipentekoste uko," anati, "Ine ndidzawuika iwo mu dongosolo." Iwo ukuyenera kuti ukhale mu dongosolo, ndipo chirichonse chiyenera kuti chizichitidwa mwadongosolo, monga momwe Mzimu unalamulira. Kotero iye anati, "Tsopano, ngati ndibwera, ndipo inu nonse nkuyamba kuyankhula mu malirime; ndipo osaphunzira akabwera umo, iye ati, 'Chabwino, kodi nonsenu simunachite misala?'; nayenda kutulukamo."

335 Ndi basi zomwe mpingo wa Chipentekoste ukuchita. Iye anati, "Tsopano, mmalo mwake, ngati mmodzi wa inu anenera ndi kuulula zinsinsi za chinachake, (mmodzi wa inu akhale

mneneri, mwakuyankhula kwina)," iye anati, "ndiye kodi anthu sagwa pansi ndi kuti 'Mulungu ali ndi inu'?"

336 Chabwino, ine ndingakhoze bwanji kuikana mphatso ya kuyankhula mu malirime pamene ine ndiyenera kuti ndikane mphatso ya kulosera, ine ndiyenera kuzikana mphatso zina izi? Tsopano, mipingo yambiri, mipingo yaikulu, Nazareni, Pilgrim Holiness, ndi ina yotero, iwo amaganiza ngati munthu ayankhula mu malirime iye ndi mdierekezi. Ndiko kuchitira mwano Mzimu Woyera, komwe kulibe chikhululukiro. Ndi chomwe Ayuda anachita, anawaseka anthu okhala ndi Mzimu Woyera, ndipo anaweruzidwa nataika, chifukwa cha izo. Kulondola! Kodi Yesu sanati, "Ngati inu muyankhula mawu amodzi otsutsa Mzimu Woyera, izo sizidzakhululukidwa konse kwa inu mu dziko lino kapena dziko likudzalo"? Kotero khalani osamalira; ngati simukumvetsa, khalani phee.

337 Ndipo anthu inu omwe muli nawo Mzimu Woyera ndipo mwaitanidwira mu maudindo, aphunzitsi . . . Tsopano, kodi inu mungalingalire . . . pano ndipo ine nditaima pano kuyesera kuphunzitsa, ndipo apa nkumalumpha munthu, pambali pa ine, ndi kuyamba kuphunzitsa pa nthawi yomweyo, munthu wina nkuima apo akuimba nyimbo ya chisangalalo? Chabwino, ndi chisokonezeko bwanji!

338 Chabwino, umo ndi momwe ziriri ndi kuyankhula mu malirime. Muzizilola izo zizibwera mwadongosolo, monga momwe Mzimu ungamaziperekere izo, inu mukhoza kumayankhula ndi malirime.

339 Tsopano inu mukuti, "Chabwino, M'bale Branham, ine sindingachitire mwina izo."

340 O, inde, inu mukhoza! Paulo anati inu mukanakhoza. Iye anati, "Ngati pali mmodzi wa inu, pakati pa inu, yemwe amayankhula ndi malirime, ndipo apo nkukhala popanda wotanthauzira, alole iye kukhala bata." Ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe akufunira kuyankhula, akhale bata. Iyo ndi mphatso, m'bale. Ine—ine ndikupemphera, Mulungu andilole ine ndikhale ndi chitsitsimutso kuno masiku ena awa kotero ife tikhoza kudzalowa mu zinthu izo kwa inu, inu mukuona. Pomwe inu mungakhoze kuwona kuti ndi mphatso, ndipo mphatso imeneyo imafuna idzigwira ntchito nthawi zonse. Mukuona? Koma inu mukuyenera kumakhala ndi nzeru za Mzimu Woyera kuno kuti muzidziwa ndi pati ndi momwe mungamaigwiritsire ntchito mphatso imeneyo. Ndipo izo . . .

341 Inu mukuti, "Chabwino, ulemerero kwa Mulungu, Baibulo linati pamene Mzimu Woyera ubwera iwe siumasowa mphunzitsi aliyense. Iyeyo ndi mphunzitsi Iyeyekha." O, m'bale, inu mungakhoze bwanji kukhala aang'ono chotero powerenga Lemb- . . . Nchifukwa chiani Mzimu Woyera unaika aphunzitsi mu mpingo, ndiye?

342 Mukuti "Ine sindikusowa kukhala naye aliyense kuti azindiphunzitsa ine. Mzimu Woyera umandiphunzitsa ine." Iwo umatero, kupyolera mwa mphunzitsi. Iye anaika aphunzitsi mu mpingo.

343 Iye anati, "Kodi onsewo ndi aphunzitsi, kodi onsewo ndi atumwi, kodi zonsezo ndi mphatso zamachiritso?" Mzimu Woyera unaziyika zinthu izi mu mpingo, ndipo Iye amazigwiritsa ntchito izo zonse, ndipo iliyonse ya izo imagwira ntchito mwadongosolo.

344 Tsopano zangokhala ngati phazi langa; lina la iwo kuti, "Ine ndikupita mbali *iyi*," linalo nkuti, "Ine ndikubwerera mmbuyo njira *iyi*." Tsopano, kodi inuno muchita chiani? Dzanja nkuti, "Ine ndikuti ndikwere pamwamba apo," ndipo linalo likupita mozungulira kumbali iyi. Kodi thupilo likhala lowoneka motani? Mukuona?

345 Koma, tsopano, ngati lingaliro pano liti, "Phazi, sunthira mtsogolo, nonse inu. Dzanja, iwe upite limodzi nawo. Mutu, iwe ukhale molunjika. Mikono, inu muchite mofanana," chirichonse chikuyenda mwachiyanjano. Tsopano, pamene ine ndikafika apo, ine sindinagwiritse ntchito mikono yanga. Tsopano, phazi lachita ntchito yake, abusa atsiriza kulalikira; tsopano, mikono, inu chitanino ntchito yanu. Mwaona? Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

346 Chabwino, nanga bwanji ngati mikono ikanati izifikira monga *chonchi*, "O, kodi ziri pati izo? Ziri pati izo?" ndipotu mapazi akulalikira? Mwaona, inu simunafike apo panobe. Mwaona, khalani phee, nkono; ifika nthawi yoti inu mugwiritsidwe ntchito pakapita kanthawi; dikirani mpaka inu mukafike pamenepo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Imeneyo ndiyo mphatso, imeneyo ndiyo mphatso ya Mzimu ikugwira ntchito.

347 Ine ndimawakonda Ambuye. Sichoncho inu? Ameni. Mvetserani, ine ndikudziwa chinthu chimodzi chomwe ine ndingachinene cha inu, inu ndithudi muli ndi chipiriro; maminiti twente itadutsa teni. Tsopano, abwenzi, tayang'anani kuno monga chonchi tsopano. Ine. . . Uku ndi kudziwa kwanga kopambana. Ine ndimayenera kuti ndifulumire kudutsa mu mulu uwo monga choncho. Ngati ine. . . Ngati inu simugwirizana nazo izo, izo musalekane nane. Inu mukhale m'bale wanga, mwaona. Ine ndikukukondani inu, ndipo ine ndikungonena zinthu izi chifukwa zimenezo ziri mu mtima wanga. Izo ndi zomwe ine ndikuzikhulupirira, ndipo umo ndi momwe ine ndikuzifotokozera izo, ndipo umo ndi momwe ine ndikuzibweretsera izo, ndi kuchokera mu Baibulo.

348 Tsopano, ngati inu mukuti, "M'bale Branham, ine sindikukhulupirira basi izo mwanjira imeneyo." Izo zikhala ziri bwino mwangwiro, mwaona. Ife sitidzaganiza mosiyana

mulimonse, ife tizingopitirira patsogolo pomwe monga abale ndi abwenzi.

349 Ndi—ndipo ngati inu mukuti, "Chabwino, ine—ine ndikukhulupirira ngati ine ndiri wa mpingo wa Methodisti kapena mpingo wa Baptisti, ine ndidzapulumutsidwa mulimonsebe." Chabwino, m'bale, izo nzabwino mwangwiro. Ine ndikukutchanibe inu "m'bale wanga," chifukwa inu mukumukhulupirira Yesu Khristu. Mukuona? Ndiko kulondola. Kotero ife tikhala tiri abale ndi abwenzi chimodzimodzi basi.

350 Koma ine ndikungoyala kwa mpingo uwu, masiku ochepa awa pano, Chiphunzitso chomwe mpingo uno umaima nacho. Mukuona? Ndi chomwe mpingowu umaimira! Ndipo ngati pali dikoni pano yemwe samakhulupirira ubatizo wa mu Dzina la Yesu Khristu, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, kapena mphatso za Mzimu kukhala zikuwonetseredwa, dikoni ameneyo, pakali pano pamene ine ndiri chiimire, sakuyenera kukhala mu mpingowu mpaka iye atazikonza izo. Ndizo ndendende kulondola. Ndipo gulu loyang'anira liyenera kuti liziwone izo. Ndendende! Mpingo uno sumalamulidwa ndi madikoni; mpingo uno umalamulidwa ndi Baibulo ndi Mzimu Woyera, wokha. Inde, bwana. Tsopano, chotero zinthu zimenezo, ife tikukhulupirira ichi ndi Chiphunzitso cha mpingo uno.

351 Ife tiribe umembala uliwonse konse. Palibe aliyense ali membala pano, koma aliyense yemwe amabwera ndi membala, pakuti ife tikukhulupirira kuti ndife tonse mamembala a Thupi limodzi mwa ubatizo wa Mzimu Woyera.

352 Ndipo ife tikukukakamiza iwe, m'bale wanga wokondedwa wa Chikhristu kapena mlongo, kuti ubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu ndi kulandira Mzimu Woyera. Ngati iwe unalandira kale Mzimu Woyera, utabatizidwa kale mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera, Mulungu akudalitse iwe! Inu mukuti, "M'bale Branham, kodi ine ndichite chiani pa izo?" Funsolo linayankhidwa. Ine ndikhoza kungonena monga Paulo ananenera, inu muyenera kuti mubatizidwe mobwereza!

353 Tsopano, yang'anani kuno, Machitidwe. Tiyeni tiwerenge izi, Agalatia 1:9. Zilembeni izi, inu amene mukulemba izo. Paulo anati, munthu yemweyu amene ananena izi, iye anaphunzitsa zinthu izi. Inu mukukhulupirira izo tsopano? Ndi kulondola uko? Paulo anali atawauza iwo kuti anayenera kuti abatizidwenso kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo Paulo anati, "Ngati mngelo wochokera Kumwamba . . . " Agalatia 1:8, "Ngati mngelo wochokera Kumwamba akanati akuphunzitseni inu chinthu chirichonse pambali pa Ichi, musiyeni iye akhale kwa inu wotembereredwa." Ngati iye ali arkibishopu, ngati iye ali papa, ngati iye ali mtumiki, ngati iye ali mneneri, ngati iye ali m'busa, ngati iye ali mngelo wochokera Kumwamba, kapena aliyense yemwe angakhale ali, iye anati, "Ngati

iwo aphunzitsa china chirichonse pambali pa Ichi, msiyeni iye akhale kwa inu wotembereredwa!" Ndi kulondola uko? Ndipo iye anazibwereza izo kachiwiri, kuti, "Monga ine ndanenera, chomwecho ine ndikunenanso izo kachiwiri: Ngati iwo aziphunzitsa china chirichonse kupatula Ichi, msiyeni iye akhale wotembereredwa!" Nkulondola uko?

354 Kotero Ambuye akudalitseni inu. Ine ndaziwerenga izo kuchokera mu Mawu, ndipo inu mupange kusankha kwanu.

355 Tsopano ndi angati amaikonda nyimbo yabwino yachikale ija:

Chikhulupiriro changa chikuyang'ana kwa inu,
Inu Mwanawankhosa wa ku Gologota,
Mpulumutsi Waumulungu;
Tsopano ndimveni ine pamene ndikupemphera,
Ndichotsereni ine kulakwa kwanga konse,
Ndi kundirola ine kuchokera mu tsiku ili
Ndikhale Wanu kwathunthu!

356 Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake, inu mu mpingo uno. Ngati munthu woti adzafa akulalikira kwa anthu oti adzafa, pozindikira kuti uwu ukhoza kukhala uli ulaliki wotsiriza umene ine ndinayamba ndalalikirapo; ndipo ine ndayesa kulalikira ulaliki uliwonse umene ine ndatero, ngati kuti iwo unali wotsiriza wanga, ngati munthu woti adzafa kwa anthu oti adzafa. Tsopano ndikufunseni inu, abale anga, ndi mbadwa zimzanga za mmudzi uno ndi dzikoli, kodi inu mukumverera kwenikweni kuti mukusowa kuyenda kwapafupiko ndi Mulungu ikatha misokhano iyi? Mulungu akudalitseni inu! Ine monga . . . m'bale wanu, ndikulankhula kwa inu, pemphero langa lodzipereka liri, kwa inu, kuti inu mulandire kuyenda kwapafupiko uku ndi Mulungu.

357 Ndipo mulole, pa Tsiku Lachiweruzo, pamene mausiku awa omwe ine ndakhala ndikulalikira, padzakhale ngati—tepi yaikulu yojambulidwa ikuseweredwa pa Tsiku ilo, ndipo liwu langa lidzatuluka apo, ndipo ine ndidzayenera kudzaima apo ndi kudzapereka umboni, pakuti mawu anga mwina adzandidalitsa ine kapena kundiweruza ine pa Tsiku limenelo. Ndipo awo akhala ali mawu anga kwa zaka zina twente zosamvetsetseka, ndiri mnyamata wamng'ono wa pafupi usinkhu wa zaka twente, ndikulalikira Uthengawu, ndipo ine ndiri forte-faivi tsopano. Ndipo ine sindinawasinthe konse Iwo pang'ono, chifukwa ine sindingakhoze kuwasintha Iwo pamene Baibulo likadali mwanjira iyo.

358 Ine ndazizika Izo mwa mabishopu ndi china chirichonse, ndipo ine sindinayambe ndamuwona wina panobe yemwe angakhoze kuyankhula mosiyana ndi Izo, malingana ndi

Mawu. Iwo amati . . . Chabwino, tsopano, ine . . . Wansembe uyu, kuno masiku pang'ono apitawo, iye anati, "M'busa Branham, ife sitimatenga Baibulo; ndi mpingo, kwa ife." Kotero iwe sungakhoze kuyankhula kwa munthu ameneyo. Koma ngati mungazikhazikitse izo pa Baibulo, izo nzosiyana. Mukuona?

359 Ine ndikupemphera kuti Mulungu atero . . . Aliyense wa abwenzi anga Achikatolika muno, ndi aliyense wa abwenzi anga Achiprotestanti, ndi ngakhale . . . Iwo palibenso . . . Ngati wina . . . Ine—ine ndikungomukonda aliyense wa inu. Ndipo Mulungu akudziwa ngati izo ziri zoona kapena ayi. Zipenyani mu mzere wa pemphero, pamene wakhungu—wakhungu ndi wolumala, Iwo sumati, "Chikatolika."

360 Kuno pali bambo pomwe pano pa nsa- . . . pomwe pano, wa Chikatolika, akufa ndi khansara, atadyedwa yense; iye anabwera kunyumba yanga, ndipo Mzimu Woyera unabwera pa iye, unamuchiza iye ku khansara imeneyo. Iye sanamuuze iye konse ngati iye anali wa Chikatolika kapena ayi; ine sindinanene nkomwe mawu kwa iye. Iye anabwera kuno, anadzabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu ndipo analandira Mzimu Woyera. Apo pali bamboyo apo pomwe, wazamalonda mu Louisville. Eya. Mwaona?

361 Iwo sumafunsa ngati iwe uli wa Chikatolika kapena ayi. Izo ndi ngati mtima wako ukuchita njala yofuna Mulungu. "Odala ndi iwo amene amva njala ndi ludzu lofuna chilungamo, pakuti iwo adzakhutitsidwa." Ndi kulondola uko? Ameni. Ambuye akudalitseni inu.

362 Ndi angati amaidziwa nyimbo yabwino yachikale iyi, *Chodala Ndi Chimango Chomwe Chimatimanga?* Ndi anthu angati pano ali usinkhu woposa zaka forte, kwezani manja anu ndi ine, nkuti, "Ine ndikuikumbukira nyimbo yachikaleyo, kuyambira zaka forte, *Chodala Ndi Chimango Chomwe Chimatimanga*"?

Chodala ndi chimango chomwe chimamanga
Mitima yathu mu chikondi Chachikhristu;
Chiyanjano cha mitima ya apaubale
Chiri chonga chija chakumwamba.

363 Kodi inu simumazikonda nyimbo zachikale izo? Mvetserani, ine ndikufuna kuti ndinene izi, ngati ife tikanakhala nazo nyimbo zochuluka zachikale izo mmalo mwa kuchuluka kwambiri kwa izi zongopitiriza zomwe ife tiri nazo, ine ndikukhulupirira mpingo ukanakhala bwinoko. Ine ndimazikonda, nyimbo zabwino izo zachikale zomwe zinalembedwa ndi Mzimu Woyera.

364 A nthawi-yakale aja, ine ndinkakonda kukumbukira, bambo wachikulire wachikuda, ankakonda kukhala panja kuseri kwa nyumba, kumusi uko mu mapiri aku Kentucky. Pamene iye asungulumwa, iye ankakhoza kukhala pa chipika—chakale

chija ndipo iye ankakhoza kumamenya pa chipikacho. Ine ndikumukumbukira iye bwinobwino basi, anali ndi nkombero waung'ono wa tsitsi loyera kuzungulira mutu wake. Iye ankakhoza kumaimba nyimbo yachikale iyo, nyimbo yachikale:

Ine n'dzauka nkupita kwa Yesu,
Iye adzandikumbatira ine mmikono Mwake;
Mu mikono ya Mpulumutsi wanga wokondedwa,
O, kuli kululutira zikwi khumi.

365 Palibe kukometsera kochuluka kwa iyo. Ndi angati anayamba ayimvapo nyimbo yachikale iyo? Mai! Izo ndiye zabwino. Mvetserani.

54-0515 Mafunso ndi Mayankho
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org